Chitsutso

Jeffersonville, Indiana, USA
Julaye 7, 1963

1 Zikomo inu, M'bale Neville. Tiyeni titsale chiyimire mphindi chabe tsopano ku pemphero. Tiyeni tiweramitse mitu yathu. Kodi ziripo zopempha zoyankhulidwa zirizonse, ngati izo zingati zidziwike ndi dzanja lokwezedwa, kwa Mulungu yekha, kuti, "Ine... Sungani mu malingaliro mwanu tsopano chimene inu mukufuna kuti mumufunse Iye, ndipo mukhulupirire icho ndi mtima wanu wonse, pamene ine ndikupereka pemphero langa chifukwa cha

Inunso.

2 Atate akumwamba, ife tikuchiwerengera ichi mwayi wotero, kuti tabwera ku nyumba ya Ambuye, pa tsiku lolunda lino, ndi kudzapeza Kuwala kwa Mwana kwa Mulungu kukuwala, ndi kumva Mzimu Woyera ukuyimba kupyolera mwa anthu, ndi kuyankhula kupyolera mwa anthu, kuundana kwakung'ono kwa kuwala kwa dzuwa mkatimu. Ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha izi, kuwala kwa dzuwa Kwakumwamba pozungulira mitima yathu. Momwe ife tikukuthokozerani Inu chifukwa cha izo.

Tsopano anthu anu angokweza kumene manja awo mu kusonkhana uku, kuti iwo ali nazo zopempha, zomwe iwo akanakhumba kuti Inu mukanawayankha iwo mmawa uno. Ndipo ine ndikupemphera, Atate, kuti Inu mupereke chirichonse cha zopempha zawo. Ziripo zochuluka kwambiri, zomwe zawunjikidwa pa gome, ndi zopempha zochuluka kwambiri kulikonse, za anthu odwala, ovutika; kuitana kwa pa foni, mtunda wautali, pafupi makumi asanu pa tsiku. O Mulungu, kodi ife tichita chiyani? Ingotitsogolerani ife, Ambuye. Ife sitikudziwa njira iti yoti tipite kapena choti tichite, koma Inu mukhoza kulondolera zinthu izi, ndipo ife tikupemphera kuti Inu muzipereka izi kwa ife. Chifukwa, icho_icho ndi cholinga chathu, Ambuye, moyo umene ife tiri nawo pa dziko lapansi waperekedwa kwa ife ndi Inu, ndipo ife tikufuna kuti tiwugwiritse iwo ntchito pokulemekezani nawo Inu. Tsopano Inu mutilondolere ife mu zinthu zimenezo, Atate.

Tidalitseni ife lero pamene ife tasonkhana palimodzi kuti tadzamve Mawu a Ambuye, kuti tidzaimbe nyimbo, kuti tidzapereke pemphero. Imvani mapemphero athu. Sangalalani nafe mu nyimbo zathu, ndipo yankhulani kwa ife kupyolera mu Mawu, pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Ameni.Mukhoza kukhala pansi.

3 Ine sindikudziwa basi malo aliwonse amene ine ndikanati ndichitenge kukhala uli mwayi waukulu kuti ndiyimepo, kuposa momwe izo zikanakhalira kuti ndiyime mu_mu guwa, kuti ndinyeme Mkate wa Moyo kwa oyembekezera, anjala, anthu aludzu. Ndipo uwu ndi mwayi waukulu.

Poyamba, ine ndikanafuna kuti ndifunse ngati aliyense wa banja la a Wright ali pano, Hattie kapena Orville, kapena aliyense? Hattie. Kodi Orville ali ndi inu, Hattie? Chabwino, mufunseni iye ngati iye angati adzere cha kunyumba, mwamsanga, pa chimene ine ndinamuuza iye, inu mukudziwa. Adzaime cha kunyumba, ngati iye angathe. Ine ndinaiwala kuti ndichibweretse icho pobwera limodzi nane, mmawa uno, chinachake cha garu wawo wamng'ono yemwe iwo ali naye kumeneko. Kotero ine basi...Ngati inu muti, mudzangoyendetsa cha kunyumba komweko pamene inu muzichoka ukatha utumiki.

4 Ndipo tsopano, Edith, mchemwali wa Hattie, yemwe ife tikumudziwa ngati msungwana wamng'ono yemwe wakhala chilumalire chiyambireni iye ali khanda. Ndipo iye ali mkazi tsopano, ndipo iye ali mu maonekedwe oipa kwambiri. Tsopano ine, pafupi chaka chapitacho, ine ndinapita uko pamene iye anali ndi vuto lake loyamba, ndipo mwamsanga ine ndinapeza chomwe vuto lake linali, mwa thandizo ndi chisomo cha Mulungu. Tsopano, kwenikweni, lomwe liri vuto ndi mwanayo...

Iye akakhala, miyendo yake imagundana palimodzi, ndipo iye sangakhoze nkomwe kuisuntha iyo moitang'alitsa, ndi chifukwa cha kupsyinjika kowirikiza kulumikizana kwa misempha. Koma, chimene icho chiri, palibe chinthu cholakwika mwathupi ndi mwanayo, kunja kwa kukhulana kwa kupuwala ali mwana pamene iye anali pafupi usinkhu wa miyezi isanu ndi umodzi. Iye ankafuula ndi kulira moyo wake wonse, pafupifupi, mpaka ife tinamupempherera iye zaka zambiri zapitazo, ndipo iye wakhala wokondwa chiyambireni, mpaka pafupi chaka chapitacho.

5 Ndipo tsopano ndi kwenikweni kusintha kwa usinkhu. Mwakuyankhula kwina, kusintha kwa moyo wake, ndipo misempha yake ili mu chikhalidwe chomangika choterocho. Ndipo dona wamng'onoyo ali nacho mmalingaliro ake kuti iye akufa, iye sakhala moyo basi, basi kuchokera ku ora limodzi mpaka ku lina.

Ndipo inu mukudziwa. Ndipo akazi athanzi, amphamvu amakhala ndi nthawi yovuta, nthawizina amachita kubayidwa mankhwala owatonthoza, ndi kupita kosamalira openga, ndi kukalandira chithandizo chodzidzimutsa ndi chirichonse, pa nthawi imeneyo.

Munthu wokhalapo ali nako kusintha kuwiri kwa moyo.

Iwo amakhala nako kusintha kuchokera ku unyamata kupita uzibambo; kuchoka ku umai...kuchoka ku

usungwana kupita ku umai. Pafupi khumi ndi zisanu ndi chimodzi, zaka khumi ndi zisanu ndi ziwiri, iwo amakhala ngati gulu longowuluka ndi usiku. Ndipo ngati inu mutati mungopirira nawo iwo pa usinkhu umenewo. Ine ndiri naye mwana wamkazi ali mu usinkhu umenewo pakali pano, Rebekah. Muzimupempherera iye. Ndi Billy, O, aliyense wa ife, tadzera mu usinkhu wosokonezeka umenewo. Ndipo kotero ife timayenera kupirira nawo iwo, pozindikira kuti ndi china chake chimene iwo ayenera kudutsamo.

6 Ndipo tsopano, Edith, ndi kusintha basi kwa zaka zisanu ndi ziwiri. Zaka zisanu ndi ziwiri zirizonse, moyo wako umasintha. Kotero nthawi kasanu ndi kawiri kuchulukitsa kasanu ndi kawiri, inu mukuona, ndipo izo zimapangitsa izo ngati kuvuta, ndipo ndiko kusintha kwathunthu. Ndipo izo zimawavutitsa akazi. Amuna kawirikawiri amakhala ngati amakhala nako kutengeka kopusa pa nthawi imeneyo, ndipo nthawizina amawasiya akazi awo. Koma akazi amakhala opanda chonde pambuyo pa izo. Ndipo ife tonse timadutsa mu izo, ndipo ife tiyenera kumakumbukira kuti ndizo zinthu zomwe ife timayenera kupirirana wina ndi mzake, ndi kumvetsa zinthu zimenezo.

Ndipo Edith wamng'ono walowa mu chikhalidwe ichi, ndipo iye wataya kulemera kochuluka, ndipo iye akuwoneka moyipa. Ndipo ine ndikukuuzani inu, usiku wina, osati nonse a inu palimodzi, koma kaulendo kakang'ono kokha kupita kumeneko..Iwo akumakhala naye iye, usana ndi usiku. Ndipo kaulendo kakang'ono kupita kumeneko kuchokera ku kachisi kuno, makachisi anzathu kuno, ena a inu anthu pitani uko ndi kukawona banja la a Wright. Ine ndikutsimikiza iwo angayamikire izo. Kungopita uko, kukhala nawo iwo kanthawi pang'ono, ndi kukayankhula ndi iwo, kugwira nawo chanza, ndi zosaposa kucheza pang'ono kwa chibwanawe. Ife timaiwala zimenezo mophweka kwambiri, inu mukudziwa. Ndipo pamene izo zifika ku nyumba yathu yomwe, ndiye ife timayamikira izo. Ndipo ife tiyenera kumakumbukira, ena amayamikira izo, nawonso. Ndipo banja la a Wright, ine ndikutsimikiza, angayamikire izo. Ine_ine ndikudziwa inu mukanazichita izo ngati inu mukanadziwa kuti chikhalidwe ichi chinalipo. Koma inu simumadziwa izo, choncho ine ndinali kukuuzani inu mmawa uno, pa chifukwa ichi.

7 Pitani ndipo mukawachezere banja la a Wright, ndipo mukayese kumusangalatsa Edith. Tsopano, musati mukamuwuze iye kuti akuwoneka moyipa. Mukamuuze iye "akuwoneka bwino," iye "akhala bwino." Chimene, iye akhala bwino ngati titi tipitirize kugwirizitsa pa iye. Ndicho chifukwa chimene ife tiri pano. Iye ndi mlongo wathu, ndipo ife tiri pano kuti tigwiritsebe mu nthawi izi chifukwa cha mwana ameneyo. Basi monga momwe ine ndikufunira kuti wina agwirizitse chifukwa cha ine ndi kumapemphera pamene ine ndikudutsa mu mayesero anga, ndipo inu mumafuna wina pa anu.

Ndipo banja la a Wright lakhala liri limodzi la ziwalo zakale kwambiri amene amabwera ku kusonkhana kuno. Iwo, ine ndikulingalira, ndi M'bale Roy Slaughter ndi Mlongo Slaughter. Ine ndinawawona iwo mphindi zingapo zapitazo, ndinawagwedezera dzanja iwo pamene iwo anali kubwera muno. Ndinaganiza, inemwini, pamene ine ndimayendetsa pozungulira ngodya, "Ndi zaka zingati zimene ine ndamuwona M'bale ndi Mlongo Slaughter akutenga malo awo mu mpingo uno, kupyola mu zitunda-ndi- zidikha, ndipo akumkabe patsogolo?" Ndipo banja la a Wright, ndipo monga choncho, iwe umawayamikira anthu amenewo, inu mukuona. Ndipo tiyeni_tiyeni tizisonyeza kuyamikira kwathu kwa iwo.

8 Tsopano, lero, ine ndiri nawo Uthenga wautali. Iwo uli pa chitsutso.

Ndiyeno, usikuuno, ine ndamva kuti pali mgonero ndi kutsukana mapazi, zina zotero. Kotero abusa ayankhula, ndipo ife tikhala...ife tibwera kuno. Ndipo ngati inu muli apafupi, mubwere ndi kudzasangalala nawo_uthenga wochokera kwa m'busa, kuchokera kwa Ambuye, ndiyeno ndiponso kuchokera ku kutsukana mapazi ndi mgonero, usiku uno. Mukhala modzazana kwenikweni usikuuno, kotero ife tikhala okondwa kukhala nanu inu, ngati inu mulibe malo ena oti mupiteko.

Ndipo ife tikufuna kumuyamikira Don Ruddell, ndi m'bale wathu, ndi M'bale Jackson. Ndipo abale awa ndi abale athu, mipingo yapaulongo yomwe tayanjana. M'bale Jack Palmer ali panowa, yemwe amasunga gulu uko mu Georgia. Ndipo ife tikufuna kuwayamikira amuna awa ndi mtima wathu wonse. Chifukwa, nthawi zomwe ife timakhala ndi misonkhano, pamene ine ndibwera kuno, ndipo iwo amabwera kudzatichezera ife, ndipo ife tikuyamikira izo.

9 Ine ndikumuwona, mmawa uno, bwenzi langa labwino, Doctor Lee Vayle ndi akazi awo. Ine ndinamuzindikira Mlongo Vayle pamenepo, poyamba, ndipo ine ndimangoyang'ana pozungulira kuti ndiwone pamene M'bale Lee anali. Ndipo ine ndiri nako, kanenedwe ka Kummwela kachikale, "ngowe yotolera nayo," mwaona, paliponse ine ndikamupeza iye. Ine ndimamufunafuna iye tsiku lirilonse, pa msonkhano waukulu uja, kuti akhale ali uko kuti azindithandiza ine. Ndipo ine ndinati, "Chabwino, ngati Lee abwera, mumulole iye alalikire, ndipo ine ndidzangopanga pemphero la odwala." Ndipo ife tinamuyitana iye, ndi china chirichonse, ndipo sitinakhoze konse kumupeza iye. Kotero, ine ndiri nayo, ngowe yoti ndimutole nayo, pamene ine nditi ndiyankhule. Ndipo ife tiri oyamikira kukhala naye M'bale ndi Mlongo Vayle muno, mmawa uno.

Ndipo mwina mwake alipo ambiri owonjezerapo pano amene ife sitiri kuwamvetsa. Ine ndikumuwona mlongo pano, ine ndikukhulupirira, wochokera ku Chicago. Ine sindingakhoze...Ine ndikulidziwa gulu pano,

koma ine sindingakhoze basi kutchula maina awo ndendende. Kotero ife tikuwayamikira iwo kuchokera kulikonse, paliponse pamene inu muli.

10 Ine ndikuwona abale pano, anyamata awiri omwe ali oti adz adzozedwe (aang'ono mu utumiki, basibe) mmawa uno. Awiri, abale athu achikuda ochokera uko mu New York, angolandira kumene zikalata zawo kupyolera mu mpingo wa Philadelphian, ndipo apereka mpingo uno ngati ndi kumene iwo amachokerako. Ndipo ife tisanjika manja pa iwo, kuti Mulungu adalitse utumiki wawo mu New York. Ife tiri nayo mipingo iwiri kapena itatu kumeneko. Ine ndikukhulupirira M'bale Milano ali nalo limodzi la magulu aang'ono kumeneko, ndipo ife tikuwayamikira iwo. Ndipo pano pali awiri owonjozera akupita uko tsopano kuti akapange, kukhala nawo mautumiki kwa anthu kumeneko. Ndipo ife tikuyamikira zinthu izi.

Ambuye akudalitseni inu, kwambiri.

11 Ine ndikuyang'ana pozungulira ndi kuwona ena osiyana, ndipo iwe basi sungakhoze kutchula maina awo, koma ine ndikudziwa kuti Iye akumvetsa.

Tsopano, ine ndikukhulupirira, ngati mlongo wathu, walimba, kapena mmodzi wa iwo abwere kuno ndi kudzatiyimbira ife.

Pamene khala la Moto linamukhudza mneneri,

Kumupanga iye wangwiro monga wangwiro akanakhalira,

Ndipo pamene mawu a^liwu la Mulungu linati, “Ndani ati atipitire ife?”

Ndiye iye anayankha, “Ine ndiri pano, nditumeni ine.”

Pamene, ife tikuwadzoza atumiki awa pa kusanjika kwa manja. Tsopano, ife tikuzindikira kuti njira ya Mwamalemba ya kudzozera mtumiki ndi kusanjika kwa manja. Ine ndikuganiza ndi pamene abale athu a Mvula Yotsiriza, kapena anthu aku Battleford, ndi ena otero, anakhala osokonezeka; ndipo pamene iwo anawona uko, kusanjika kwa manja, nkuti azipatsana mphatso zauzimu. Tsopano, ife sitimakhulupirira kuti mphatso zimabwera pa kusanjika kwa manja. Ife timakhulupirira kuti...kusanjika kwa manja ndiko kuvomerezera kwa chimene ife tachiwona kale. Mwaona? Ndi “ameni.” Mwaona?

12 Tsopano, pamene iwo anasanjika manja pa Timoteo, ndi pa abale aja, iwo anali atazindikira mwa amuna amenewo kuti munali mphatso. Kumbukirani, “Kondoweza mphatso iyo imene inali mwa iwe, yochokera kwa agogo ako aakazi a Loisi.” Ndipo iwo anaiwona iyi mwa Timoteo, ndipo chotero akulu anasanjika manja pa iye ndi kumudzoza iye. Osati kuika manja pa munthu yemwe palibe chimene chinayamba chawonetseredwa, inu mukuona. Ndipo iwo amangopempha madalitso. Ndipo ife tonse tikukhulupirira izo. Kotero sitimapatsana mphatso zauzimu; ife timangowazindikira iwo, ndi kusanjika manja pa iwo, kuti tiwavomereze iwo, kuti ife tikukhulupirira kuti Mulungu wachita zinthu zoterozo kwa anthuwo.

Ine ndinazindikira, mmawa uno, kutali mmbuyo, M'bale McKinney wochokera^Ine ndikukhulupirira ndi Kinney kapena McKinney, mtumiki wa Chimethodisti wakhala kumbuyo uko, yemwe wangodzozedwa posachedwapa kuno, nayenso, ine ndikukhulupirira uko kunali kulondola, kuchokera pa nsanja; kuti akagwiritse iyo ku Ohio, limodzi ndi M'bale Dauch ndi Mlongo Dauch, ndi gulu lochokera uko ku Ohio. O, pamene ife tonse tisonkhana limodzi, malo aang'ono awa kubwera palimodzi, ndi zodabwitsa. Popanda chipembedzo; popanda zilumikizano za chirichonse, koma kwa Yesu Khristu yekha, ndizo zonse, mwaona, basi “titangokhala limodzi mu malo a Mmwamba mwamba.”

13 Chabwino, mlongo, ngati inu muti mutipatse ife...Tiyeni tingoimba imodzi iyi ndime imodzi ya iyo, “Pamene khala la Moto linamukhudza mneneri.” Tiyeni tiyimbe iyo limodzi tsopano.

Khala la Moto linamukhudza mneneri, Kumupanga kukhala wangwiro,

Liwu la Mulungu linati, “Atipitira ndani?” Ndiye anayankha, “Ndine, nditumeni.” Yankhulani, Ambuye, yankhulani, Ambuye,

Tsopano abale muzibwera kuno, ngati inu mungatero.

Yankhulani,ndifulumira kukuyankhani.

Lolani abale ena otumikira azibwera kuno, ngati angatero, omwe ati asanjike manja pa iwo. Othandizira apa kachisi pano, M'bale Ruddell, M'bale Lamb, ndi iwo.

...ine ndidzayankha, “Ambuye, nditumeni.” Ziichedwetsani iyo, chonde.

Ochuluka mtchimo ndi manyazi akufa; Imvani kulira kwachisoni ndi kowawa; Fulumira, m'bale, fulumira kukawapulumutsa; Yankha msanga, “Mbuye, ndiri pano.”

Yankhulani, Ambuye, yankhulani, Ambuye, Yankhulani, ndifulumira kukuyankhani; Yankhulani, Ambuye, yankhulani, Ambuye, Yankhulani, ndiyankha, "Ambuye, nditumeni."

Dzina lanu ndi ndani, m'bale?

"Orlando Hunt."

" M'bale Orlando Hunt, wochokera ku Mzinda wa New York. Ndi kulondola uko? M'bale

"Joseph Coleman."

" Joseph Coleman."

Tsopano ngati inu mutangotembenukira kwa omvetsera, abale anga.

14 M'bale Hunt ndi M'bale Coleman, kuyitana kwa Mulungu pa mitima yawo. Ndipo monga ife tangoimba nyimbo, "Alipo mamilioni tsopano ali mu tchimo ndi manyazi, akufa." Iwo amva kulira kwachisoni ndi kowawa kuja. Ndipo ife tikuwapempha iwo: fulumirani, abale, fulumirani abale kuti mukawaombole iwo! Mwaona, mwamsanga yankhani, "Ambuye, ine ndiri pano." Ndi momwe iwo akuyankhira, mmawa uno.

Ndipo monga ife, monga abale a mpingo uno, ndi gulu ili, tikuvomereza ichi, mwa kusanjika manja pa iwo ndi kuwapatsa iwo dzanja lamanja la chiyanjano, ngati kuti akhale mboni za Yesu Khristu, ndi kuthandizira kwathu pano, kuti ife tiziwaimira iwo kumbuyo pa chirichonse chimene chiri chaulemu ndi cholondola, mu Uthenga. Mapemphero athu adzakhala mosalekeza kwa amuna awa, kuti Mulungu adzawagwiritse iwo ntchito kuti amulemekeze Iye. Ndipo mulole mautumiki awo akhale olemera ndi aakulu mu New York. Mulole wawo_moyo wawo ukhale wodzaza ndi utumiki kwa Iye, kubweretsa mkati mitolo yofunika ku Ufumu. Mulole akhale miyoyo yaitali, yosangalala. Mulole Ambuye Mulungu awamangirire iwo ndi Kukhalapo Kwake kosatha, ndipo awapatse iwo thanzi ndi nyonga, ndi kuwasunga iwo mu utumiki Wake mpaka Yesu Khristu adzawaitanire iwo Kwawo Kwamuyaya mu mpumulo wa Kumwamba.

15 Lolani osonkhana awa tsopano, pamene ife tikuweramitsa mitu yathu, ndipo ife atumiki tikupita patsogolo kuti tisanjike manja athu pa iwo.

Atate athu Akumwamba, ife tikusanjika manja athu pa M'bale Hunt, mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu, monga chimene ife tachidziwa cha iye, Ambuye, chakhala chiri chilungamo. Ndipo ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha kuitanidwa uku mu moyo wake, wa utumiki. Ambuye, kayankhuleni kupyolera mwa m'bale uyu, azipindula miyoyo, kubweretsa chiombolo, Ambuye, kwa iwo amene ali mu ukapolo, zonse matenda ndi_ndi zamisala, ndi zamthupi ndi zauzimu. Ambuye, mupatseni iye utumiki weniweni, kuti iye akhoze, pa mapeto a ulendo wake, kuyang'ana mmbuyo umo podutsa mu njira yaitali imeneyo ndi kuwona kuti iye wakhala wokhoza, mwa chisomo cha Mulungu, kumugonjetsa mdani aliyense. Kupyolera mwa Yesu Khristu Ambuye wathu, ife tikupempha izi. Ameni.

16 Pa M'bale Coleman ife panonso tikusanjika manja athu, monga mboni, Ambuye, kuti tikuvomerezera kuitanidwa kwake, kuti ife, mpingo uno, gulu lino la anthu, tikumukhulupirira iye ngati wantchito wa Khristu. Ndipo ife tikupempha kuti Inu mumudalitse iye ndi kumupatsa iye utumiki wawukulu, wamphamvu, kuti iye azikapindulira miyoyo kwa Inu, Ambuye, ndi kumakaombola amumsinga, ndi kuswa mphamvu za Satana, pozungulira miyoyo ya anthu omwe iye akuyanjana nawo. Perekani kwa iye, Ambuye, moyo wochuluka zipatso, thanzi labwino ndi nyonga. Ndipo, iyenso, pamene iye adzafika ku mapeto a ulendo. Mulungu, perekani kuti iye adzakhoze kuyang'ana mmbuyo njira yaitali ndi kudzawona kumene, mwa chisomo cha Yesu Khristu, iye wakhala ali wokhoza kuswa zomangira zirizonse za mdani, mwa ulemu kwa Mulungu.

Atate Akumwamba, mulole amuna awa tsopano akakhale moyo chotero ndi kukagwira ntchito mu kukolola kwa Mulungu. Mulole madalitso Anu akhale pa iwo ndipo akhale nawo mpaka nthawi yomwe ife tonse titi tidzakomane pa mapazi a Mbuye wathu wamkulu. Mu Dzina la Yesu Khristu ife tikupempha izi. Ameni.

Mulungu akudalitseni inu, M'bale Hunt, akupatseni inu utumiki wochuluka zipatso. Mulungu akudalitseni inu, m'bale, ndipo akupatseni inu utumiki wochuluka zipatso, inunso, M'bale Coleman. Mulungu akudalitseni inu. Kachiwiri:

Khala la Moto linamukhudza mneneri, Kumupanga kukhala wangwiro,

Liwu la Mulungu linati, "Atipitira ndani?" Anayankha, "Ndiri pano, nditumeni."

O, yankhulani, wanga..(Mulole Iye ayankhule kwa mitima yochuluka yaing'ono.)..yankhulani, Ambuye, (Oitanidwa ndi Mulungu!)

...mwamsanga ndidzakuyankhani; Yankhulani, Ambuye, yankhulani, Ambuye, Yankhulani, ndiyankha, "Ambuye,

nditumeni."

17 Momwe ife tikumuthokozera Ambuye mmawa uno chifukwa cha ulemu waukulu uwu, kwa mpingo kuchitira umboni kutumiza kunja kwa atumiki mu munda mu tsiku lotsiriza lino. Chisomo cha Mulungu chipite ndi inu, abale anga! Ine ndikuyembekeza Iye akutumizani inu ku minda yakunja ndi kudutsa mdziko, mukulalikira chuma chosafufuzidwa ichi cha Yesu Khristu, kumene icho chiri chosoweka kwambiri. Losowa kwambiri, dziko liri lero.

Tsopano, zochuluka kwambiri za zinthu zabwino izi, ife tikungoyenera kuti titenge pang'ono pano ndi pang'ono apo, polinga kuti tizitengere izo zonse mu msonkhano mmawa uno. Tsopano lero ife tiri, ine ndikuyankhula pa phunziro limene ine nthawizina sindimakonda kufika pa nthawi zenizeni zopambana izi.

Tsopano, Lamlungu latha, ngati ena a inu simunali pano ndipo simunawumve Uthenga wa Eksodo Yachitatu; ndipo ngati inu mukanafuna matepi, ine ndikukhulupirira inu musangalala nayo imeneyo, Eksodo Yachitatu.

18 Kodi ife tiri ndi chiyani, mnyamata wodwala apa, kapena chinachake? O, mnyamata wamng'ono, wopuwala. Eya. Mulungu atamudalitsa iye. Ndi zimenezo. Chabwino. Basi pa mapeto a msonkhano, ife tikhala tikupempherera odwala, mulimonse, inu mukuona.

Ife tikukupemphani inu, mwinamwake ngati inu mungathe, kuti mupeze Uthenga, wa Eksodo Yachitatu, nthawi yachitatu yomwe Kuwala, Mngelo wa Ambuye yemwe wawaitanira anthu ku eksodo, wadzisonyeza Iyeyekha mowonekera pa dziko lapansi, mu eksodo. Mwaona? Ine ndikuganiza ndicho chowonekera kwenikweni, kwa ine: eksodo yachitatu!

Kodi inu mungasamale ngati ine nditavula chikhotho changa? Ndi motentha kwambiri mu kachisi mmawa uno, ndipo choziziritsa chokha chimene ife tiri nacho ndi pamene iwe ungadzikupize. Iwe uyenera kutulutsa mphamvu yako yomwe. Kotero ife tikukonza, tsiku lina, kudzaika chinthu choziziritsa muno, mwamsanga pamene ife titi tidzakhale titakonza zinthu.

19 Tsopano, ife tikhala woyamikira, ngati inu mukufuna kuti muumve Uthenga, Eksodo Yachitatu. Tsopano, ife takhala nako kutuluka kochuluka, koma ife ndithudi tikhoza kuika dzanja lathu pa malo, nthawi, a kutuluka kutatu kumene Mulungu, mu maonekedwe a Lawi la Moto, wabwera pansi kuti adzaitane ndi kuwalekanitsa anthu. Tsopano, ndiko kulekanitsa kwa anthu.

Ndipo ife tikupeza kuti, pamene Iye anaitana eksodo Yake yoyamba, Iye anapita patsogolo pa iwo mu Lawi la Moto, ndipo anawatsogolera iwo kupita^kuwatsogolera iwo kuti apite ku dziko kumene kenako Iye anawonekera patsogolo pa iwo, mu maonekedwe a Munthu wotchedwa Yesu Khristu. Iye anabwera kuchokera kwa Mulungu, ndipo anapita kwa Mulungu. Ndipo Iye anakanidwa. Ndipo Iye anabwera ndiye kuti adzaitane anthu kuchokera ku chikhalidwe chofunda chimene iwo anali atalowamo, chonga chimene iwo anali nacho uko mu Igupto, anali atapereka njira kwa tchimo ndi ku njira za Aigupto. Ndipo Mulungu anawaitana iwo atulukemo.

Ndipo tsopano ife tikupeza, nthawi yachiwiri, iwo anapereka njira pansi pa ukapolo kwa Ufumu wa Chiroma. Ndipo iwo anapita kumbali mu tizikhulupiriro ndipo anachoka ku kudzipereka kwenikweni kwa kupembedza, ndipo Mulungu kachiwiri anatumiza eksodo ina. Ndipo Iye anawonekera mu maonekedwe a Munthu yemwe ankatsogolera anthu.

20 Mu eksodo yoyamba, Iye anali Lawi la Moto. Ndiye, pamene Iye anadza pa dziko lapansi, mu dziko kumene Iye anawatsogolerako iwo. Ndi choyimira chokongola bwanji icho chiti chidzakhale mu Zakachikwi, kumene Iye akuwutsogolera Mpingo tsopano. "Ife tidzamuwona Iye monga Iye aliri, ndipo ife tidzakhala nalo thupi longa thupi Lake Lomwe laulemerero."

Ndipo lero, mwa Kuwala kwa Uthenga kunyezimira kuchokera ku Kuwala, Lawi la Moto mowoneka pakati pathu! Sayansi yakupenya Iko. Iko kuli mu magazini, ndi pa dziko lonse. Ndipo Iko, zonse mwasayansi ndi mwauzimu, kwazindikiridwa monga Lawi la Moto lomwelo, mwa zizindikiro zomwezo ndi zinthu zomwezo zomwe Iko kunkachita nthawizonse.

Ndipo tsopano mkati mwa masiku pamene pali zotentheka zochuluka ndi zinthu, komabe, Mulungu nthawizonse akudzizindikiritsa Iyeyekha. Tsopano ife tikupeza izi. Ndipo ndi chinthu chaulemerero bwanji icho chiri kuti udziwe izo, "Kachisi wa padziko uyu, tsiku lina," thupi lakale lofooka ili lomwe timadwaliramo ndi kusautsidwiramo, "tidzasinthidwa ndi kupangidwa monga thupi Lake Lomwe laulemerero; ndiye ife tidzamuwona Iye monga Iye aliri," ndi kudzakhala naye Iye mu Dziko lomwe ife tikupitako lero. O, ine^pafupifupi kutipanga ife kumverera ngati tiyime ndi kuimba Ine Ndikupita Ku Dziko Lolonjezedwa. Iwo mwinamwake adzakhala akuimba imeneyo pa utumiki wa ubatizo, mulimonse, chifukwa ndiyo nyimbo yathu ya ubatizo.

21 Tsopano kwa abale, konse kuno ndi mu dziko kumene matepi amapita, ndipo ndiko kuzungulira dziko lonse. Mauthenga awa sali kulondoleredwa kwa munthu wina payekha. Ndipo ife sitikanafuna kuti anthu

aziganiza kuti ife ndife monga kafuko kamtundu winawake, kapena gulu la otentheka omwe tadzisonkhanitsa tokha palimodzi, "kuti tidzilekanitse tokha, mowoneka ngati, osakhala nacho Chikhulupiriro," kapena kudzilekanitsa tokha motsutsa wina aliyense, kapena motsutsa Mulungu, kapena motsutsa Mpingo. Ndife ofuna Mpingo. Koma ife tikungoyesera kulozera, mwa Mzimu Woyera ndi thandizo Lake, chifukwa cha kusankhana uku kumene ife tiri nako lero. Ife, ife sitiri kukhulupirira mu izo. Ife tikukhulupirira kuti mipingo yonse iyenera kuti izisonkhana palimodzi, osati kusankhana; Amethodisti ku gulu lawo, ndi Abaptisti ku awo, ndi Aumodzi, ndi Autatu, ndi yomwe ife tiri nayo, onse ali opatukana. Ife timakhulupirira kuti iyo iyenera kukhala palimodzi, monga gulu limodzi lalikulu logwirizana la Thupi la Yesu Khristu, kuyembekezera Kudza kwaulemerero uko. Iwo asakhale ali opatukana, konse.

22 Ndipo chimene chimailekanitsa iyo, chikuyenera chikhale chifukwa chenicheni china chamaziko choti ife sitiri amodzi. Mu kuwerenga izi, ine ndinazindikira, mu kuwerenga izo, si mtundu wa khungu lathu; chifukwa, lachikasu, lakuda, labulauni, ndi loyera, onse amapatukira mu mabungwe osiyana. Si mtundu wa chakudya umene ife timadya; ife tonse timadya chakudya chofanana. Ife timavala mtundu womwewo wa zovala, ndi zina zotero. Koma ine ndikuwona pamene mwamaziko izo ziri, ndi munthu yemwe wachoka pa njira yopunthidwa ya kuphunzitsa kwa Uthenga, munthu aliyense. Ndipo pakuyenera kuti pakhale njira yina kuti motsimikizika isonyeze chimene chiri cholondola ndi cholakwika. Ndipo njira yokha yomwe iwe uti udzachitire izo, ndi osati kuika kutanthauzira kulikonse pa Mawu, kungowawerenga Iwo momwe Iwo aliri ndi kuwakhulupirira Iwo mwanjira imeneyo.

23 Munthu aliyense akaikapo kutanthauzira kwakekwake, izo zimapangitsa Iwo kunena chinachake chosiyana.

Kuchibweretsa icho kubwerera ku bungwe lapachiyambi la mpingo wa Katolika. Chimene, mpingo wa Katolika umakhulupirira kuti Mulungu ali mu mpingo Wake, "Ndipo Mawu alibe chochita ndi iwo; ndipo Mulungu ali mu mpingo Wake." Ndipo ife Achiprotestanti, monga ife tikupeza, ndi monga Chivumbulutso 17, kuti onse a iwo awunjikidwa palimodzi, ndi kuti mpingo wa Katolika unali "mayi" wa mabungwe onse. Ndipo ife tikuona kuti bungwe la Chiprotestanti, komabe mwakhungu, mwakhungu liri nacho chikhalidwe chomwecho cha mpingo wa Katolika. Baibulo limawutcha mpingo wa Katolika "hule," ndipo limautcha mpingo wa Chiprotestanti "timahule," limanena kuti hule anali "mayi wa timahule." Ndipo awo ndiwo anthu, ndiye mkazi wa mbiriyoyipa yemwe samakhala mowona ku malumbiriro ake achikwati. Ndipo ife tonse timadzitcha kuti ndife Mkwatibwi wa Khristu, ndipo komabe osawona chotero. Ndi chiyani chimene chikanapanga kusawonako? Pa kukhala mosiyana ndi_ khalidwe limene Mulungu waliyika kuti Mkwatibwi Wake azikhala nalo. Ndilo lingaliro langa langa, Baibulo, ndipo Ilo ndiro Mawu osalephera a Mulungu, ine ndikukhulupirira.

24 Ndipo, chotero, ife tikupeza kuti mpingo wa Chiprotestanti, polinga kuti ukhale nalo bungwe, umadzilekanitsa wokha ngakhale pochoka ku Malemba, kuti upange bungwe lake.

Atumiki, odzozedwa, amagwiritsa ku zinthu zomwe iwo, Tsopano, iwo amabwera kowerengera kwanga ndi mu zipinda, mwa mazana, ndi kudzandiuza ine, "M'bale Branham, inu mumapanga zitsutso zimenezo kwa anthu. Palibe yemwe ati aime motsutsa Izo. Iwo amadziwa kuti icho ndi Choonadi."

Bwanji, ine ndimati, "Nanga, bwanji inu simukuzichita izo?"

"Chabwino, inu mukuona, ngati ine nditati nditero, ine ndidzakhala ndikupempha mkate wanga. Osati munthu wina ine ndiri ndi utumiki. Ine ndiyenera kufika kwa Ambuye, ndipo ine ndiyenera kufika kwa anthu. Ndipo ine ndidzakhala wopanda wondiyimira kumbuyo."

Kodi inu mukuzindikira kuti Khristu ali wotiyimira wathu yekha! Baibulo liri chotiyimira chathu. Mwaona? Koma, izo, onani, ndiye izo zikuponyera_mpingo wa Chiprotestanti ndendende chinthu chomwecho chimene mpingo wa Katolika uli.

25 Mpingo wa Katolika sumasamala...Chabwino, ine sindikuti...Ine sindikupanga izo mwamwano chotero, ponena kuti iwo samasamala chimene Baibulo limanena. Iwo_iwo amalikhulupirira Baibulo, koma, onani, iwo ali...kulowezana kwa Utumwi ndi chimene mpingo wa Katolika wakhazikitsirapo. Ndiko kulowezana kwa mapapa, ndi kumamutcha Petro papa woyamba, ndi mpaka mmusi. Tsopano, iwo amazikhulupirira izo. Iwo amazikhulupirira zimenezo motsimikiza.

Ndipo Achiprotestanti, (onani) iwo akusonkhana limodzi ndi kukhala nalo bungwe ndendende basi monga iwo anachitira ku Nicaea, Roma, kumene iwo anachita bungwe mpingo wa Katolika ku Khonsolo ya Nicaea. Ndipo ife tikupeza kuti iwo onse ali ofanana. Iwo ali onse ofanana. Iwo akusiya Mawu a Mulungu, kuti apange bungwe. Mwaona? Ndiyeno pamene izo zifika ku Zoonadi zochuluka zazikulu zimene zimawoneka zachilendo lero, Izo ndi zakwina kwa iwo, chifukwa iwo angophunzitsidwa kokha mwa mwambo. Ife tiribe mwambo koma Baibulo. Ife tiribe kanthu koma Mawu Oyera a Mulungu, ndipo Apo mpamene ife taima.

26 Ndipo tsopano, lero, ine ndikufuna kuti ndiwerenge Lemba lina, miniti chabe, kuchokera mu Mawu

oyera, opatulika a Mulungu, opezeka mu Bukhu la Luka Woyera. Mutu wa 23 wa Luka Woyera, kuti tiyambirepo, tipeze...nsanja ya chimene ine ndikufuna kuti ndinene, lingaliro la maziko pa chinthu chimene ine ndikufuna kuti ndiyankhulepo. Ndipo inu mukutembenuzira tsopano ku Luka Woyera, mutu wa 23, ndipo ine ndikufuna kuti ndiwerenge ndime imodzi. Ndizo zonse zomwe ine ndikusowa kwa maziko awa mmawa uno, kuti ndiziyikepo izi. Tsopano ife tikuwerenga ya 20 mutu wa 23, ndime ya 33 ya mutu wa 23.

Ndipo pamene iwo...anafika ku malo, amene amatchedwa Gologota, kumeneko iwo anamupachika iye, ndi ochita zoipa, mmodzi ku dzanja lamanja, ndi winayo ku lamanzere.

Tsopano ine ndikufuna kuti nditenge mawu anai kuchokera pamenepo, kuchokera pa kuwerenga uko, kuti tiyike maziko pa chimene ine ndikufuna kuti ndinene, "kumeneko iwo anamupachika Iye," mawu anai. Ndipo tsopano phunziro langa likutchedwa^Ine_ine ndikubweretsa chitsutso kwa mipingo ya zipembedzo ya tsiku lino, ndiponso yambiri ya oyima paokha, chifukwa chomupachika Yesu Khrisu mwatsopano mu tsiku lino. Ndikuwatsutsa iwo.

Mmawa uno, iwo ukutchedwa: Chitsutso.

27 Ndipo ine ndikufuna kukhala ngati kuligwiritsa ilo ntchito mochuluka ngati kuti chinali chipinda cha bwalo la mulandu, pamene izo zinali...Ndipo pakutibe, guwa ndi mpingo ndilo bwalo la mulandu. Baibulo linati, "Ndiwo mpando wachiweruzo....kuti icho chiyenera kuyambira mu nyumba ya Ambuye." Ndipo izi ziri monga mpando wachifumu ndi nduna, ndi mboni, ndi ena otero.

Ndipo ine ndiri nawo, lero, ngati mboni yanga, ndiwo Mawu a Mulungu. Ndipo chitsutso changa chiri chotsutsa mipingo ya lero. Tsopano ine sindiri kumubweretsa wochimwa kuti alowe mu izi. Ine ndikungoyankhula izi kwa mpingo. Ndipo izo ziri zoti zikhale mu ma matepi tsopano, ndipo ine ndiyesa kuti ndidutsemo mofulumira momwe ine ndingathere.

Ine ndikuwutsutsa m'badwo uno chifukwa chomupachika kachiwiri Yesu Khristu.

28 Ndipo tsopano kuti ndichite ichi mu m'badwo uno umene ife tikukhalamo, ine pochita ichi, ine ndiyenera kusonyeza umboni. Ngati ine ndingati ndibweretse chitsutso, iwe uyenera kusonyeza umboni wa mulandu wakuphawo umene wachitidwa. Ine ndiyenera, kuti ndiwatsutse iwo, ine ndiyenera kuti ndibweretse umboni kuti nditsimikizire izo, kuti izo ziri, kuti zimene ine ndikunena zionekere pamaso pa Woweruza wamkulu. Chimene, ndipo ine ndikudzitenga ndekha ngati nduna ku...pa chitsutso ichi. Kuti, Mawu a Mulungu, pokhala mboni yanga, ine ndikuwutsutsa m'badwo uno chifukwa cha kupachika.

29 Ine ndiyenera kusonyeza, ndipo ndisonyeza, kuti mzimu womwewo uli pa anthu lero umene unabweretsa kupachikidwa koyamba, ndipo akuchita chinthu chomwecho. Ine ndiyenera kuchita izo, ngati icho chiti chikhale kupachika, kuti iwo amupachika. Ine ndiyenera kusonyeza kanthu kuti kachitidwe komweko mwa anthu lero kali kuchita chinthu chomwecho, mwauzimu, chimene iwo anachita mwathupi apo. Iwo anamupachika, mwathupi, Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu.

Ndipo tsopano, lero, mwa Mawu omwewo, ndi mwa Mzimu Woyera womwewo ndi Mawu omwewo, ine ndikukhumba kuti ndiyisonyeze mipingo apo pamene iyo ikuima, kuti iwo akuchita chinthu chomwecho lero, ndipo Baibulo linati iwo akanadzachita izo, ndipo kutsimikizira kuti ili ndi tsiku limene ife tiri kukhalamo.

Izo sizikanakhoza kukhala zikuchitidwa zaka zingapo zapitazo. Ine ndikuti, zaka makumi asanu zapitazo izo sizikanakhala zikuchitidwa, koma lero izi ziri mu nthawi yake. Ndipo izo sizikanakhala zikuchitidwa, mwinamwake, zaka khumi zapitazo, koma izo zikhoza kuchitidwa lero chifukwa nthawi yatha. Ife tiri pa nthawi yotsiriza. Ndipo ine ndikukhulupirira, monga wantchito Wake, kuti ife tiri basi pafupi kuti tiwoloke kuchokera mdziko lino, kupita ku Lina.

Chotero, nthawi ya kulapa, kwa fuko, iyo yapita. Ine ndikukhulupirira kuti fuko lino silingakhoze kulapa. Ine ndikukhulupirira kuti ilo lawoloka mzere wa pakati pa chifundo ndi chiweruzo. Ine ndikukhulupirira kuti ilo likuzandima mu muyezo.

30 "M'bale Branham, inu musanati muyambe mulandu wanuwo, kodi inu mutsimikizira chotani izo?" Izi zokha, kuti ife tiri olakwa ndi machimo omwewo amene Mulungu anawonongera nawo dziko, mu dziko la chigumula. Ndife olakwa ndi machimo omwewo amene Iye anawonongera dziko mu Sodomu ndi Gomora. Ndipo, tsopano, ndipo ife tiri nawo umboni wonse wofanana wauzimu uli pano patsogolo pathu, umboni wonse wofanana, wodziwika konsekonse mdziko, umene unabweretsa pansi zifundo za Mulungu pa mibadwo imeneyo. Kuti, iwonso, pokana, zinabweretsa chiweruzo. Kotero ngati m'badwo uno wakana chifundo chomwecho chimene chinakanidwa mu masiku amenewo, Mulungu angakhale wosalungama kuti awasiye iwo kuti adutse nazo opanda chiweruzo. Monga Jack Moore, mzanga wa ine, pena anati, "Ngati fuko lino lidutsa nazo opanda chilango chochokera kwa Mulungu, ndiye Mulungu adzakhala ali wokakamizidwa kuti azutse Sodomu ndi Gomora ndi kuwapepesa chifukwa chowawotcha iwo."

31 Tsopano, ife tikudziwa kuti mwauzimu iwo akuchita chinthu chomwecho lero, chifukwa iwo akuchita icho, nawonso, mwa cholinga chomwecho, ndipo mwa njira yomweyo imene iwo anachitira mu kupachikidwa kwa Ambuye, mwathupi. Iwo akuchita izo chifukwa cha nsanje, chifukwa cha khungu lauzimu. Kuti, iwo sakufuna kuti apenye. Iwo sangamvetsere kwa Izo. Yesu, mu ulendo Wake kuno pa dziko lapansi, Iye anati, "Yesaya anayankhula bwino za inu, 'Inu muli nawo maso ndipo simungakhoze kupenya, ndi makutu ndipo simungakhoze kumva.' "

Chifukwa chomwecho, chofanana. Cholinga chofanana ndi zifukwa zofanana, iwo akubweretsa kupachikidwa kwa Khristu mwatsopano, mochitanso, (monga ife titi tifike ku izo pakapita kanthawi), pa zifukwa zomwezo zimene iwo anachitira apo. Iwo sangakhoze kupeza kanthu kena kotsutsira Izo. Iwo sangayerekeze kuti ayesere kuzitsutsa Izo. Ndipo iwo amadziwa kuti umboni ulipo. Ndipo iwo amadziwa kuti Baibulo limanena chomwecho. Ndipo chinthu chokha chimene iwo angakhoze kuchita ndi kuchitira mwano Iwo. Ndizo ndendende. Kotero, ndipo zonse izi, zifukwa zofanana.

32 Ndipo tsopano, pa maziko awa, ine ndikuchita makani kwa m'badwo uno pa kumupachika Yesu Khristu; chifukwa chomupachika, ndi olakwa; ndi manja akuda, authakati, awumbombo, azazipembedzo ali nawo pa kumupachika Kalonga wa Moyo yemwe ankafuna kuti adzipereke Iyeyekha kwa anthu.

Inu mukuti, "Munthu yemweyo?"

"Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali Mulungu. Ndipo Mawu anapangidwa thupi, ndipo anadziwonetsera Iwowokha." Mawu anawonetseredwa mu thupi, ndipo iwo analiweluza thupi ndipo analiyika Ilo ku imfa, chifukwa Mawu anali atawonetseredwa. Ahebri 13:8, amati, "Yesu Khristu ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse." Ndi Mawu omwewo. Mwaona? Ndipo, mwa chifukwa chomwecho, iwo akuyesera kuti awapachike Mawu.

33 Tsopano, ku mutu wanga, kuti ndiswere mmbuyo pa phunziro limene ine ndikufuna kuti ndilitenge pamenepo, mawu anai. Tiyeni tifotokoze, "kumeneko." "Kumeneko," mzinda woyera kwambiri mu dziko, Yerusalemu. "Kumeneko," mzinda wachipembedzo kwambiri mu dziko. Kumeneko, "iwo," anthu achipembedzo kwambiri mu dziko, pa phwando la chipembedzo, phwando la Paskha. "Kumeneko," malo achipembedzo kwambiri, mzinda wachipembedzo kwambiri, bungwe lalikulukulu mwa mabungwe onse, mutu wa zinthu zonse, kumeneko, "iwo," anthu achipembedzo kwambiri pa dziko lonse, anali atasonkhana kuchokera konsekonse mu dziko. Iwo "anamupachika," imfa yochititsa manyazi kwambiri yomwe ikadakhalapo, kumupha, munthu akanakhoza kuphedwa nayo; wamaliseche, atamuvula zovala kuzichotsa pa Iye. "Iye ananyoza chitonzo." Mtanda uli nako kasanza katakulungidwa pa Iye; koma iwo anamuvula zovala Zake. Yochititsa manyazi kwambiri...

34 "Kumeneko," (mzinda wawukulukulu wachipembedzo,) "iwo," (anthu achipembedzo kwambiri,) "anamupachika," (imfa yamanyazi kwambiri,) "Iye," (Munthu wofunika kwambiri.)

Ngati izo siziri zokwanira kuti ziwutsutse m'badwo uno! "Kumeneko," bungwe lachipembedzo kwambiri, lalikulukulu kwa mipingo yonse itasonkhana palimodzi mu malo amodzi. "Iwo," anthu achipembedzo kwambiri a mitundu yonse, anthu amene ayenera kukhala ali omupembedza kumene a Mulungu. Iwo anasonkhana pa phwando lalikulukulu lopatulika limene iwo anali nalo, kuyeretsa kwa Paskha, pamene iwo anabweretsedwa kuchokera ku msinga kumka mu kumasuka. Ndipo "kumeneko" mu nthawi imeneyo, "iwo" pa nthawi imeneyo, anthu achipembedzo kwambiri, mu phwando lachipembedzo kwambiri, pa malo achipembedzo kwambiri, anabweretsa pa Kalonga wa Moyo chinthu chochititsa manyazi kwambiri chimene chikanakhoza kuchitidwa, kumuvula Mwamuna ndi kumupachika Iye pa mtengo. Chifukwa, "Wotembereredwa ali iye," litero lamulo limene iwo ankapembedza nalo, "wotembereredwa ali iye amene apachikidwa pa mtengo." "Ndipo Iye anapangidwa themberero chifukwa cha ife." Kumuvula zovala zake, kumumenya Iye, ndi kumutonza Iye, Mulungu yemwe wa Kumwamba; kutenga zovala Zake kuzichotsa pa Iye, ndi kumukhomera Iye pa mtanda. Iye! "Kumeneko iwo anamupachika Iye," pansi pa chilango chachikulu cha Chiroma.

35 Imfa yochititsa manyazi kwambiri lero siikanati ikhale kuwomberedwa. Imfa yochititsa manyazi kwambiri lero siikanati ikhale kuti ugundidwe ndi galimoto ndi kuphedwa, kumizidwa ndi madzi, kuwotchedwa ndi moto. Koma imfa yochititsa manyazi kwambiri lero ili chilango chachikulu chapoyera, kumene dziko lonse lingakuweruze iwe ndi kukutcha iwe wolakwa. Ndipo dziko lonse linaika manja awo pa Mwamuna uyu ndipo anamutcha Iye wolakwa, pamene Iye anali wosalakwa. Ndipo Iye anafa pansi pa adani, (osati abwenzi Ake, osati malamulo Ake), koma pansi pa kupachika kwa mdani. Kalonga wa Moyo, Munthu wofunika kwambiri yemwe anayamba wakhalapo, kapena ati adzakhalepo konse, Yesu Khristu. "Iye," Munthu wofunika kwambiri! Sungani zimenezo mmalingaliro tsopano pamene ife tikumanga nsanja imeneyo mozungulirapo lero.

36 Kodi inu mukanati mulingalire, pa malo monga Yerusalemu, kumene kwa zaka mazana makumi awiri ndi asanu, kapena zoposerapo, kuti anthu...kapena mazana a zaka. Ine ndikhoza kukhala nditatalikitsa pang'ono pa izo. Zikanakhoza kukhala ziri pafupi zaka mazana asanu ndi atatu kapena asanu ndi anai, kapena chinachake. Ine sindikudziwa kuti ndi motani, utali wake, kuyambira nthawi yomwe Solomoni

anamanga kachisi. Ine ndikulingalira, pafupi zaka mazana asanu ndi atatu, zinazake zonga izo. Ndipo iwo anali atayang'anira Mesiya yemwe anali kudza. Iwo anali atasonkhana kumeneko pa kupembedza kwa pa Paskha. Tangoganizani za izo tsopano! Likulu la Afarisi onse, Asaduki, ndi zimene inu muli nazo, mu kusonkhana kumodzi kwakukulu, kuti amupembedze Mulungu. Malo oyera kwambiri, Yerusalemu, kachisi wa Ambuye, ndipo anthu a Ambuye, anamutenga Ambuye Mwiniwake ndipo anamupachika Iye, ndi chilango chachikulu. Chinthu choterocho.

37 Tsopano mawu anai aja, iwo, "Kumeneko iwo anamupachika Iye." Tsopano, inu mukanali kusonyeza Baibulo, inu mukuona. Ndi mawu anai okha, koma Baibulo limachepetsa Zoonadi Zake. Tsopano, ine, ine ndiyenera kuti ndipite mozungulira, kuti ndifotokoze zimene ine ndikuziyankhula, koma Baibulo silisowa kuchita kufotokoza kanthu. Ilo basi liri lonse Choonadi, kotero Baibulo silisowa kuchita kufotokoza chirichonse. Ilo silimasowa kuchita kufotokoza izo, chifukwa Ilo liri lonse Choonadi.

Pano pali mawu anai a unyolo Wake wawukulu wa Choonadi. Ine ndiyesera kuti ndiwafotokoze iwo. Ndipo kuti ndiyesere kuwafokoza Iwo, momveka, zingapange nyumba yazowerenga. Palibe njira kwa ine yoti ndingafotokoze mawu anai amenewo. Koma tsopano tiyeni ife, mwa kuthandiza kwa Iye Yemwe anapangitsa Iwo kuti alembedwe, tiyesere kufotokoza mawu anai awa, kuti tibweretse izo mwa njira yotero kuti anthu akhoze kumazimvetsa izo.

Chimene ife tiri nacho patsogolo pathu tsopano, ife tiri nako kupachikidwa koyamba kutayikidwa patsogolo pathu; pa malo opatulika kwambiri, anthu achipembedzo kwambiri, imfa yochititsa manyazi kwambiri, kwa Munthu wofunika kwambiri. O, ndi zotsutsana chotero. Mai, o, mai, ndi chochititsa manyazi!

38 Tsopano tiyeni titenge, choyamba, mawu oyamba, "kumeneko." Tiyeni tikambe pa iwo maminiti pang'ono ife tisanati tibweretse chitsutso. Ife tiswera izi pansi ndi kukusonyezani inu chimene iwo anali akuchita, ndiye ife tipeza ngati chitsutso changa chiri cholondola kapena ayi. "Kumeneko," Yerusalemu, malo oyera kwambiri ophweka, chifukwa kachisi anali kumeneko; malo oyera kwambiri, chifukwa, iwo, kachisi, anali kumeneko. Ndipo Ayuda ochokera konsekonse mdziko anasonkhana ku malo amodzi awa, malo okomaniranapo a kupembedza. Kwambiri^malo aakulu kwambiri a kupembedza amene analipo, kunali ku Yerusalemu. Kachisi anali kumeneko. Ndizo, "Izo zinalembedwa, 'Anthu onse ayenera kuti azikapembedza ku Yerusalemu,' " chabwino, chifukwa ndicho chirikati cha kupembedza.

Ndipo lero inu mumawamva iwo... mmodzi wa iwo amafuna anene kuti iwo, "O, ife tabwera ku misonkhano yayikulu iyi," yomwe zipembedzo izi ili nayo iyo. Ndipo ife tiri nako kutsegulira kwa izo...ku Mzinda wa Vatikani, ndi kudzozedwa uku kwa mapapa, ndi zina zotero. Iwo, aliyense akuti, "Ife tonse tiyenera kuti tipite ku malo amsasa wa Amethodisti, kapena msonkhano wawukulu wa Bible Baptisti." Kapena, "Ife tonse tiyenera kupita ku Roma, ndi uko kumene chirikati chachikulu," iwo amakutcha, "kwa Chikhristu."

39 Mu nthawi ya nkhondo yotsiriza, pamene Roma anagwa, asirikari achi German awa Ambiri a inu anyamata mukudziwa za izi. Asirikali achi German aja anafika mpaka kukalowa mu Mzinda wa Vatikan uko, ndipo akuwombera pa Achimereka pamene iwo anali kupita patsogolo. M'bale Funk, ndi M'bale Roberson, ndi ambiri, ndi M'bale Beeler, ndi ambiri a abale aja omwe anali mu nkhondo ija, akudziwa. Ndipo inu mukudziwa chiyani? Ife tinapereka ulamuliro kuti iwo asati awombere pa mzinda umenewo. Achimerika, inu munaima pamenepo, ndipo inu munali chandamale kwa iwo. Koma ku Westminster Abbey mu England, inu mukhoza kuwombera pa iye chabwino; ndiko kumene Achiprotestanti anasonkhana. Kotero izo zinali zabwino kuti awombere pa iwo, koma osati kuti awombere pa Vatikan. Chifukwa, monga Purezidenti Roosevelt...ine ndinamvetsera zoyankhula zake pamene iye ankalengeza izo usiku umenewo, zotchedwa, Zoyankhula za Pambali pa moto. Iye anati, "Pamene Roma anagwa," iye anati, "manyazi oterowo, chifukwa Roma ndiwo mutu wa Chikhristu chonse." Kodi inu mukanalingalira wachiprotestanti kunena zimenezo?

40 Kotero chirikati chachikulu cha chipembedzo cha Chikhristu, chabwino, ife tikuti_tikuti tiziyike izo monga Yerusalemu, ngati inu mukufuna kutero. Ngati inu mukanafuna kuti muchite izo, tiyeni tiziyike izo ku Yerusalemu. Mutu wa yonse ina iyi, a Sanhedrin, ndi wa Afarisi, ndi wa Asaduki, onse a iwo ankapita ku Yerusalemu. Linali likulu lenileni.

Ndipo mu moyo wa bungwe, iwe uyenera kuvomereza kuti Mpingo wa Roma Katolika ndiwo manthu wa yonse imeneyo. Iye zedi ali. Ndipo iye anayamba kuchokera pa Pentekoste. Ndi kumene iwo anafika pamene iwo anachita bungwe. Tsopano ife, Achiprotestanti, tangokhala alongo pang'ono ochokera ku mpingo umenewo.

Ndipo tsopano tiyeni tinene kuti kukanakhala kuli kumeneko ku Vatikani, lero.

41 Kapena, kumeneko ku Yerusalemu, monga izo zinaliri mu tsiku limenelo, "Pamene anthu onse ankayenera kumabwera ku Yerusalemu kuti kudzapembedza." Nchifukwa chiyani iwo ankachita izo mu masiku a Yesu? Nchifukwa chiyani iwo ankati anthu onse ayenera kukapembedza ku Yerusalemu?

Chifukwa, alipo malo amodzi okha amene Mulungu ati adzayanjane naye munthu, pamenepo ndi pansi pa magazi a nsembe. Ndicho chifukwa iwo ankayenera kumabwera ku Yerusalemu. Mulungu sadzakomana naye konse munthu pena paliponse koma pansi pa Magazi. Pamene iwe uwagudulira Magazi pansi, ndiye malo ako okumaniranako ndi Mulungu achotsedwapo. Mulungu anapanga kusankha Kwake koyamba mmunda wa Edeni, kuti munthu akanamadzamupembedza kokha Iye pansi pa magazi okhetsedwa a nsembe. Ndipo ndiwo malo okha amene Mulungu ankakomana naye munthu apo, ndipo ndiwo malo okha omwe Mulungu anayamba wakumanapo naye munthu.

42 Ndipo ndiwo malo okha omwe Iye akukumana naye munthu lero, ndi pansi pa Magazi okhetsedwa a Nsembe. Mwaona?

Ine sindikusamala kaya ndinu wa Methodisti, Baptisti, Presbateria; ngati inu mungakhoze kuiwala zosiyana zanu, Roma Katolika, chirichonse chimene inu mungakhale muli, ndipo nkubwera pansi pa Magazi okhetsedwa, Mulungu adzakomana nafe tonse ife pamenepo. Ndi pamene ife tonse tingakhoze kukomana ndi kuyanjana pa malo ofanana. Koma, mwinamwake, Iye sadzakomana nawe basi chifukwa ndiwe wa Methodisti; Iye sadzakomana nawe basi chifukwa ndiwe wa Chipentekoste. Iye adzakomana ndi iwe pansi pa chikhalidwe chimodzi, ndicho, pansi pa Magazi okhetsedwa, pamene machimo ako okhala atavomerezedwa ndi kuchotsedwa mu Kukhalapo Kwake, ndiye, mwa Magazi. Ndipo Magazi nthawizonse ali pamaso pa Iye, ndipo chotero Iye angakhoze kukuwona iwe kupyolera mu Magazi okhetsedwa amenewo okha. Ndipo iwe umakhala woyera monga chisanu, mwaona, pamene iwe ulapa machimo ako. Mwina mwake, iwe suli pamenepo, iwe sungakhoze kuyanjana.

43 Ndicho chifukwa chimene inu simukuwona zinthu zikuchitika mu mipingo. Iwo amavomereza kuti iwo amawakhulupirira Magazi, koma iwo amakana dongosolo lomwe lofikira ku Magazi; Mawu. Mwaona? Pali njira imodzi yokha Mulungu ati adzalemekezere Mawu amenewo. Inu simudzawalemekeza konse Mawu amenewo, pobwera ndi kuti, "Ine ndine wa Chiroma Katolika. Ine ndikukakamiza ichi kuti chichitidwe." Inu simungakhoze kuchita izo. Methodisti, Baptisti, kapena Achipentekoste, inu simungakhoze kuchita izo. Njira yokha yomwe inu mungakhoze kuchitira izo ndi pansi pa zifundo za Mulungu, kupyolera mu chisomo Chake, ndi kubwera kupyolera mu Magazi okhetsedwa a Yesu Khristu, ndi kuti, "Ambuye, ine ndikutenga lonjezo." Mwaona? Ndiyeno ngati inu muli kwenikweni pansi pa Magazi amenewo, Mulungu ali wokakamizidwira ku Mawu amenewo. Koma, choyamba, inu muyenera kukhala pansi pa Magazi amenewo. Inu mukuchiona icho tsopano?

44 Palibe zodabwitsa kuti iwo sangakhoze kukhulupirira mu zozizwitsa. Palibe zodabwitsa inu simungakhoze kukhulupirira mu zauzimu. Palibe zodabwitsa kuti iwo amazitsutsa izo. Chifukwa chomwecho chimene iwo anazitsutsira izo kumbuyo uko, ndi chifukwa chomwecho chimene iwo akuzitsutsira izo lero. Iwo ali olakwa monga wolakwa angakhalire. Chifukwa, pansi pa Magazi okhetsedwa pokha... Ndipo iwo amene angayerekeze... m'bale wina wamng'ono yemwe angayerekeze, pansi pa kudzichepetsa, kuti amutenge Mulungu pa Mawu Ake, ndi kuyenda kumka uko ndi kukavomereza machimo ake, ndi kuiwala ziphunzitso zonse izi ndi zinthu, ndi kuima pamenepo pansi pa Magazi ndi kuwakhulupirira Iwo, ndiye iwo amafuna kumutcha iye "wotentheka." Iwo amafuna kumuyika pa malo monga ife tingati tinenere izo; (awo si mawu abwino oti nkuwagwiritsa ntchito pa guwa, koma ndi motero kuti inu mumvetse,) iye ndi "wosamvetseka." Pambuyo pa zonse, kodi ife tonse sindife osamvetseka? Mwaona, okhulupirira ndi osamvetseka kwa osakhulupirira, ndipo osakhulupirira ndi osamvetseka kwa okhulupirira, kotero ndani yemwe ali wosamvetseka? Mwaona? Mlimi ndi wosamvetseka kwa munthu wamalonda; munthu wamalonda ndi wosamvetseka kwa mlimi, mwaona, kotero ndi ndani iye, mulimonse?

Ine ndikukuuzani inu, chipulumutso ndi chochitika cha payekha munthu ndi Mulungu, okha, munthu mmodzi, "kufunafuna chipulumutso chatokha ndi mantha ndi kunjenjemera." Ndipo ine sindikudziwa maziko ena, monga mphunzitsi, mmawa uno, kapena monga mtumiki wochokera kwa Khristu, kuposa kuti ndiziyale izi pa Mawu. Ine sindingakhoze kuziyika izo pa china chirichonse.

45 Tsopano ife tikupeza apo, ndiye, kuti pansi pa magazi pokha, kuti Mulungu ankakomana naye wopembedza, kotero iwo ankakakomana ku Yerusalemu. Ndipo Khristu ali Mwanawankhosa woperekedwa ndi Mulungu wa Nsembe. Ndipo lero alipo malo amodzi okha amene Mulungu ati adzakomane naye munthu, ndipo ndiwo pansi pa Magazi a Yesu Khristu. Pena paliponse, ndi potsutsidwa; Mulungu sadzazimva konse izo. Inu mukhoza kuchita mtundu wonse wa kutengeka, ndi mtundu wonse wa zoikidwapo, ndi kunjenjemera, ndi kulumpha, ndi kukhala nawo magazi ndi moto ndi utsi, ndi china chirichonse; koma ponsepo ngati moyo umenewo suli kufanizana ndi Mawu, ndi Mulungu mwathunthu kuwutsimikizira moyo umenewo, ndiye apo palibe chifukwa chomayesera izo, chifukwa iwe uli kunja. Ndipo Mulungu sadzakomana nazo konse izo mpaka izo zitabwera pansi pa chisamaliro cha Magazi amenewo. Ndiko kulondola.

46 Kotero, inu mukuona, mu Lemba, ife tiri naye Yerusalemu, Mpingo uli naye; iye ali Kumwamba, Yerusalemu Wakumwamba, kumene Mulungu ali Mulungu. Ndipo, lero, izo siziri pansi pa kachikhulupiriro kena kapena chinachake, chimene ife timayesa kuchipanga icho kukhala Yerusalemu. Ife tikadakonda... Amethodisti, akanafuna kupanga likulu la Amethodisti ku Yerusalemu. Akatolika akanakonda kulipanga

Roma. Ndi malo osiyana kumene ife tiri nawo malikulu athu, ife tikanafuna kukupanga iko, Yerusalemu. Koma Baibulo likunena, kuti, "Yerusalemu wathu ali wochokera Kumwamba, yemwe ali mayi wa onse okhulupirira."

47 Tsopano, ndipo Khristu ndiye Mwanawankhosa woperekedwa ndi Mulungu. Zindikirani momwe izo zinali moyenera tsopano, kusonyeza kuti Yerusalemu uja anali kutha. Liti? Iye anali akuchita bwino mpaka ora limenelo. Magazi a mwanawankhosa anali abwino mpaka tsiku limenelo, koma tsopano pa kupachikidwa izo zikusintha. Kachitidwe kakale katha. Apo panali kena katsopano, ndipo Mwana wankhosa anali ali pa Nsembe. Mwanawankhosa, Mwana wankhosa wansembe, anali pa malowo. Iwo anali kumuweruza ndi kuchita chinthu chomwecho uko chimene iwo ankayenera kuti achichite. Ndiko kulondola.

Mulungu akhale akudalitsidwa, chifukwa chowona Kuwala kodabwitsa uku kwa Kumwamba mu tsiku lino lotsiriza! Chifukwa, mipingo ili kuchita chinthu chomwecho lero. Mpaka ora limene bungwe lachipembedzo latsutsidwa ndi kutsimikiziridwa kuti likuchita nsembe Mawu a Khristu, kuyambira pamenepo pakubwera Mawu, ndipo Mawu okha. Kuyambira, pa mwana wankhosa wakale wapaskha anathayo ndipo Khristu wakhala Mwana wankhosa wathu, pa tsiku la kupachikidwa. Ndipo tsiku limene chipembedzo chinawapachika Mawu a Mulungu ndipo linavomereza kachikhulupiriro mmalo mwa Mawu, ndilo tsiku limene Mawu anafika pa kugwira ntchito kwathunthu. Izo zachitika posachedwa pomwepa.

48 Zindikirani, chachiwiri. Choyamba, "kumeneko," Yerusalemu. Chachiwiri, "iwo," iwo. Ndani? Ayuda, opembedza. Taganizani za izo! Opembedza iwoweni anali kumupha Mmodzi yemweyo amene iwo ankadzinenera kuti amamupembedza. Kodi inu mukanakhoza kulingalira chinthu choterocho, monga anthu anzeru omwe anali ansembe, omwe anali ophunzitsidwa, omwe anali ndi digirii ya udokotala mpaka iwo... mwina mwake...Iwo, ankayenera kutuluka kuchokera ku m'badwo wina wake iwo asanati...kapena_ kapena mbumba, asanati iwo akhale wansembe konse. Iwo ankayenera kuti akhale Alevi. Makolo awo anali ansembe. Agogo awo aamuna anali ansembe. Agogo-agogo-agogo-agogo- agogo-agogo awo aamuna anali ansembe. Ndipo iwo ankayenera kumakhala moyo woyeretsedwa chotero, mpaka, dontho limodzi mowatsutsa iwo, iwo akanakhoza kugendedwa. Panalibe chifundo chimene chinkaperekedwa. Woyera? Ndithudi, koma chiyero chodzipangira-okha. Iwo ankayenera kumachita monga choncho, kuti asonyeze nkhope zawo kwa mpingo wawo. "Mkati mwa iwo," Yesu anati, "ndinu odzaza ndi mafupa a anthu akufa."

Momwe ine ndingakhoze kubweretsa chitsutso apo pomwe! Ndipo munthu yemwe akudziwa kuti Icho ndi Choonadi, Mawu awa kuti ali Choonadi, ndipo kumalekerera pa Iwo, kungoti asonyeze nkhope pamaso pa bungwe linalake, u-nhu, ine ndiri nawo ufulu woti ndiwatsutse iwo, kumene, pa Mawu a Mulungu.

49 Zindikirani, "iwo," opembedza, amuna amene anali atayang'anira lonjezo, amuna amene anali ataliyang'anira ilo, kupyola mu zaka ndi mibadwo, ndipo alibe chinthu choti nkuchita koma mu seminare imeneyo mowirikiza. Koma iwo anali atawagawaniza Mawu malingana ndi kuphunzitsa kwa seminare, ndipo iwo anali ataphonya Choonadi chomwe cha Iwo. "Iwo," ansembe, utumiki wa tsiku limenelo! "Kumeneko," ku likulu lawo, "iwo," utumiki wa tsiku limenelo, unali kumupha Mulungu yemwe, Mwanawankhosa yemwe. Mmodzi yemweyo amene iwo amadzinenera kuti anali kumupembedza, iwo anali kupha.

Ndipo, lero, ine ndikutsutsa gulu ili la atumiki odzozedwa; mu tizikhulupiriro tawo ndi zipembedzo, iwo akumupachika, kwa anthu, Mulungu yemweyo amene iwo akudzinenera kuti iwo amamukonda ndi kumutumikira. Ine ndikuwatsutsa atumiki awa, mu Dzina la Ambuye Yesu, pa kachiphunzitso kawo, kamene amati nako kuti "masiku a zozizwitsa anapita," ndikuti "ubatizo wa madzi mu Dzina la Yesu Khristu suli wokwanira ndipo si wolondola." Pa Mawu aliwonse awa, omwe iwo alowezeramo tizikhulupiriro, ine ndikuwatsutsa iwo, ngati olakwa, ndipo Magazi a Yesu Khristu ali mmanja mwawo, chifukwa chomupachika katsopano Ambuye Yesu, nthawi yachiwiri. Iwo ali kumupachika Khristu, ku gulu, kutenga kuchokera kwa iwo chinthu chimene iwo akuyenera kuti azichipereka kwa iwo. Ndipo iwo akulowezetsamo chinthu chinachake mu malo Ake; kachikhulupiriro ka mpingo, kuti atchuke.

50 Kumeneko iwo, "iwo," amodzi amene amayenera kuti azidziwa bwinoko. Ngati aliyense akanati azidziwa bwinoko, akanakhala ali atumiki amenewo. Ngati aliyense akanati azidziwa bwinoko, akanakhala ali azibusa a tsiku lino. Ngati aliyense akanayenera kudziwa, mabishopu, ndi maarchbishopu, ndi atumiki, ndi madokotala azauzimu, amayenera kumadziwa mosiyana. Koma bwanji iwo sakutero? Ha! Ndi zosagwirizana bwanji! Nchiyani chimene tiri nacho patsogolo pathu pano koma_zosagwirizana! Iwo amadzinenera kuti iwo amapembedza Mulungu, ndipo iwo akumupha Kalonga wa Moyo.

Iwo... "kumeneko iwo anamupachika Iye," ndipo kuno iwo kachiwiri akuchita chinthu chofanana, pakuti Iye ali Mawu. Ndicho chimene Iye ali, chinyezimiro chokha cha Mawu. Ndipo ndicho chimene Iye ali lero, chinyezimiro cha Mawu, kuyesera kuti amupeze munthu wina woti Iye mwini adzinyezimiritse kupyoleramo.

51 Ndipo anthu awa amawasunga osonkhana kutali ndi Mulungu. Ndipo ngati pali chiri chonse chikuchitika, ndipo icho chikayankhulidwa mwa osonkhana, iwo amachinyoza icho kuchokera pa nsanja,

kuchokera pa guwa, ndi kumati, "Ndi kutentheka. Khalani kutali ndi izo!" Mu kuchita izo, iwo akumupachika Yesu Khristu mu 1963, ndipo ali olakwa basi monga anthu aja pa tsiku lijalo. Ndilo neno lowopsya, koma ndi choonadi.

Ndicho ndendende chimene iwo akuchita lero. Ndipo pa malo awa, pa malo a kumupachika Khristu, pa malo a kuwatenga Mawu ndi kuwatengera Iwo kutali ndi anthu; chiri ndendende chimene iwo anali kuchichita kumeneko. Mawu omwe amene Mulungu anali kuwanyezimiritsa kupyolera mwa Mwana Wake Yemwe, kuti atsimikizire kuti Iwo anali, ndipo Mmodzi yemwe iwo ankadzinenera kuti iwo ankamukonda, Yehova yemwe anali atadziwonetsera Iyemwini mwa Malemba, anachita ndendende chimene Iye anati Iye akanati adzachite, ndendende chimene Mulungu anati Iye akanati adzachite, ndipo ananyezimiritsa Izo pamaso pa iwo. Chifukwa cha chikondi cha magulu awo a mpingo, ndi zinthu monga choncho, iwo anamuweruza Kalonga wa Moyo.

52 Ndipo ine ndikuliweruza gulu lomwelo lero, ndipo ine ndikuwatsutsa iwo, ngati olakwa pamaso pa Mulungu, mwa Mawu a Mulungu, kuti iwo akuchita chinthu chomwecho. M'badwo uno watsutsidwa.

Kumbukirani Ahebri 13:8, "Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwa nthawizonse."

Kodi iwo anamutsutsa chotani Iye? Chifukwa kuti tizikhulupiriro tawo sitikanamulandira Iye, ndipo pansi mu mtima mwawo iwo ankadziwa mosiyana. Kodi Nikodimo, mu mutu wa 3 wa Yohane Woyera, sanafotokoze bwinobwino izo? "Mphunzitsi, ife, Afarisi," alaliki, aphunzitsi, "ife tikudziwa Ndinu mphunzitsi wotumizidwa kuchokera kwa Mulungu, pakuti palibe munthu akanakhoza kumachita zinthu zimene Inu mukuchita kupatula ngati Mulungu akanakhala ndi iye." Mwaona? Iwo mwapagulu anachitira umboni izo mwa mmodzi wa amuna awo otchuka, ndipo chifukwa cha tizikhulupiriro tawo, iwo anamupachika Khristu. Ndipo lero palibe mwerengi yemwe sangakhoze kuwerenga Machitidwe 2:38 mofanana monga ine ndingakhoze kuwawerenga Iwo, ndi ena onse a Iwo, mofanana basi monga ine ndingakhoze kuwawerenga Iwo. Koma chifukwa cha tizikhulupiriro tawo, ndi chifukwa cha matikiti achipembedzo chawo omwe iwo ali nawo mu thumba mwawo, zilemba za chirombo zomwe iwo akunyamula konsekonse ngati makadi achiyanjano; ndi, potenga zinthu zimenezo, iwo akudzipachikira kwa iwoeni Yesu Khristu katsopano, ndipo akumupachika Iye pamaso pa gulu, ndi kuchitira mwano Mulungu yemwe amene analonjeza kuti adzachita Ichi, kubweretsa tsoka pa mtunduwo.

53 Tsopano, kumeneko, "iwo," osati wochimwa. "Iwo," amenewo ndi, mpingo wa tsiku limenelo, iwo anapeza cholakwika ndi Munthu Yemwe anali Mawu. Ndi kulondola uko? Iwo anapeza cholakwika ndi Munthu Yemwe anali Mawu. Tsopano iwo akupeza cholakwika ndi Mawu akugwira ntchito kupyolera mwa munthu. Mwaona, iwo akungosemphanitsa izo. Amene, ali mwa munthu, Uwu, Mzimu Woyera ukugwira ntchito kupyoleramo, ndiko kutsimikizira kwa Mulungu. Kodi iwo ankadziwa chotani kuti Iye anali Khristu? Chifukwa ntchito Zake zinatsimikizira chimene Iye anali. Iye anati, "Ndani mmodzi wa inu angakhoze kunditsutsa Ine za tchimo? Ngati ine sindinachite ndendende basi chimene Lemba linati Ine ndikanati ndidzachite! Ndipo ndani^Wina andiuze Ine pamene Ine ndalephera penapake, ngati Ine sindinasonyeze chizindikiro chirichonse kuti Ine ndine Mesiya, kuti Ndine Mmodzi yemwe amene inu munalonjezedwa."

Akuti, iwo anati, "Chabwino, ife tiri naye Mose. Ife timamukhulupirira Mose."

Anati, "Ngati inu mukanati muzimukhulupirira Mose, inu mukanandikhulupirira Ine. Ngati inu...Mose anawona tsiku Langa ndipo anakhumba kuti adzakhale mu tsiku lino. Mose analiwona liri kutali komwe, ndi aneneri. Ndipo pano inu muli, mukukhala pafupi kumene ndi Iwo, ndipo mukumanyoza." Anati, "Inu onyenga," anati, "inu mungakhoze kuzindikira maonekedwe a mumlengalenga, koma chizindikiro cha nthawi inu simungakhoze kuchizindikira."

54 Ndi icho apo, chizindikiro cha nthawi.

Kodi anamuika mu gulu lanji Iye? "Wotentheka, munthu wamisala." Eya, iwo anapeza cholakwika ndi Munthu Yemwe anali Mawu. Iye anali Mawu. Yohane Woyera, mutu wa 1, amatsimikizira izo, "Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali ndi Mulungu. Ndipo Mawu anapangidwa thupi, ndipo anakhala pakati pathu..."

Iye anali Mawu amoyo a Mulungu, chifukwa Iye anali akufotokozera Mulungu kupyolera mwa Iyemwini. Iye anali kwathunthu wodzipereka ku Mawu a Mulungu, mpaka Iye ndi Mawu anali ofanana. Ndipo ndicho ndendende chimene Mpingo uyenera kukhala uli lero, kuti Mawu a Mulungu ali ofanana. Iwe ungakhoze bwanji kukhala gawo la Mawu amenewo pamene iwe ukuchita kukana onse a Iwo? Ndipo chifukwa chimene izo zakhala ziri, si chifukwa cha anthu; ndicho chifukwa ine ndikuganiza Mulungu anayankhula kwa ine za kuwatcha anthu Ake "Marike" ndi "Mariketa." Ndi chifukwa cha zipembedzo zaumbombo izi, zomwe zawafikitsa anthu amenewo kumakhala kunja uko momwe iwo akukhalira. Iwo akupachika Choonadi. Ndipo anthu amachitcha Icho mwano, ndipo iwo amapangira Icho mwano, kani. Iwo amachitcha Icho kutentheka, ndi zina zotero, ndipo osadziwa kuti iwo akuchitira mwano Mulungu yemweyo amene iwo amapita ku mpingo kuti akamutumikire.

Chotero, ine ndikulitsutsa gulu ili la azibusa lero. Ine ndikutsutsa m'badwo uno, mu Dzina la Yesu Khristu, pansi pa ulamuliro wa Mawu a Mulungu. Inu mukumupachika Iye kachiwiri.

Zindikirani, "Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse," Mawu a Mulungu otsimikiziridwa mwa munthu.

55 Fanizitsani Magologota awiriwa ndi zosumira zawo. Kumbukirani, "Chifukwa Iye ankadzipanga Iyeyekha Mulungu, ife sitikhala naye Munthu uyu kuti azilamulira pa ife." Chinali chiani chosumira chimene iwo akanakhoza kuchipeza, mu upo mmawa ujawo, pamene iwo anamupachika Yesu? Kuti, "Iye ankadzipanga Iyeyekha Mulungu." Iye anali Mulungu. "Ndipo Iye ankaswa Sabata." Ndipo Iye anali Ambuye wa Sabata. Iwo anamuweruza Iye chifukwa kuti Iye ankadzipanga Iyeyekha Mulungu. "Iwe ulibe ufulu woti uzichita izi. Iwe ulibe ufulu. Ansembe athu aakulu, ngati chirichonse chibwera, chimabwera kudzera mwa ansembe athu."

Tsopano fanizitsani izo ndi Gologota walero. Pamene, Mulungu, icho chinawakondweretsa kwambiri Atate, Mulungu Mzimu, kuti amuwutse Mwana Wake Yemwe; anamufungatira Maria, mwa Mzimu Woyera, ndipo anabalapo thupi limene limakhoza kumutumikira Iye ndi kutumikira cholinga Chake kwa Iye. "Mulungu anali mwa Khristu, chidzalo cha Umulungu mwathupi, mwa Iye," akunyezimiritsa chimene Mulungu anali, kwa anthu, kulirola_kulirola dziko lonse lidziwe chimene Mulungu ankafuna aliyense payekha kuti akhale: mwana wamwamuna, ndi wamkazi. Iye anamutenga Munthu mmodzi ndipo anachita izo. Ndipo chifukwa kuti Iye sanajowinane ndi magulu awo achibungwe, iwo anamuweruza Iye ndipo anamupachika Iye.

56 Tsopano fanizitsani Gologota uyo ndi lero. Chifukwa cha kukondera kwa bungwe, chifukwa cha kusagwirizanika pakati pa masikolala omwe amayenera kumawadziwa Mawu a Mulungu ndi dongosolo; chifukwa cha ichi, Mulungu akhoza kutenga kagulu kakang'ono ka anthu komwe Iye angakhoze kugwiriramo ntchito, kwinakwake, ndi kudzinyezimiritsamo Iyeyekha, omwe ati adzazichepetse okha ku Mawu. Ndipo iwo sangakhoze kunena kuti izo siziri chomwecho. Iwo sakanakhoza kunena kuti Iye sanachite izo, pakuti gulu lawo linali mboni za izo. Izo zinali patsogolo pawo. Iwo sakanakhoza kuzikana izo. Iwo sakanakhoza kukana zodzinenera Zake, chifukwa, Mawu omwe amene iwo ankati iwo anali kuwakhulupirira, anali Amodzi Omwe anali atatsimikizira kuti Iye anali. Chifukwa, Mulungu anawatenga Mawu amene ankayenera kuti akhale Mesiya ndipo anawasonyeza Iwo kupyolera mwa Munthu, ndipo iwo ankayenera kuti amuchotsepo Iye. Ndi njira yokha yomwe iwo akanakhoza kumapitirirabe, inali pakumuchotsapo Mesiya. Ndipo iwo anachita izo kupyolera mu khungu ndi umbuli, mosasamala za maphunziro awo. Iwo anali anzeru, aluntha; kuyankhula mwachidziko. Monga ife tinafanizitsa usiku wina, pamene Kuwala kunamugunda bwana wachinyamata wolemera, onani chimene iye anachita. Iye anakana; munthu wanzeru. Paulo, munthu wina wanzeru, Kuwala kunamugunda iye. Kodi iye anachita chiyani? Iye anakuvomereza Iko. Iye anaiwala izo, zonse zomwe iye anayamba wazidziwa, kuti iye akakhoze kumudziwa Khristu. Icho chinapanga moyo wake kukhala woyenera kwa Uthenga. (Uthenga wa usiku wa Lamlungu latha.)

57 Apo izo ziri lero. Iko kukumugunda mwinamwake munthu wina wamng'ono, yemwe anapita kumbali, ali nako kuitana kwa Mulungu, iye anamverera, anapita ku seminare inayake ndipo anakaphunzira kachikhulupiriro kenakake. Iye ayenera kumakhala moyo mwa kachikhulupiriro kameneko kapena kusiyana nalo khadi lake la chiyanjano. Ngati iye atero, iye amakhala ndi chilemba chakuda, palibe aliyense angamulandire iye, chifukwa nthawi ina iye anali waku chinachake ndipo tsopano iye sali wa icho. Iwo amalingalira kuti pali chinachake cholakwika ndi munthu ameneyo, ndipo iwo sangakhale naye iye mu msonkhano wawo. Pamene, osonkhana akungoyang'anira chizindikiro chimodzi, icho ndicho, ngati iye akukhulupirira chimene iwo amakhulupirira. Ngati iye ali nayo khadi, ngati iye ali wa Methodisti, ngati iye ali ndi khadi...iye ndi wa chiyanjano china, kapena Waumodzi, kapena Wautatu, kapena chirichonse chimene icho chingakhale chiri, mpingo wa Mulungu, kapena mu magulu a Chipentekoste, ndi magulu ena onse awo. Ngati iye akunyamula khadi, iwo amamverera kuti likulu lamufufuza iye bwinobwino, ndipo lawayesa malingaliro ake, ndi kumupatsa mayeso ofufuza misala, ndi kuwona ngati I.Q. yake inali yokwera mokwanira kuti iye angakhoze kuyankhula pamaso pa iwo. Ngati iye satero, iwo amamukana iye. Ndiko kulondola.

58 Koma, inu mukuona, osonkhana ayenera kukhala akumayang'anitsitsa dzanja la Ambuye, kuwona ngati Mulungu wamupatsa iye kudzoza kwake kapena ayi. Ndicho chimene ife tikuyenera kukhala tikumayang'anapo. Koma lero iwo akumupachika Mwana wa Mulungu katsopano. Pamene, munthu ali wokhoza, mwa chisomo cha Mulungu, kukhala woitanidwa ndi Mulungu, kuti amulole Mulungu kuti adzinyezimiritse Iyeyekha kupyolera mwa iye. "Ntchito zimene Ine ndizichita inu mudzazichita inunso," Iye anatero.

Zindikirani ndi tsiku lanji lomwe ife tiri kukhalamo! Iwo, iwo akutenga, iwo akutenga Gologota yomwe, ife tikhoza mmawa uno, ndipo chifukwa chomwe. Tsopano, iwo ankadziwa kuti icho chinali Choonadi; koma chifukwa cha nsanje, kukondera. Kodi Yesu anati chiyani kwa iwo? "Ngati Ine ndikutulutsa ziwanda ndi chala cha Mulungu, ndiye ndani_inu mukutulutsa izo ndi yani? Aloleni iwo akhale okuweruzani anu,

mukuona, ngati Ine ndi chala cha Mulungu ndikutulutsa ziwanda."

Tsopano, basi monga inu munawamva iwo akuti, "Kodi inu mungatsimikizire kuti ndi chala cha Mulungu?" Ine ndimafuna kuti ndiwone, ine ndikanafuna nditalimva funso limenelo akumufunsa Iye. Iwo anali anzeru mokwanira kwa ilo.

Zindikirani, "Chifukwa kuti Iye ankadzipanga Iyeyekha Mulungu," ndipo Iye anali Mulungu. "Ndipo ife sitikhala naye Iye kuti azilamulira pa ife."

59 Koma tsopano chinthuchi, kulira komwekuja kwachikale kukubwera kachiwiri, "Baibulo ilo linalembedwa ndi munthu," iwo amatero. "Ife sitikusowa kumakhala moyo mwa Ilo." Ilo ndi Mulungu^Awo ndi Mawu a Mulungu. Ndi Mulungu, Mwini wake.

Ine ndinali kuyankhula kwa munthu dzulo, anati, "Chabwino, munthu wina ayenera kuti analemba Baibulo limenelo."

Ine ndinati, "Inde, analipo. Dzina Lake, ife timamudziwa Iye ngati Mulungu." Ilo linalembedwa mu zaka zikwi zinai motalikana, pafupifupi, Malemba, mmbuyo kuyambira kwa Yobu, njira yonse mpaka ku Chipangano Chatsopano, ndipo linalembedwa ndi mazana mwa_mwa^ndi mazana a zaka kutalikirana; ndipo linalembedwa ndi anthu osiyana, ndipo iwo asakudziwana ndi enawo, mu madera osiyana a dziko, ndipo palibe Mawu amodzi a Ilo ati adzatsutse winayo. Ine ndikulimba mtima kumufunsa aliyense kuti abwere pansi pa Magazi a Yesu Khristu ndi kutenga lonjezo lirilonse mkati Mmenemo! Mulungu ali wokakamizika kuti azilisamalira Ilo. Koma iwo sangachite izo. Iwo amabwera, nati, "O Ambuye, ine ndikufuna kuti ndichite chinachake. Ndipatseni ine mphatso yaikulu. Aleluya, Ambuye! Ulemerero kwa Mulungu, ine ndikukhulupirira ine ndiri nayo iyo. Aleluya!" Izo sizidzagwira konse ntchito. Iwe ukhoza kubweretsa kuwerenga maganizo kochuluka, koma izo sizingagwire ntchito. Mulungu ayenera kukuzindikira kulapa kumeneko. Mulungu ayenera kuzichita izo. Ife tikhoza kunena zochuluka motsatira mzere umenewo, koma ine ndikuyembekeza inu_inu mukumvetsa.

60 Penyani, koma tsopano iwo sakhala nawo Mawu kuti aziwalamulira iwo. Ine ndikati, "Mmodzi aliyense wa inu mubwerere mmbuyo. Inu munabatizidwa molakwika. Inu munabatizidwa mwa mpingo wa Katolika."

"Ndiwe ndani kuti utiuze ife zimenezo?" Si ine ayi; ndi Mawu. "Koma ine ndikukuuzani inu, ife_ife tikukhulupirira..." Ine sindikusamala chimene inu mukhulupirira; ndi chimene Baibulo limanena. "Koma ife sitisowa kumakhala moyo mwa Ilo." Inu muzichita izo, kapena inu muli pansi pa chiweruzo cha Baibulo ili. Pakuti, "Aliyense yemwe ati adzachotse Mawu amodzi kuchokera kwa Ilo, kapena kuwonjezera amodzi kwa Ilo, yemweyo adzachotsedwa kuchokera, ku gawo, la Bukhu la Moyo," kaya iye akhale mtumiki, mlaliki, kapena aliyense yemwe iye ali. Inu muyenera kubwera pansi pa ulamuliro wa Mawu awa, pakuti Iwo ndiwo Mulungu. Baibulo limati Iwo ndi Mulungu. "Ife sitikhala nawo Iwo kuti azilamulira pa ife." Iwo amatenga tizikhulupiriro tawo, ndi zipembedzo, ndi tinthu tawo tating'ono timene iwo amakhulupiriramo, ndipo ito tatengedwa ndi maupo a anthu, ndipo atenga izo mmalo mwa Mawu a Mulungu.

61 Kodi iwo anachita chiyani? Iwo anatenga Barabasi, wakupha, mmalo mwa Mwana wa Mulungu, pa tsiku la kupachikidwa koyamba. Ndipo lero iwo akutenga mawu a munthu wina, lomwe liri bodza ndi njira ya imfa, ndipo akumakana kuti atenge njira ya Moyo, Mawu a Mulungu. Ine ndikuwuweruza m'badwo uno, ndikuwutsutsa iwo, mwa Mawu a Ambuye, kuti iwo ali olakwa. Iwo ndi olakwa pa kumupachika kapena kuyesera kuti awupachike Mzimu...

62 Iwo akumaitanitsa chitsitsimutso, kulikonse. Inu mukhala nacho chitsitsimutso motani pamene Mawu Iwoeni sangakhoze kugwira ntchito kupyolera mwa anthu? Ine ndikufuna wina kuti andiyankhire ine izo. Izo zingakhoze kuchita motani, pamene inu mukuchikana Chitsitsimutso chomwe Mwiniwakecho? Mwabwino mneneri anayankhula za iwo, "maonekedwe aumulungu." Maonekedwe awo omwe, mmbuyo umo, anawakana Mawu a Moyo. Maonekedwe awo omwe, lero, akukana chinthu chimene chingakhoze kuwabweretsera iwo chitsitsimutso; tizikhulupiriro tawo ndi maonekedwe. Inde, bwana. Iwo amatenga chipembedzo ndi tizikhulupiriro tawo mmalo mwa Mawu, ndipo izo zimapachika Mawu Ake ndi kumawapangitsa Mawu Ake opanda mphamvu kwa anthu. Pamene iwo awaona Mawu a Mulungu mowonekera bwinobwino ndi kungodziyika Okha, kuti Mulungu anapanga lonjezo kuti Iye akanadzachita izi, ndipo pano Iye akuchita izo, ndipo iwo amawaseleula Iwo ndi kuchoka kwa Iwo, ndiko kuchitira mwano. Ndipo iwo akuyesera kuti aziwapachika Mawu Iwoeni. Iwo akuwapachika Iwo motani? Iwo sangakhoze kuwapachika Mawu koposa momwe iwo angakhoze kumupachika Mulungu. Iwo akhoza kulipachika thupi limene linagwirizira Mulungu, Mwana wa Mulungu. Iwo akanakhoza kulipachika ilo, koma iwo sangakhoze kumupachika Mulungu. Iye ankayenera kuti akhale, nthawi imeneyo, pa nkhani ya kuti akhale Nsembe, kuti abweretsemo ana aamuna ambiri omwe ali okonzedweratu ku Moyo Wamuyaya. Iwo ankayenera kuchita izo pamenepo, koma iwo sangakhoze kuchita izo tsopano. Iwo sangakhoze kuchita izo, pakuti Mawu Iwoeni adzakhalapobe. Koma iwo...

63 "Kodi iwo akuchita chiyani? Kodi iwo akupangika motani? Kodi inu mukunena chiyani ndiye, mlaliki? Inu mukumanga chotani nsanja yanu apa, kuti iwo akumupachika Iye, ndiye?" Iwo akupachika mphamvu za

Uthenga pa anthu, ndi tizikhulupiriro tawo. Ndiko kupachika. Ndi kumene anthu akumakhala mu nyumba zachisoni zazikulu izi, zotchedwa mipingo, zipembedzo, ndi kumalemba mzere wa kachikhulupiriro, ndipo Mawu a Mulungu sangakhoze kukhala nayo mphamvu pa iwo, chifukwa iwo akunyoza zinthu zomwezo zimene Khristu anati zikanati zidzachitike. Izo sizikubwera basi molingana ndi kachikhulupiriro kawo. Ndipo ngakhale Yesu sanabwere molingana ndi kumvetsa kwawo kwa Iye pobwera. Iye anabwera mwa njira yomwe Mulungu anamutumizira Iye, ndipo Iye anabwera ndendende ndi Mawu. Palibe zodabwitsa Iye anati Iye anali "atazibisa Izo kwa maso a anzeru ndi aluntha, ndipo anaziulula Izo kwa makanda monga omwe akanati aphunzire." Kodi inu mukumvetsa?

64 O, iwo akupachika mphamvu ya mawu.

Ine ndiri nawo mulu wa Malemba pano. Ine mwina ndingati ndingowerenga awiri kapena atatu a iwo. Iwo akuwapachika Iwo. Inu mukuti, "Kodi iwo akuwapachika chotani Mawu?" Pamene Yesu anati kuti Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse, Ahebri 13:8; iwo akuti, "Mwanjira yakutiyakuti Iye ali." Mwaona? Chabwino. Ndipo Yesu anati, lamulo Lake lotsiriza kwa Mpingo, "Pitani inu ku dziko lonse," Marko 16, "pitani inu ku dziko lonse, ndipo kalalikireni Uthenga. Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira. Dziko lonse; kwa cholengedwa chirichonse!" Ndipo ilo silinafikidwe thekha panobe. Ndipo alipo mamilioni akufa, chaka chirichonse, omwe sali, omwe sanayambe konse amvapo Dzina la Yesu. Kotero, ilo likadali lamulo laaliyense. Ilo likadali lamulo la Mulungu. "Dziko lonse, ndipo kalalikireni Uthenga kwa cholengedwa chirichonse. Iye amene ati akhulupirire nabatizidwa adzapulumutsidwa; iye amene sakakhulupirira adzawonongedwa. Ndipo zizindikiro izi ziwatsatira iwo amene ati akhulupirire: mu Dzina Langa iwo adzatulutsa ziwanda; iwo adzayankhula ndi malirime atsopano; ngati iwo atenga njoka, kapena kumwa zinthu zakupha, izo sizidzawapweteka iwo; ngati iwo ayika manja awo pa odwala, iwo adzachira." Ndipo iwo amati, "Izo zinali za m'badwo umenewo," ndipo iwo amawapanga malamulo a Mulungu kukhala opanda- mphamvu kwa Awa, ndipo iwo akupachika mphamvu ya Mawu kwa anthu. Ameni.

65 Petro anati, pa Tsiku la Pentekoste, ali ndi mafungulo aku Ufumu;

Omwe Yesu anali atangomupatsa iye, "Chirichonse chimene iwe uti unene kuno, Ine ndidzachinena icho kumwamba Uko." Ndipo pa Tsiku la Pentekoste iwo anafunsa chimene iwo akanati achite kuti alandire Mzimu Woyera, amene iwo anali akusangalala nawo Iwo; akuwapenya ena akumachita chimene iwo akanachitcha kupusa; akuzandima, ndi kudumpha, ndi kugwa, ndi kumachita ngati iwo anali ataledzera. Ndipo iwo, kumati, "Anthu awa akhuta vinyo watsopano."

66 Koma apo panali mwamuna yemwe anaimirira, dzina lake Petro, yemwe anali nawo mafungulo aku Ufumu, ndipo anati, "Awa sali oledzera," Machitidwe 2, "monga inu mukuganizira, powona kuti ndi ora lachitatu la tsiku. Koma ichi ndi chija chimene chinayankhulidwa." Onani, kubwerera kumene ku Mawu kachiwiri, kusonyeza kuti Mzimu ukadali Mawu, ndipo Mawu akadali Mzimu, Mawu a Mulungu. "Ndipo izo zidzachitika, monga zinayankhulidwa ndi mneneri Yoeli, Yoeli 2:38. 'Ndipo kudzachitika mu masiku otsiriza, atero Mulungu, Ine ndidzatsanulira Mzimu Wanga pa mnofu wonse.' " Mvetserani kwa mneneri ameneyo ataima apo. Tayang'anani pa iye, wopanda mantha, ataima pamenepo pa gulu limenelo, ndipo akuwaweruza iwo, akuwatsutsa iwo. Anati, "Ili ndi Lemba! Ichi ndi chija chimene chinayankhulidwa ndi mneneri! 'Ine ndidzatsanulira Mzimu Wanga pa mnofu wonse. Ana anu aamuna ndi aakazi adzanenera. Pa adzakazi Anga ndi antchito aakazi Ine ndidzatsanulirapo Mzimu Wanga; ndipo Ine ndidzasonyeza zizindikiro mu miyamba mmwamba, ndi pa dziko lapansi; moto, ndi mizati ya utsi, ndi nthuzi.'" Kutsimikizira Izo mwa Mawu, kuti Izo zinali Mawu. Ndipo iwo anaseka ndi kuzitonza Izo, ndipo iwo anapita ku chiweruzo. Ndipo mzindawo unawotchedwa, ndipo iwo anadyerana ana a wina ndi mzake. Ndipo lero iwo ali anthu omwazikira konsekonse mu dziko, kusonyeza kuti Mzimu Woyera ukadali Mawu a Mulungu, kuti ubweretse Mawu awa kuti uwapangitse Iwo kukhala amoyo.

67 Yesu Khristu anali Munthu, Mwamuna, Mulungu. Aleluya. Iye anali chiwonetsero cha Mulungu. Iye anali Mulungu mwa maonekedwe a thupi, kuti anyezimiritse Mawu a Mulungu a m'badwo umenewo, kuti awupange m'badwo umenewo kuwona lonjezo la Mulungu la m'badwo umenewo.

Ndipo Mzimu Woyera uli chinthu chomwecho lero. Ndi Mzimu wa Mulungu pa Mawu olembedwa, kuyesa kuti umupeze winawake woti udzinyezimiritsiremo Wokha kwa m'badwo uno, kuti utsimikizire kuti Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Yohane Woyera 14:12, "Ntchito zimene Ine ndizichita inunso mudzatero." "Yesu Khristu ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse." Mwaona, mowirikiza kuyesera kuti upeze njira Yake kuti udzinyezimiritse Iwowokha.

Ndipo iwo sakanakhoza kuchita izo. Anthu ankaganiza zochuluka kwambiri za zipembedzo zawo, zisa zawo zazing'ono zomwe iwo anali nazo, ndi zina zotero, zotchedwa "mipingo," yawo kotero iwo samakhoza kumvetsera kwa izo. Kotero iwo akuchita izo lero, chinthu chomwecho, kumupachika mwatsopano.

68 Petro, pa Tsiku la Pentekoste, iye anati, "Inu amuna amene mukukhala mu Yerusalemu, mu Yudea, mvetserani ku mawu anga. Awa sali oledzera. Ngati inu muti mukhale bata, ine ndikusonyezani inu

chimene icho chiri.” Ndipo iye akupitirira apo ndi kuzifotokoza kwa iwo. Pamenepo mitima yawo inalaswa, pamene iwo anamva Ichi, anati, “Kodi ife tingachite chiyani kuti tikhale opulumutsidwa? Kodi ife tingakhoze kuchita chiyani kuti tilandire Uwu? Ife takhutitsidwa kuti mawu anu ali olondola.”

Iye anati, “Lapani, mmodzi aliyense wa inu, ndipo mubatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu kwa chikhululukiro cha machimo anu, ndipo inu mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera. Pakuti izi ziri kwa inu ndi ana anu, iwo amene ali kutali, ngakhale ochuluka monga amene Ambuye Mulungu wathu ati adzawaitane. Ichi ndi chimene iwo ayenera kuti achite. Lapani, ndipo mubatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu.”

69 Ndipo, lero, mpingo wa Roma Katolika unatenga, “Atate, Mwana, Mzimu Woyera,” kuti zitenge malo Ake. Mmalo mwa Ilo, mgonero. “Kutulutsa kunja lirime ndi kudya kokulumunya, ndipo wansembe nkumwa vinyo, ndipo ndinu amodzi palimodzi.” “Mgonero,” mmalo mokhala Mzimu Woyera, umatchedwa, “Ukalisitiya woyera.” Ndipo “Atate, Mwana, Mzimu Woyera,” ubatizo wa utatu, pamene izo sizinayankhulidwe nkomwe mu Baibulo. Dzina la Atate, Mwana, Mzimu Woyera ndi Ambuye Yesu Khristu. Ndipo pamene iwe usonyeza izo kwa m'badwo wokhotakhota uno Monga Petro anati, “Zipulumutseni nokha ku m'badwo wokhotakhota uno.” Pamene iwe usonyeza Izo kwa iwo, kodi iwo anachita chiyani? Anaziseka Izo, ndi kuti, “Mpingo wathu sumaphunzitsa Izo mwanjira imeneyo.” Ndiye ndinu olakwa, ndinu olakwa pa kupachikidwa kwa Yesu Khristu, pa kuchotsa Mphamvu ya Mulungu yomwe kwa anthu. Inu mukuwapachika Mawu omwe kwa iwo, ndipo inu mukudziweruza nokha ndi osonkhana nanu, kuwatsogolera iwo ku msampha wa imfa.

70 Monga ine ndinanena za mtumiki uja Lamlungu latha, anali Marteni Lutera Mfumu kumusi uko ndi anthu ofunika awo, kuwatsogolera iwo kupita ku msampha wa imfa womwe. O, ngati wina akanangokhoza kukayankhula kwa munthu ameneyo! Ndikukhumba ine ndikanatero. Kuwukira pang'ono chabe kwa lingaliro la ku sukulu, mwaona, kapena zina^ Nzosiyana bwanji? Mai, ubwino! Ngati anthu alibe mtima wokwanira kuti aziyanjana naye munthu chifukwa cha khungu lake, iwo aweruzidwa ndi akufa, mulimonse. Fuko limawapatsa iwo ufulu. Musati muzimenyana nazo izo. Musatero...

Bwanji ngati wina atati achi Irishi onse kapena winawake, achi German onse, kapena winawake, akanati asamayanjane nawo? Izo sizikanati ziwavute Akhristu. Iwo akanati azipitabe patsogolo. Ndipo munthu uyo ndi Mkhristu. Monga mtumiki, iye sayenera kumawatsogolera anthu awo mwa kuwukira potsutsa izo. Iwo apangitsa mamilioni kuti afe. Izo ziyambitsa kuwukira kwina. Ndipo ndi chamanyazi kuti azichita zimenezo.

71 Chinthu chomwecho chikuchitika komwe kuno. Ndendende chinthu chomwecho kachiwiri. Ndiko kulondola. Mwaona? Anthu, bwanji ngati iwo akanati angoyang'ana pa Choonadi ndi kuwona chomwe Choonadi chiri. “Mpingo wathu sumakhulupirira zimenezo. Ife tiri nayo njira yina.” Chabwino, iyo sindiyo njira yolondola. Iyo sindiyo chinthucho.

Iye anati, “Lapani, ndipo mubatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu kwa chikhululukiro cha machimo.” Tsopano iwo sangati achite izo. O, ndiye kodi iwo anachita chiyani? Tsopano icho ndi chinthu chimodzi chokha, pa mazana. Ife tifika ku izo, mwinamwake, mofulumira monga ife tingakhozere.

72 Tsopano kupachikidwa kwachiwiri, ndiye. Ngati munthu avomereza “Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera,” ka_kachikhulupiriro mmalo mwa Mawu, maudindo mmalo mwa Dzina, kodi iye akuchita chiyani kwa anthu? Iye akupachika mphamvu ya Mawu kwa anthu, pamene iye anena, kuti, “Marko 16 anali wa m'badwo umenewo kokha.” Ndipo Mulungu anati, Iyemwini apo pomwe, Yesu akuyankhula kwa iwo, anati, “Pitani inu ku dziko lonse, ndipo kalalikireni Uthenga kwa cholengedwa chirichonse. Iye amene akhulupirira ndi kubatizidwa adzapulumutsidwa; iye amene sakhulupirira adzawonongedwa. Ndipo zizindikiro izi zidzawatsatira iwo^” Mpaka kuti? Fuko lirilonse, kachikhulupiriro kalikonse, lirime lirilonse, mtundu uliwonse, anthu aliwonse, Uthenga womwewo. “Ndipo zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akukhulupirira.” Ndipo pamene munthu ayesera kuti azizidulamo izo kuzichotsa mu Baibulo, iye akupachika mphamvu za Uthenga kwa gulu limenelo. Kotero ine ndikukutsutsani inu, mu Dzina la Yesu Khristu! Inu muli olakwa pa kumupha Ambuye!

73 Mpingo unkamuda Iye. Chifukwa chiyani? Iye anali Mulungu wawo yemwe. Iwo ankamuda Iye, ndipo anamukana Iye kuti akhale Mesiya wawo. Ayi, bwana, iwo sanali kufuna Mesiya wonga ameneyo. Ndipo lero mpingo ukuchita chinthu chomwecho. Iwo ukuwakana Mawu. Iwo sali kuwafuna Iwo. Iwo ndi osiyana ndi chimene iwo anakhala akuphunzitsidwa kuti azikhulupirira ndi tizikhulupiriro tawo. Ndipo Mawu ndiwo Mesiya. Inu mukukhulupirira izo? Chabwino, chinyezimiritso cha Mawu ndiye ndi chiyani? Kunyezimiritsa Mesiya, chimene chiri Mzimu Woyera pakati pathu. Iye akudzinyezimiritsa Iyeyekha, kuyesera kutero, paliponse pamene Iye angakhoze kupeza nyali yomwe Iye angakhoze kuyang'aniramo, yomwe siyinachite utsi ndi tizikhulupiriro ndi zinthu, Iye akhoza kudusitsiramo Kuwala.

74 Kumbukirani, “iwo anawuka ndipo anakonza nyali zawo,” ndi kutsuka motulukira utsi, koma izo ndi mochedwa kwambiri. Kotero pamene munthu awaona Achilutera awa, Achipresbateria, Amethodisti, akuyesera kuti abweremo mu masiku otsiriza ano kuti adzalandire Mzimu Woyera, bwanji, inu mukudziwa iwo samaulandira Iwo. Chabwino, iwo akhoza kuyankhula mu malirime ndi kudumpha mmwamba-ndi-pansi,

koma penyani chimene chimachitika. Iwo mwamtheradi^ Ndicho chizindikiro cha nthawi kuti iwo watha. Ife tiri ku mapeto. Pafupi nthawi iliyonse, Mpingo ukhoza kumva mpikisano, kuti, "Ubwere mpaka mmwamba!" Ameni. Chimodzimodzi basi zikuikidwa ndithu mu dongosolo. Mzimu Woyera pano ukumupanga Yesu Khristu chenicheni kupyolera mwa iwo amene Iye angakhoze kugwiriramo ntchito, kudzitsimikizira Iyeyekha; kubwera pansi, kujambulitsa chithunzi Chake, kuchisonyeza icho, kupangitsa sayansi kuzitenga, kuyankhula za izo, ndi china chirichonse, kutsimikizira chimodzimodzi basi chimene Iye anati Iye akanadzachita. Kuchita chimodzimodzi zinthu zomwe Iye anati Iye akanadzachita, Mwamalemba. Tsopano, osati kachikhulupiriro kena, kapena lingaliro lopangidwa ndi munthu wina, magazi ochuluka, moto, ndi utsi, ndi zinthu; koma umboni wa Mwamalemba wa Umesiya.

Ziri nawo zosanzira zambiri, ndi osanzira, ndi_ndi zina zotero; koma izo zikungopangitsa Mawu enieni kuti Iwo aziwala mwakupambana kwake, ndiko kulondola, kuwalola anthu omwe ali auzimu, omwe angakhoze kuweruza pakati pa cholondola ndi cholakwika. Mwaona?

75 Akumukana Iye! Anamukana Mesiya wawo, "Ife sitinamufune Iye." Ndi chinthu chomwecho iwo akuchita lero, "Chabwino, ngati ine ndinali woti ndipite kumusi uko ndi kumakachita monga gulu ilo, ine sindikuzifuna Izo konse." Chabwino, ndiye iwe ulibe Iwo, konse. Ndizo zonse. Mwaona? Nzofanana tsopano.

Ngakhale Iye anali atazindikiritsidwa bwinobwino, iwo sankamufuna Iye. Iwo ankamuda Iye. Izo zinali chifukwa chiyani? Iye ankawatcha azibusa awo mulu wa "njoka." Iye anati, "Inu gulu la makoma oyera. Sindinu kanthu koma manda. Kunja kwa inu muli okongoletsedwa ndi mikanjo ndi makolala otembenuzidwa, ndipo mkati ndinu mafupa a anthu akufa." Mwaona? Iye sankabweza nkhonya ayi. Mgalileya mmodzi wamng'ono, mwana wa akalipentala, koma Iye sankabweza nkhonya ayi. Iye ankawauza iwo.

"Musati muziganiza," Yohane anati, wotsogolera kudza wa Iye, anati(Iye ali wina yemwe sankabweza nkhonya iliyonse.) Iye anati, "Musati muzibwera cha kuno mukumati muli naye Abrahamu ngati atate wanu. Mulungu ndi wokhoza mwa miyala iyi kuwukitsa ana kwa Abrahamu." Inde, bwana. "Nkhwangwa yaikidwa ku muzu wa mtengo, ndipo mtengo uliwonse umene subala chipatso udulidwira pansi ndi kuponyedwera kumoto." Inde, bwana. Mulungu ndi wosamalitsa, ndi wolimba ndi wokhazikika ndi Mawu Ake. Inde, bwana.

76 Zindikirani, Yesu, wotsimikiziridwa ndi Lemba... Kodi inu mukundimva ine? Yesu anazindikiritsidwa ndi Mulungu kupyolera mu Malemba, kuti Iye anali Mesiya. Ndi kulondola uko? Ife tifika ku chitsutso cha Petro, mu maminiti pang'ono, ndipo inu mupeza ngati izo zinali kapena ayi. Iye anali atatsimikiziridwa bwinobwino, kuti Iye anali Mulungu atawonetseredwa mwa Munthu, wotchedwa Mwana wa Mulungu. Ndiko kulondola. Ngakhale, Iye anali atazindikiritsidwa bwinobwino ndipo atavomerezera Mawu olonjezedwa, kuti Iye anali Mesiya. Mose anati, "Mesiya uyu, pamene Iye abwera, Iye adzakhala ali mneneri," ndipo zinthu zonse izi zidzachitika. Mkazi wamng'ono ali^ataima pa chitsime, ndi chikhalidwe choipa chonse icho chomwe iye anali, kodi izo zinkaphiphiritsa chiyani? Kuti Mulungu mu masiku otsiriza ano adzakokamo otaidwa kunja.

77 Mukukumbukira usiku watha, chikwati...Kapena, nthawi yina yomwe ine ndinalalikira pano. Pa mgonero wa chikwati, iwo ananena momwe iwo ananenera. "Ine ndakonza phwando lalikulu, ndi zina zotero. Ndipo anthu onse awa, ine ndawaitana iwo, ndipo mmodzi aliyense anali nacho chowiringula.

'Ine sindingakhoze kuchita izo, chifukwa izo zingawononge tizikhulupiriro tathu. Ine sindingakhoze kubwera, chifukwa ine ndiri naye wanga...Ine ndakwatira mkazi; iye sandirola ine kuti ndibwere.

Ine ndakwatiwa kwa mpingo kumusi kuno. Mayi anga anali a Methodisti, kapena Abaptisti, kapena Akatolika, kapena, Ine sindingakhoze basi kuima kuti ndichite Izo.' "

Iye anati, "Ndipo inu simunafune kubwera? Ndipo inu simudzalawa mgonero Wanga! Koma pitani kunja uko ndipo kawakakamizeni aziwerewere ndi mahule, ndi zidakhwa, ndi alionse omwe alipo. Kawabweretseni iwo muno, ndipo Ine ndidzawawongola iwo. Ine ndakonza mgonero Wanga, ndipo Alendo anga...gome langa lakonzedwa, ndipo kuyenera kukakhala kuli winawake kumeneko." Iwo sanabwere. Iye anali akuwaweruza Ayuda amenewo. Nanga bwanji lero?

"Ine ndine wa Presbateria. Ine sindingakhoze...

Ine ndine wa Chilutera.

Ine ndine waumodzi.

Ndine wauwiri.

Ndine ichi. Ine sindingakhoze... Ine sindingakhoze...

Ndi inu pamenepo. Inu simukakhala muli kumeneko ndiye! Ndizo chimodzimodzi zimene Iye ananena.

Chabwino.

78 Anatsimikiziridwa bwinobwino, Mesiya. Anatsimikiziridwa bwinobwino, Mawu, Mawu olonjezedwa. Mulungu yemwe analonjeza Mawu, kuti ichi ndi chimene Mesiya akanati adzakhale, apa Iye anabwera ndipo anaima ndendende. Iye anati kwa iwo, "Tsopano, ndi pati pamene Ine ndalephera? Ngati inu simungakhoze kundikhulupirira Ine ngati Munthu, khulupirirani ntchito zimene Ine ndikuzichita; pakuti izo ziri zinthu zomwe zikufotokoza Yemwe Ine ndiri. Izo ziri zomwe zikunena kuti ndine Mesiya. Inu simukufuna kuti mundikhulupirire Ine, chifukwa inu mukuganiza kuti_ kuti Yosefe uko^Ndipo ine ndinabadwira kumeneko mu kanyumba kakang'onoko, ndipo bambo anga ondilera kuno ndi kalipentala kumusi uko. Ndi inu..."

79 Pamene Iye anabwera ku Galileya uko, iwo, ndipo ankati apange...Iye anati, "Hei, Ndi ndani Munthu uyu? Ndi ndani Uyu? Chabwino, Munthu uyu, sali uja...Kodi sali a Joses ndi onse aja abale Ake kuno? Kodi sali achemwali Ake ndi ife? Kodi Mayi Ake sakutchedwa Maria, ndipo bambo Ake amatchedwa Yosefe? Kuti, kodi inu munamutenga kuti Munthu wonga ameneyo? Ndi sukulu iti yomwe Iye anachokerako? Iye alibe khadi la chiyanjano. Iye alibe nyota zirizonse. Kodi munthu wonga ameneyo...Kodi inu munamutenga kuti uyu, chonchobe?"

Ndipo Baibulo linati Iye anakhumudwitsidwa. Iye anati, ntchito zambiri zamphamvu Iye sakanakhoza kuzichita; ndipo anatembenuza nsana Wake ndipo anapita nachoka kwa iwo. Iye anati, "Mneneri amakhala wopanda ulemu akakhala pakati pa abale ake omwe pokha, mwaona, kwawo komwe," penyani, "kapena kumudzi kwawo komwe."

Ndi Uyo apo, atatsimikiziridwa bwinobwino, Mesiya. Sanali kutenga mayamikiro Akeake. Iye ankati, "Ine sindingakhoze kuchita kanthu koma chimene Ine ndiwawona Atate akuchita." Ndipo Iye anawatsutsa iwo kuti akafunse ngati ameneyo sanali Mesiya.

80 Ndipo tayang'anani pa kamkazi ka mbiri yoyipa kachikulire kaja; iye anazindikira izo. Iye, sanali atamwera izo. Nyali...Iye anali mwamakhalidwe wolakwa, ndithudi. Palibe mmodzi yemwe akanavomereza izo. Malamulo a Mulungu amatsutsa izo. Iye anali mwamakhalidwe wolakwa. Koma iye... Mwaona, Mulungu samakuweruza iwe pa chimene iwe uli. Iye samaweruza ndi momwe iwe wakulira kapena momwe iwe wachepera. Iye amaweruza mtima wako, chimene iwe ukufuna kuti ukhale. Ndipo iye sanali kufuna zirizonse za zinthu izo. Ndipo pamene Ichi chinawalitsidwa patsogolo pake, Ndicho chimene iye ankachifuna. Ziribe kanthu chimene iye anali panthawiyo, iye anali wokonzeka kuti abwere. Mwaona? Mulungu amaweruza mtima. Munthu amaweruza mawonekedwe akunja. Mulungu amayang'ana pa mtima. Ziribe kanthu chimene iye anali; Kuwala kuja kunawalira, ndipo izo zinakhazikitsa icho. Iye anagwira chenicheni cha Moyo Wamuyaya.

81 O, maine, ndi zolemera bwanji izi ziri, kwa ine, onani, kuziwona ndi kudziwa kuti izo ndi Choonadi. Ine ndizi_Ine ndiziima ndi Ichi. Ine ndilola^Mulungu wa Kumwamba adzaukitsa, ndipo liwu langa lidzakhala liri pa tepi ya maginito ya Mulungu ya nthawi yayikulu kutsidya, ndipo iyo idzatsutsa m'badwo uno mu tsiku lotsiriza. Chifukwa, izo_izo ziri pa tepi ya maginito, ndiye izo zidzakhala pa tepi Yamuyaya apo. Ndiko kulondola. Kuwutsutsa m'badwo uno wa alaliki omwe ali nawo mawonekedwe aumulungu, ndi kumakana Mphamvu ya Mawu ndi mawonetseredwe Ake pamene Iwo azindikiritsidwa bwinobwino kuti Iye akanali Yesu Khristu, yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Ine ndikuwatsutsa iwo, mwa Mawu a Mulungu.

Ine ndiyenera kufika ku lonjezo lina, mwamsanga, chifukwa ife tiri nawo pafupi maminiti khumi ndi asanu okha.

82 "Kumeneko iwo...kumeneko iwo.." Chiyani? O, maine! Gologota. Ndipo iwo "anamupachika" Iye, chachitatu. Iwo anamupachika Iye, osati pa kuzindikira lonjezo la Mulungu la Mawu atachita kuwonetseredwa. Ndipo nchifukwa chiyani iwo anamupachika Munthu ameneyo? Kodi inu mungakhoze kungolingalira? Ndiroleni ine ndipite mmbuyo miniti. Nchifukwa chiyani anthu amenewo akanakhoza kumupachika Munthu wonga ameneyo?

Monga Maria...Monga ine ndinawerenga bukhu nthawi ina, lotchedwa Kalonga wa Nyumba ya Davide. Ilo linalembedwa ndi Ingraham, Dokotala Ingraham. Bukhu lodabwitsa! Ilo ndi sewero, ilo likuyenera kukhala mwatheka loona, la zolembedwa zina zakale zinatengedwa kuchokera kwa mkazi dzina lake Edina, Iye anapita ku Palestina, kuchokera uko mu Igupto, kupita ku Cairo, ine ndikukhulupirira izo zinali, kuti akatsirizitse maphunziro ake. Ndipo iye anali ali kumeneko pa nthawi ya Khristu, ndipo iye ankayenera kuti aziwalembera abambo ake moyankha. Izo zikanakhala bwino ngati inu mukanalitenga ilo ndi kuliwerenga ilo. Ilo, ndi labwino kwenikweni, Kalonga wa Nyumba ya Davide. Munthu yemwe uja yemwe analemba Lawi la Moto; ndipo, kuchokera kwa ilo, Cecil DeMilles anatengamo Malamulo Khumi.

83 Tsopano ife tikupeza kuti, mu bukhu ili, Edina uyu analemba moyankha. Ndipo iye anati, pa tsiku la kupachikidwa, kuti Maria Magadala, mwa yemwe Iye anatulutsamo ziwanda zisanu ndi ziwiri, anathamangira patsogolo pa unyinji, anati, "Kodi Iye wachita chiyani? Kodi Iye wachita chiyani? Kuchiritsa kokha odwala ndi kuyesa kuti awawombole iwo amene anali mu ndende! Kodi Iye wachita

chiyani koma zabwino? Munthu wina anene izo!”

Ndipo mwamuna anamuwomba iye kuti achoke pamalopo, pafupifupi, ndipo anati, “Kodi inu mungamukhulupirire mkazi wopusa uyo, pamaso pa ansembe anu?”

Ndi zimenezotu. Mwaona? Kodi Iye anali atachita chiyani? Iye sanachite kanthu. Nchifukwa chiyani iwo anamupachika Iye? Chifukwa chiyani? Chifukwa chiyani? Chifukwa iwo sanali kumuzindikira Yemwe Iye anali. Ndicho chinthu chomwecho lero. Alaliki, ndi anthu a masiku ano, ndi aphunzitsi athu amakono, awaphunzitsa anthu chotero kuti azikhulupirira kuti Izi ndi “ufiti, kapena mdierekezi, kapena kuwerenga maganizo, kapena matsenga ena, kapena kuchenjera kwa mtundu wina,” mpaka anthu sakuzindikira kuti ndiko kutsimikizira kwa Mawu a Mulungu a tsiku lino. Ndi zizindikiro za tsiku-lotsiriza.

84 Mipingo, ngati iwe suli wa mu bungwe lawo, iwo amati, “Nha, chabwino, ndiko kudzipangitsa kwina. Ndi_ndi matsenga. Chabwino, tapenyani pansi apa kwa Akuti-ndi- akuti ndi Akuti-ndi-akuti.” Koma asiye iwo nthawi imodzi kuti adzatsimikizire Chinthu chenichenicho ngati al nga. U-nhu. Asiyeni iwo nthawi imodzi kuti adzatsimikizire kuti Izo ndi zolakwika. Iwo sangakhoze kuchita izo. Izo sizinayambe zadziwika kuti ndi zolakwika, ndipo Izo sizidzatero konse, chifukwa Izo ndi Mulungu. Mwaona? Koma iwo amakonda kuloza chala. Iwo amaganiza, “O, chabwino, ngati izo zikanakhala munthu wina ali ndi dzina lalikulu!” Chifukwa ndi gulu laling'ono, kagulu kakang'ono kokhala ngati kotaidwa kunja, “Chabwino, ife tinamukana munthu ameneyo ku mpingo wathu.” Mwaona? “Iwo, iwo ankakonda kumabwera ku gulu lathu, mwaona, koma iwo anapita ndi ili, ndipo iwo anapita ndi ilo, ndipo tsopano, inu mukuona, iwo akuthera^...Chabwino, penyani chimene icho chiri, yemwe iye ali.” Ine sindikusamala. Iwo akanakhoza kumanena chinthu chomwecho za Petro, Yakobo, ndi Yohane. Kapena, “Anthu osadziwa ndi osaphunzira,” iwo ankati. Koma iwo anachita kuzindikira, chinachake chinali chitachitika chiyambireni nthawi imeneyo. Iwo anakhala ali ndi Yesu. Icho ndi chomwe chinapangitsa kusiyana. Mwaona?

85 Iwo ankachita izo chifukwa iwo sankadziwa Yemwe Iye anali. Iwo sankadziwa kuti kutsimikizira kwa Mawu a Mulungu sikunali kuima mmwamba umo mu tsiku limenelo... Tsopano, izo zinali pa tsiku limodzi, ndipo uko kunali kulondola; izo zinali, pa tsiku limodzi, kuti azisunga malamulo amenewo ndi zinthuzo. Koma malamulo omwewo omwe anali, iwo anali akuwasunga, ankawalozera iwo ku nthawi yomwe pamene Iye akanadzabwera ndi kudzakhala Munthu uyu yemwe Iye ankayenera kukhala ali. Iwo anali nalo gawo ili, koma iwo sanatenge gawo linalo.

Ndipo ndi chinthu chomwecho chimene iwo akuchichita tsopano. Iwo ali nawo mpingo, ndipo iwo “amakhulupirira mwa Yesu Khristu,” ndipo iwo akuti amatero, ndi zina, koma amakana ora limene ife tikukhalamo! Akubweretsa panobe fanizo lakale kachiwiri: munthu nthawizonse amamuyamikira Mulungu chifukwa cha chimene Iye anachita, kuyang'anira mtsogolo ku chimene Iye akanati adzachite, ndi, kapena ati adzachite, ndipo nkumanyalanyaza chimene Iye akuchita, ndipo nkumaweruzidwa ndi icho. Mwaona? Iwo amaganiza, “Mulungu ndi wodabwitsa. Ndi wamkulu bwanji Iye! Chimene Iye ati adzachite: Iye adzabwera, ndipo kudzakhala Mkwatulo, tsiku lina, ndipo tidzapita Kwathu,” ndi kumakana zizindikiro zomwe ndi zodabwitsa pakali pano pa nthawi yomwe Lemba likunena kuti Iye adzakhala akuchita izo. Kuchiphonya Chinthu chonse! “Ngati wakhungu atsogolera wakhungu,” Yesu anati, “iwo onse adzagwera mu dzenje.” Ingopempherani Mulungu kuti atsegule maso athu mu masiku otsiriza ano. Chabwino.

86 Tsopano, mofanana, iwo akuchita mofanana lero. Iwo akumukana ndi kumupachika Mulungu yemweyo, lero, pa kusamudziwa Iye. Mofanana, pa kumukana Iye. Ndi kutero, pa kukana zinthu zimene iwo ali kuzichita lero, iwo sali kumupachika Khristu kachiwiri, chimodzimodzi, koma iwo akuchitira mwano Mzimu Woyera. Ndipo pa kuchita izo, iwo ali...Akuchitira chotani mwano Mzimu Woyera? Motani? Kodi iwo anawuchitira mwano Iwo chotani uko, kumbuyo uko? Bwanji, iwo sakanakhoza kuwuchitira mwano Iwo apo; Iwo unali usanabwere apobe. Iwo anamutcha Yesu, “Belezebule,” anamutcha Iye “Belezebule,” chifukwa Iye ankakhoza kudziwa zinsinsi za mitima yawo, ndi zinthu. Iwo anati, “Uyu ndi mdierekezi.” Mwa kuyankhula kwina, “Iye ndi wambwebwe. Ndi momwe Iye akuchitira izi, ndi mwa mbwebwe. Iye sali kanthu koma mdierekezi.” Mwaona, iwo anali asanakhale naye mneneri kwa zaka mazana anai, ndipo iwo anali atachokamo mu izo. Mwaona? Iwo anangokhala ndi malamulo awo. Iwo anati, “Uyu ndi Belezebule.”

87 Ndipo Yesu anati, “Ine ndikukhululukirani inu pa izo, koma pamene Mzimu Woyera ubwera,” onani, tsopano, “inu muyankhule liwu motsutsa Iwo, ndipo icho sichidzakhululukidwa konse kwa inu.” Kumbukirani, izo zidzatero, ndipo sizingakhoze, palibe njira iliyonse, palibe chifundo, pamene inu muchitira mwano, ndi kuwutcha Mzimu wa Mulungu, Mawu a Mulungu omwe akhala atatsimikiziridwa ndi Mzimu (Onani, Mawu amanena chomwecho, Mzimu umawatsimikizira Iwo,) ndipo inu mukatcha Iwo “chinthu chosayera,” inu mumadutsa mzere pakati pa chifundo ndi chiweruzo, ndipo simungakhoze konse kukhululukidwa pa izo. Ndicho chifukwa ine ndikuwutsutsa m'badwo uno, za kulakwa, kwa kumupachika, kumuchitira mwano Mwana wa Mulungu wowonetseredwa monga izo zinalonjezedwa ndi aneneri onse, ndi Khristu Iyemwini, kuti zidzakhala mu masiku otsiriza; monga izo zinali mu masiku a Nowa, mu masiku a Sodomu.

Kuchitira mwano, Chimene, iwo akupachikira, kwa anthu, Mwana wa Mulungu kachiwiri, Mawu Ake

otsimikiziridwa. Mawu amodzi kuwatsutsa Iwo sungakhoze kukhululukidwa konse. Tsopano kodi inu muchita chiyani ndiye? Inu muima pati? Iwo aweruzidwa, akungoyembekezera ora la mkwiyo wa Mulungu kuti utsanuliridwe. Iwo udzawaphwasula iwo.

88 Kukonda kachiphunzitso kazipembedzo zopangidwa ndi anthu, mbalume, bwinoko kuposa momwe iwo amachitira ndi Mawu a Mulungu otsimikiziridwira; m'badwo uno wa anthu. O! ine ndikungokhumba ine ndikadakhala nayo nthawi yaitali ya izi. Mwaona? M'badwo uno wa anthu, m'badwo uno ukukankha vumbulutso la Mulungu. Koma ife tikuyenda pamene atumwi anaponda. Ndiko kulondola.

"'Mulungu,' inu mukuti? Chabwino, ena amanena izo nawonso." Mulungu akutsimikizira Izi.

Yesu anati, "Ngati zintchito siziyankhula za Ine, ndiye ingopitirirani ndi kukanena kuti Ine ndikuzinena izo Inemwini. Koma ngati ntchito zikuyankhula, inu kulibwino mukhulupirire ntchitozo, mwaona, chifukwa ndi ora." Anati, "Inu mumadziwa kuti mawa dzuwa liwala, kapena kudzakhala nyengo yolunda; mu mlengalenga mwafiira ndipo mwatsika, mawa kudzakhala kwabwinoko." Anati, "Inu mungakhoze kuzindikira nkhope ya milengalenga; koma zizindikiro za nthawi, inu simukudziwa kanthu za izo. Ngati inu mukanamudziwa Mulungu, inu mukanalidziwa tsiku Langa."

Ndipo iwo anati, "Inu mukudzitengera mochuluka kwambiri pa Nokha; Inu mukudzipanga nokha Mulungu." Ndipo iwo anamuika Iye pa mtanda.

89 Ndipo Mzimu Woyera, lero, suli Munthu wachitatu ayi. Ndi Mulungu, Iyemwini, akuwonetseredwa mu thupi la umunthu, mwa Magazi a Yesu Khristu, kuti awuyeretse moyo kuti Iye akhoze kumadziwalitsira Iyemwini kupyoleramo. Ndipo iwo akuwapachika Mawu omwewo atawonetseredwa. Inu mukumvetsa? Kupachikidwa kwa Khristu, lero, ndi anthu omwe ati akane Mwana wa Mulungu wotsimikiziridwa ndi kuwonetseredwa pakati pa anthu, mwa Zake_zinthu Zake zomwe Iye anati zikanadzachitika mu tsiku lino mwa Mawu Ake. Mwaona?

Tsopano, kutsimikizira komweko, kunayenera kukhala kuli kofanana, ngati Iye ali Mwana wa Mulungu yemweyo, chifukwa Iye ananena mu Yohane Woyera 14:12, tsopano, kuti, "Zintchito zimene Ine ndikuzichita inu mudzazichita nanunso." Ahebri 13:8, "Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi nthawizonse." "Ngati inu mukhala mwa Ine," Yohane 15, "ngati inu mukhala mwa Ine, ndi mawu Anga akakhala mwa inu, ingopemphani chimene inu mukufuna ndipo icho chidzaperekedwa kwa inu." Inde, bwana!

90 Kumbukirani, iwo anali anthu achipembedzo kwambiri amene anachita izo. Iwo sanali achikunja. Iwo anali anthu achipembedzo a tsiku limenelo. Ndipo ndicho chimene chikuchita izo lero, ndi anthu achipembedzo; kupachikidwa komweko, chinthu chomwecho lero.

Mwamsanga. "Kumeneko iwo anamupachika Iye." Ndiye, ndiye? Zedi. Ndiye iwo anali akuwakana Mawu a Mulungu atawonetseredwa, kumavomereza tizikhulupiriro tawo mmalo mwa Mawu.

Kodi ndi zimene iwo akuzichita lero? Ndizo ndendende, akuchita zomwezo lero. Iye anali Mawu; ndipo iwo anawakana Mawu. Ndiyo nsonga imodzi yomwe ine ndikufuna kuti inu musaiphonye, onani, ine ndikufuna kuti inu musaiphonye. Iye anali Mawu, ndipo, pamene iwo anamukana Iye, iwo anawakana Mawu. Ndipo pamene iwo anachita kumukana Iye, iwo potsiriza anamupachika Iye. Ndipo ndicho chimene iwo achita lero: awakana Mawu a Mulungu, ndipo avomereza tizikhulupiriro tawo; ndipo amupachika, mwapoyera, pamaso pa osonkhana, kugwira ntchito kwa Mzimu Woyera. Ndipo iwo ali olakwa, ndipo ine ndikuwatsutsa iwo mu Dzina la Yesu Khristu.

91 Zaka khumi ndi zisanu ine ndamuwona Iye akuyenda kudutsa dziko, ndipo iwo akugwiritsabe ku zikhulupiriro zawo. Iwo ali olakwa! Iwo awatenga Mawu omwe akanati awubweretse mpingo, mipingo yonse palimodzi, ndi kupanga mgwirizano wawukulu waubale pakati pa Achipentekoste ndi ena onse a iwo; mmalo mwa kuchita chotero, iwo anawakana Iwo, ndipo awatembenuzira Iwo pansi, awanyoza Iwo, ndi kuwatcha Iwo chirichonse tsopano. Ndipo tsopano, mwa chitaganya cha mpingo, kupyolera mu dongosolo la mdierekezi, akuyesera kuti abwere mkati ndi kumati, "Tsopano ife tibwera, kudzagula Mafuta ena." Iwo akanidwa. Ndipo iwo ali olakwa pa kumupachika Yesu Khristu. Inu muzitenge izo mwa kanenedwe ka Mulungu, kapena kanenedwe kanu sikagwira ntchito. Mwaona?

92 Iwo anawakana Mawu a Mulungu atachita kuwonetseredwa, chifukwa cha tizikhulupiriro tawo, ndipo iwo akuchita zomwezo lero. "Iye anali Mawu," Yohane, Yohane Woyera 1. Ahebri 13:8 amati, "Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawi zonse."

Tsopano iwo akumupachika Iye mwatsopano. Kodi inu mumadziwa kuti Baibulo linati ife tikanakhoza kuchita izo? Ndi angati akanafuna kuti tiwerenge mochepa pang'ono pokha? Kodi inu mungandipatse ine maminiti ena khumi ndi asanu a izo? [Osonkhana, "Ameni."_Mkonzi.] Chabwino. Tiyeni titembenuzire uko tsopano, miniti yokha, "kumupachika mwatsopano." Tiyeni tipite ku Ahebri, mutu wa 6, ndi kuwerenga mochepa pang'ono pokha. Ahebri wa 6, ndipo tiwone ngati ife "tikumupachika Mwana wa Mulungu mwatsopano," tiwone ngati izo zingakhoze kuchitidwa. Inu mukuti, "Iwe sungakhoze kumupachika Iye nthawi yachiwiri." Ife tipeza ngati ife tingakhoze kapena ayi. Mawu a Mulungu ali owona. Ndi kulondola

uko? Ndi Ahebri 6:1.

Chotero posiya chiyambi cha chiphunzitso cha Khristu, tiyeni ife tipitirire ku ungwiro; osati ku kuika maziko a kulapa ndi ntchito zakufa, ndi za chikhulupiriro cha kwa Mulungu,

Ndi za chiphunzitso cha ubatizo,^kusanjika kwa manja, ndi za kuuka kwa akufa, ndi za chiweruzo chamuyaya.

...izi ife tizizichita, ngati Mulungu alola.

93 Taonani, Paulo akufuna kuti tidziwe kuti zinthu izi apa ziri mwamtheradi zofunika; maubatizo, kuikana kwa manja, chiwukitsiro, Kudza kwachiwiri. Zinthu zonse izi ziri Zamuyaya. Izo ziri mwamtheradi Choonadi. Tsopano zindikirani,!

"Pakuti ndi kosatheka..."

Werengani izo limodzi nane... ndime imodzi iyi. Ine ndikufuna inu kuti muiwerenge iyo limodzi nane tsopano, ndime ya 4.

Pakuti ndi kosatheka kwa iwo amene anawunikiridwapo kamodzi, ndipo analawa za mphatso yakumwamba, ndipo anapangidwa kukhala ogawana nawo za Mzimu Woyera.

Ndipo analawa za mawu abwino a Mulungu, ndi

mphamvu ya dziko liri kudza,

Ngati iwo ati agwere kumbali, kuti uwakonzenso iwo kachiwiri mwa kulapa; powona kuti iwo akudzipachikira kwa iwoeni Mwana wa Mulungu mwatsopano, ndi kumuika iye ku manyazi apoyera.

Kodi amenewo ndi mawu anga, kapena Ake? "Munthu yemwe amafika ku chidziwitso." Kumbukirani, iwo sanawamvetse Iwo. Iwo anali okhulupirira ammalire. "Titatha ife kulandira chidziwitso cha Mawu a Mulungu," inu mumachipeza icho kuchokera ku chidziwitso, kuchokera pa kuwerenga ndi kuwawona Iwo, "ndiyeno nkuwakana Iwo, ndiye, inu, ndi kosatheka kuti inu mudzapulumutsidwe konse." Kodi inu munaziwerenga izo tsopano? Mwaona, "Atalandira chidziwitso cha Choonadi," basi, inu mumvetse izo. Inu simunakhale nacho Icho.

94 Izo ziri monga okhulupirira aja amene anatuluka. Izo ziri choimira chomwe cha ulendo. Ichi, yachitatu iyi, eksodo yachitatu iyi, ili basi choimira cha yonse ya iyo.

Penyani! penyani mmbuyo uko. Ndiroleni ine ndikusonyezeni inu chinachake tsopano, miniti chabe. Khululukirani kuyankhulako. Penyani.

Israeli anatengamo anthu khumi ndi awiri, mmodzi kuchokera ku fuko lirilonse, mkulu wa chipembedzo, ndipo anawatengera iwo uko ku mphepete kwa malire, dziko lolonjezedwa, ndipo anawasonyeza iwo zinthu zabwino zomwe zinali kudza, zomwe iwo anali nazo. Ndipo iwo anabwererako, akudandaula, kuti, "Ife sitinali okhoza kuzichita izo." Koma apo panali awiri mwa khumi ndi awiriwo, Yoswa ndi Kalebu, anati iwo anayang'ana pa Mawu. "Mulungu anati ilo ndi lathu, ndipo ife tiri oposa kukhoza kuti tilitenge ilo." Ndi kulondola uko?

95 Kodi anali ndani awo? Okhulupirira ammalire. Mwaona, iwo anali ndithudi obadwira mu mpingo. Iwo anali atsogoleri a anthu. Iwo anali mabishopu, monga kuti unene, amene ankayenda kumene pansi mpaka komwe Mawu a Mulungu anali atasonyezeredwa kuti ali Choonadi. "Ilo ndi dzikolo!" Iwo anali asanafikeko uko. Iwo sankadziwa kuti ilo linali kumeneko. Koma iwo anabwera uko kuti adzawone kuti ilo linali kumeneko. "Ilo linali apo!" Ndipo Kalebu ndi Yoswa anapita kutsidya, ndipo anakabweretsako mulu wa nthuza ndi kuwalola iwo kuti adyeko zina za izo. Ndipo iwo analawa za dziko labwino, ndiyeno iwo anabwerera mmbuyo ndipo anati, "Ife sitingakhoze kuchita izo. Mwaona? Ife sitingakhoze basi kuchita izo."

Pano pali gulu lomwelo, mu nthawi ya Yesu Khristu. "Mphunzitsi, ife tikudziwa kuti Inu ndinu mphunzitsi wochokera kwa Mulungu." Mwaona? Mzere wammalire! "Ife tikudziwa kuti Inu ndinu mphunzitsi wochokera kwa Mulungu. Palibe munthu angakhoze kuchita zinthu zimene Inu mukuzichita. Ife tikuzindikira kuti Mulungu ayenera kukhala ali pamenepo." Nchifukwa chiyani iwo sanazilandire izo? Nchifukwa chiyani iwo sanazitenge izo? Mzere wammalire. Mzere wammalire.

96 Pano iwo ali pa eksodo wachitatu uyu; chizindikiro chomwecho, mawonetseredwe omwewo, Khristu yemweyo, Mzimu Woyera womwewo, ntchito zomwezo, Mulungu yemweyo, Uthenga womwewo, ndipo iwo sangakhoze kuwatenga Iwo. Iwo ayenera kuti apeze khadi lawo la chiyanjano. Ndi chiyani icho? "Iwo anali nacho chidziwitso cha Choonadi." Iwo anapenya ndipo anawona kuti ndizo mwamtheradi Choonadi. Iwo sangakhoze kuchikana Icho. Magazini anachita kuchitira umboni kuti iwo anachiwona Icho. Zithunzi, mapepala, umboni, chiwukitsiro cha akufa, kufotokoza kwa madokotala za odwala, iwo ayenera kunena

kuti ndi Iye. Ndi zoneneratu, popanda chimodzi cha izo chinayamba chalepherapo kupyola mu zakazi, chimodzi chirichonse cha izo ndendende basi pa dontho, iwo sangakhoze kunena zina koma kuti ndi Mulungu. Koma iwo sangakhoze kuzilandira Izo.

97 Gulu lija la atumiki mu Chicago, mazana atatu ndi chinachake a iwo, amati adzabwera kuti adzabatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu. Kodi iwo ali kuti? Mtengo wake ndi waukulu kwambiri. Iwo sangakhoze kuzichita izo. Ndi chiyani icho? Baibulo linati, pamene iwo achita izo, kodi iwo akuchita chiyani? Iwo akudzilekanitsa okha pakati pa chifundo ndi chiweruzo. "Pakuti ndi kosatheka kuti iwo amene anaunikiridwa kamodzi," akhala atabweretsedwa kuti ayang'ane pa Icho, "ndipo anali nacho chidziwitso cha Choonadi, ndipo analawa za Mawu abwino a Mulungu, ngati iwo abwerera kuchoka kwa Icho, kumene iwo akanati adzikonzenso okha kachiwiri, kuti, 'Chabwino, tsopano, ine nditero, inde!' "

98 Inu Achipresbateria, inu Amethodisti, ndi Abaptisti, ndi Achilutera, ndi gulu ili la Full Gospel Business Men, kumati iwo "akubwera mmenemo," anautembenuzira kumbali Uthenga. Mpingo wanu udzatero. Adzakhalapo anthu pawokha kumeneko, zedi. Koma, osati mpingo; inu muyenera kutuluka mu mpingo, kuti muchipeze Icho. Mwaona? Ndiko kulondola. Anthu pawokha ndi chabwino.

Koma pamene inu mukuganiza kuti mpingo wa Presbateria udzalandira Mzimu Woyera, ndipo onse a iwo adzataya zikalata zawo, ndipo, musati konse muziganiza zimenezo. Ndipo inu mukuganiza kuti inu Amethodisti mudzachita izo? Inu simudzachita konse izo. Kodi inu mukuganiza kuti inu Autatu mudzalandira konse Dzina la Yesu Khristu ndi kudzabatizidwa mmodzi aliyense wa inu mu^Inu simudzachita konse izo. Inu simudzachita konse izo. Koma anthu pawokha adzatulukamo ndi kudzachita izo, ndiko kulondola, ndipo ndicho chizindikiro cha Kudza Kwake. Koma mipingo imeneyo ndi amene awona Choonadi, ndipo achikana Icho mu makhonsolo awo, "ndi zosatheka."

99 Ndiye, iwo ali olakwa pa kumupachika Yesu Khristu. Ndipo ine ndikuwatsutsa iwo mwa Mawu a Mulungu, kuti Mulungu wa...

"Kodi inu mukuwatsutsa chotani iwo, M'bale Branham?" Ine ndikuwatsutsa iwo, kuti Mulungu wadzitsimikizira momveka Iyemwini mu Mawu Ake, mu masiku otsiriza, ndipo wadzipanga Iyemwini kuti adziwe kuti Iye akadali yemweyo dzulo, lero, ndi kwa nthawizonse, ndipo iwo mozizira atembenuzira Iwo pansi. Ndipo ndinu olakwa pa kumupachika Yesu Khristu, pa kuchitira mwano Mzimu Woyera. Ndiko kulondola.

Ife tikutengerani inu ku Ahebri 10, kachiwiri, kumene akutiuza ife kachiwiri mu Malemba, osati kokha pakukhala "zosatheka," koma inu simungakhoze konse. Izo zimakulekanitsani inu kwa Mulungu, Mwamuyaya. Inu simungakhoze konse kubwera mu Kukhalapo kwa Mulungu kachiwiri, pamene inu muutembenuzira pansi Mzimu Woyera ndi kuwuseka Iwo.

Tsopano, onani, "munalawa za Mawu." Mwaona, okhulupirira a mmalire! "O, inu mukuti anthu amenewo sanali okhulupirira?" Iwo anali okhulupirira, kapena odzitcha okhulupirira, koma pamene izo zinafika ku Mawu^Iwo anali Israeli. Iwo anatuluka pansi pa magazi. Iwo anatuluka pansi pa zizindikiro za Mose. Iwo anali atawona zizindikiro izo zikugwira ntchito.

Mulungu anati, "Ine ndidzakutengerani inu kutsidya."

Ndipo pamene izo zinafika mpaka ku mfundo ya Mawu olonjezedwa amene anali nkudza, kodi iwo anati chiyani? "O, ife sitingakhoze kuchita izo." Mwaona Ndipo apa iwo anabwerera, ali ndi nthuza ndi chirichonse, kuti atsimikizire kuti dzikolo linali labwino. Mawu a Mulungu ndi olondola.

Mulungu anati, "Ine ndikulipereka ilo kwa inu..." Koma zochitika,

"Maine," anati, "ife tikuwoneka ngati tiziwala, apo pambali pa iwo. Ife sitingakhoze kuchita izo, ziribe kanthu chiyani."

100 Zaka pang'ono zapitazo pamene nyumba yakale iyi inaima pano ngati kachisi, winawake anabwera umo, ndipo anayenda kunja uko ndipo anadzayankhula ndi ine, anati, "Billy, iwe uzidzalalikira kwa mizati inai, limodzi la masiku amenewa, ndi mauthenga onga amenewo."

Ine ndinati, "Ine ndidzakhala ndikulalikira kwa mizati inai, chifukwa Mulungu ali wokhoza mwa mizati imeneyo kuti adzutse ana kwa Abrahamu." Inde, bwana. Ndicho Choonadi. Ine ndinati, "Ngati iwe uli ndi chinachake chimene iwe ungakhoze kutsutsira Izo, tiye tikhale nacho icho." Kungokonda kukuwa, koma pamene zifika pamalo kuti asonyeze izo, ndi zosiyana. Inde, ndi chimene chimapangitsa kusiyana. Chabwino.

Eya, ndi tizikhulupiriro tawo iwo akumupachika Iye mwatsopano. Tsopano Ahebri mutu wa 6, ndipo ife tipitiriza mpaka pansi. Ndipo ife tikhoza kumangowerenga mopitiriza mpaka pansi, mpaka pansi umu kudutsa apa. Ife tiri nayo nthawi yochuluka. Ine ndinasonyeza Lemba pano pamene izo ziti zidzakhale, Ahebri mutu wa 6. Basi, ine ndikuganiza, titenge izo zonse. "Zosatheka kwa iwo amene anawunikiridwa

kamodzi, napangidwa kugawana nawo za Mzimu Woyera^" Ife tiribe nthawi kuti tipite patali kwambiri, chifukwa ine ndiri nalo Lemba lina limene ine ndikufuna kuti inu muliwerenge mu mphindi chabe.

Zindikirani izi, "Iwo akudzipachikira kwa iwoeni Mwana wa Mulungu mwatsopano." Kodi iwo anachita chiyani? Chiyani? Pa kukhala atalawa, ndi kuzindikira kuti Icho ndi Choonadi, ndiyeno nkutembenuka apo ndi kuchikana Icho. Kodi icho chinachita chiyani? "Ndi kosatheka..."

101 Kotero ndicho chimene fuko lino lachita. Ndi chimene anthu awa achita. Ndi chimene mipingo iyi yachita. Iwo achitembenuzira Icho pansi, ndipo iwo awupachika Uthenga. Iwo apachika Choonadi, kwa anthu. Kodi iwo anachita naye motani Yesu? Iwo anamuika Iye ku manyazi, anamuvula zovala Zake pa Iye, anamupachika Iye mmwamba pa mtanda ndipo anamukhomera Iye pamenepo, Kalonga wa Moyo. Chinthu chomwecho chimene iwo achita lero ndi tizikhulupiriro tawo! Iwo achita chinthu chofanana. Iwo anavula zinthu, iwo avula ubwino ndi zovala za Uthenga, pa kuyesa kuwuika Iwo penapake, ndi kumupachika Iye pa mtanda. O, maine! Chifukwa chiyani?

102 "Kumeneko iwo anamupachika... tsopano chobwereza chotsiriza, "Iye," Iye, Munthu wofunika kwambiri uyu. Nchifukwa chiyani iwo anachita izo? Iwo sanali kumudziwa Iye. Nchifukwa chiyani iwo akuchita izo lero? Iwo sakudziwa kuti ichi ndi Choonadi. Iwo ndi osayankhula ndi akhungu kwa Icho. Iwo sakuchidziwa Icho. Ndicho chifukwa. Tizikhulupiriro tawo ndi miyambo zawatengera iwo kutali kuchoka ku Mawu a Mulungu.

Tsopano kwa inu pano, basi pa kutseka tsopano, perekani tcheru kwambiri. Mwaona? Ine ndikudziwa kuti kwatentha. Ine ndatenthedwa, inenso. Koma, o, m'bale, Mawu awa ndi Moyo ngati inu muti mugwiritse kwa Iwo. Penyani, si chinachake chimene ife timachikamba, chimene chikhoza kuchitika pano ndi mtsogolo; Ndi chinachake chimene chiri kale pano ndi ife ndipo chikuchitika tsopano. Osati chinachake chiti chidzakhale; chinachake chimene chiri kale. Ife sitiri kuchitira umboni, "Ife tikudziwa chimene Iye wachichita; ife tikudziwa chimene Iye ati adzachite," koma tsopano ife tikunena zomwe Iye akuchita. Mwaona, lino ndi ora lathu. Ife mwina sitingakhale moyo kuti tiwone Mkwatulo. Ine ndikhoza kufa lero; inu mukhoza kufa lero. Ine sindikudziwa. Koma Mkwatulo ukudza. Ndicho pamene iwo ubwera, ife tidzakhala kumeneko, musati mudandaule; u-nhu, chomwechonso adzatero onse a iwo mmbuyo kupyola mu mibadwo, amene anaukhulupirira iwo ndi kuyang'anira iwo. Iwo ankayenda mu Kuwala kwa tsiku lawo. Ndipo pano pali Kuwala, Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Tayani tizikhulupiriro tanu ndipo khulupirirani Mawu awa. Ichi ndicho Choonadi. Mawu ndiwo Choonadi. Yesu anati, "Mawu Anga ali Mzimu, Mawu Anga ali Moyo." Inu muulandira chotani Moyo pamene inu mukuwukana Moyo? Inu mutenga bwanji mbalume, imene ili imfa, ndi Mawu a Moyo? Kutulutsa Mawu a Moyo, kuti mutenge imfa, inu mulandira chotani ziwirizo pa nthawi yomweyo? Inu simungakhoze kuchita izo. "Lolani mawu a munthu aliyense akhale bodza, mbalume iliyonse bodza." Mawu a Mulungu ndiwo Choonadi.

103 Ine ndikutsutsa munthu aliyense kuti andisonyeze ine(Ndipo ine ndikudziwa tepi iyi ikupita kuzungulira dziko lapansi) Munthu aliyense, bishopu aliyense, yemwe angati abwere komwe ine ndimawerengera, kapena patsogolo pa gulu ili, ndi kuloza chala chawo pa malo amodzi aliyense anayamba wabatizidwapo mu Dzina la "Atate, Mwana, Mzimu Woyera," mu Chipangano Chatsopano. Ine ndikusonyezani inu pamene munthu aliyense anayamba wabatizidwapo...Ndipo iwo amene anabatizidwa mosiyana, anachita kubwera ndi kudzabatizidwanso, kuti alandire Mzimu Woyera. Kodi inu muchita chiyani nazo izo? Mukhala kunja uko mu tizikhulupiriro tanu? Mukhala kunja uko mu mbalume zanu ndi kufa? Ndinu olakwa! Ndi manja oipa, inu mwamutenga Kalonga wa Moyo, Mawu a Moyo, ndipo mwawapachikira Iwo kwa anthu.

104 Tsopano kodi iwo anachita chiyani? Iwo sanali kuchidziwa icho. Lero amuna akumayenda mwaumbuli. Iwo sakudziwa kuti ndicho Choonadi. Iwo akuganiza kuti ndi mtundu wina wa zongoyambitsa. Iwo samakumba mozama kokwanira kuti alowe mu Mzimu wa vumbulutso. Iwo samapemphera mokwanira. Iwo samaitana pa Mulungu mokwanira. Iwo amangochitenga Icho mopepusa, "O, chabwino, ine ndikukhulupirira kuli Mulungu. Zedi!" Mdierekezi amakhulupirira chinthu chomwecho. Mdierekezi amakhulupirira izo moposa anthu ena amanenera kuti akukhulupirira izo. Mdierekezi amakhulupirira izo ndipo amanjenjemera. Anthu amangokhulupirira ndi kumapitirira. Koma mdierekezi amanjenjemera, podziwa kuti Chiweruzo chake chikudza, ndipo anthu amakhulupirira izo ndipo samapereka tcheru kuti Chiweruzo chikudza.

Olakwa pa kumupachika Iye! Zedi! Ine ndikuwutsutsa m'badwo uno, ndikuwapeza iwo olakwa, mwa Mawu omwewo amene iwo anawapeza olakwa pa chiyambi. Ndiko kulondola. Yesu anati, "Ndani angakhoze kunditsutsa Ine?" Iye anali Mawu atapangidwa thupi. Ndipo lero Mawu omwewo apangidwa thupi.

105 Petro ananena mu chitsutso chake, mu Machitidwe. Tiyeni tingowerenga izo. Petro, pamene iye anawona izi zikuchitika, zimene iwo anali atachita, Mzimu...Penyani, Petro anali kumuteteza Khristu, zomwe iwo anali atachita. Ine ndikuteteza zomwe Mauthenga ali. Petro anali kuwatsutsa iwo pa

kumupha Munthu, Khristu, Yemwe anali Mawu. Ine ndikuwutsutsa m'badwo uno chifukwa choyesa kuti uwaphe Mawu omwe apangidwa kuwonetseredwa mwa anthu. Penyani chimene Petro ananena. Mkwiyo Wake wa chirungamo uyenera kuti unakwera pamwamba ndithu. Mvetserani pa iye apa mu Machitidwe mutu wa 2, ndipo kuyambira ndi ndime ya 22.

Inu amuna a Israeli, mverani mawu awa; Yesu waku Nazareti, wotsimikiziridwa, mwamuna wotsimikiziridwa ndi Mulungu pakati pa inu ndi zozizwitsa....zizindikiro, zimene Mulungu anazichita mwa iye pakati monga...za inu, monga inu eniake nanunso mukudziwa:

Fyuu! Taganizani momwe iwo anamverera! Mvetserani kwa izo.

Inu amuna a Israeli, kalonga, inu anthu a mpingo, inu anthu opatulika, inu ansembe, inu amuna amene mukuyenera kukhala muli amuna a Mulungu, imvani mawu awa; Yesu waku Nazareti anatsimikiziridwa ndi Mulungu pakati pa inu.

106 Tsopano ine ndikunena kwa inu azibusa, ndi kwa inu anthu. Yesu waku Nazareti, Mzimu Woyera, Iye ali pano mwa Umunthu wa Mzimu Woyera, yemwe anali Moyo umene unali mwa Iye. Iye ali pano akugwira ntchito kupyolera mwa anthu, ndi kudzifotokozera Iyeyekha mwa zizindikiro ndi zodabwitsa zimene Iye amachita. Ndipo pano izo zapachikidwa pa makoma, chizindikiritso chamwasayansi. Ndipo anthu akhala pano, omwe anali akufa, ali amoyo lero; ndipo odyedwa ndi khansara, ali bwino lero; akhungu, akupenya lero; ndi olumala, amene akuyenda lero. Iye ndi Yesu waku Nazareti.

Iye, pokhala ataperekedwa ndi uphungu wotsimikiza ndi kudziwiratu kwa Mulungu, okonzedweratu ku ntchito Yake, inu mwamutenga iye, ndipo ndi manja oipa inu...mwamupha:

107 Kodi icho ndi chitsutso? Iye akutsutsa chiyani? Khonsolo la Sanhedrin lija. Ndipo ine ndikutsutsa, mmawa uno, chitaganya cha mipingo. Ine ndikuwatsutsa Achipentekoste. Ine ndikuwatsutsa a Chipresbateria, Abaptisti, ndi chipembedzo chirichonse mu dziko. Mwa uthakati, kudzikonda, umbombo inu mwawatenga Mawu a Moyo ndi kuwapachika Iwo pamaso pa anthu, ndi kuchitira mwano Iwo, ndi kuwatcha Iwo "zotentheka," chomwe Mulungu wawutsa pakati pathu kuti akatsimikizire kuti Iye ali yemweyo, lero, ndi kwanthawizonse. Ine ndikuwutsutsa m'badwo uno!

108 Mulungu wadzitsimikizira Yekha wamoyo. Mulungu watsimikizira kuti awa ndi Mawu Ake. Inu muli ndi chiyani koma mulu wa mbalume ndi tizikhulupiriro! Ndi pati pamene inu mungasonyeze Mulungu wamoyo? Chifukwa inu mwawatembenuzira Mawu a Moyo omwe akanati akupatseni inu chinthu ichi. Inde, bwana! O, ndi ora lanji limene ife tikukhalamo tsopano. Fyuu! Zofanana...

O, ine ndikuitana....Petro anati "inu munamutenga, ndi manja oipa ndipo mwamupachika ndi kumupha:

Yemwe Mulungu...anamuwukitsa, atamasula zowawa za imfa: chifukwa sikunali kotheka kuti iye akhale atagwidwa ndi izo.

Ndipo kupyolera mu tizikhulupiriro tanu, ndi mabungwe anu, ndi zipembedzo zanu, ndi maonekedwe anu aumulungu, akadayankhulabe. Maonekedwe anu aumulungu, inu mwakana mphamvu ya chiwukitsiro Chake. Koma ora lafika, masiku otsiriza ali pano, pamene Mulungu analonjeza, malingana ndi Malaki 4, kuti Iye akanadzamudzutsa mu masiku otsiriza, "ndipo akanati adzatembenuze mitima ya anthu kubwerera ku madalitso apachiyambi ndi Chikhulupiriro cha chipentekoste cha makolo." Ndipo inu simungakhoze kuzikana izo, ndipo inu simungakhoze kuima motsutsana nazo izo. Ndipo tsopano ine ndikukuweruzani inu, olakwa, ndipo ndikuchita makani nanu, ndipo ine ndikukutsutsani inu pamaso pa Mulungu, kuti ndi manja authakati, odzikonda, achipembedzo inu mwawapachika Mawu a Mulungu pamaso pa anthu. Ndipo ine ndikukutchani inu olakwa ndi okonzekera ku Chiweruzo. Ameni. Inde, bwana!

Ine ndikutcha chinthu chomwecho chimene Petro anachita. Iye anaitanira kulapa kwa m'badwo umenewo. Ine ndikuitanira kulapa kwa m'badwo uno, kulapa kwa Mulungu, ndi kubwerera ku Choonadi chapachiyambi cha Mawu. Kubwerera ku Chikhulupiriro cha makolo athu. Kubwerera ku Mzimu Woyera, chifukwa Mulungu sangakhoze kusintha Izo. Pamene Mulungu anati, "Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira," Iye ayenera kukhala ndi izo monse kupyola mu Muyaya. Ndi Mawu Ake.

109 Pamene inu mukuti, "Gwirani chanza, kapena idyani mgonero," kapena chinachake monga icho, kapena china pa kachikhulupiriro ako, kapena chinachake pa lingaliro ilo; kuti munthu aliyense, chidakhwa chirichonse, wosakhulupirira aliyense akhoza kuchita izo. Wotsanzira aliyense, wachiwerewere aliyense akhoza kuchita izo. Kutenga mgonero, kukhala nawo maonekedwe ndi zinthu monga izo, inu mukhoza kuchita izo. Koma Yesu anati ichi chidzakhala chizindikiritso, "Zizindikiro izi zidza," osati izo zikhoza kutero, "izo zitero, mu mibadwo yonse, kwa iwo amene akhulupirira! Mu Dzina Langa iwo adzatulutsa ziwanda; iwo adzayankhula ndi malirime ena, adzayankhula ndi malirime atsopano; ndipo adzatenga njoka; kumwa zinthu zakupha, izo sizidzawapweteka iwo; adzaika manja awo pa odwala, iwo adzachira." "Adzachiritsa odwala, adzawukitsa akufa, adzatulutsa ziwanda; monga mwalandira mwaulere, perekani mwaulere."

Njira zazikulu zonse izi zopangira ndalama ndi zinthu, ndi kulumikizidwa ku zinthu lero, palibe zodabwitsa iwo ali odzaza chiweruzo. Inde, bwana! O, maine!

110 Tiyeni tiwone tsopano. Inde, bwana. Kuitanira ku kulapa, ndipo chitsutso changa tsopano. Gologota watsopano uyu ali_mpingo, wotchedwa- choncho, malo opatulika kwambiri, maguwa aakulu, guwa la Chikatolika, guwa la Katolika, zotchedwa guwa lawo. Amethodisti, Abaptisti, Apresbateria, Achilutera, Achipentekoste, malo opatulika kwambiri, kumeneko Iye akulandira kulasidwa Kwake kolimba. Gologota watsopano! Kodi iye akupezeka kuti? Mu malo opatulika kwambiri, mpingo. Kodi Iye akupachikidwa kuti? Kuchokera kwa azibusa. Inu achinyengo, inu mukudziwa bwino kuposa izo! Ine sindiri wokwiya, koma chinachake mkati mwa ine chikukondoweza. Mulungu watsimikiziridwa bwinobwino pakati pa inu.

Kodi Iye anazilandira kuti nthungo Zake, mu mbali Mwake? Kodi Iye anakupeza kuti kulasidwa Kwake? Pa Gologota. Kodi Iye akukupeza kuti iko lero? Mu guwa. Kodi iko kunachokera kuti? Yerusalemu. Kodi iko kukuchokera kuti? Chipembedzo. Iwo omwe akuti amamukonda Iye, ndi omwe anachita izo. Ndi omwe akuchita izo lero. Gologota Wake wachiwiri, kumene Iye akulandira kulasidwa Kwake motsutsa Mawu, ndi zomwe zikumubaya Iye. Kodi Iye ndi ndani? Iye ndi Mawu. Iye ndi Mawu. Kodi Iye akubaidwa kuti zolimba? Ku guwa mu malo opatulika, basi monga izo zinali pamenepo.

111 Ine ndiri nawo ufulu kuti ndiwutsutse m'badwo uno. Ine ndiri nawo ufulu kuti ndichite izi, monga mtumiki wa Uthenga wa Yesu Khristu, ndi zizindikiro Zake, ndi kutsimikizira kuti Iye ndi Mulungu. Ine ndiri nawo ufulu kuti ndibweretse chitsutso kwa m'badwo uno. Chifukwa, nsonga zolimbitsitsa za nthungo Zake zakhala ziri kuchokera pa maguwa pomwe, kumene iwo akutsutsa ndi kumati, "Musati mupite kuti mukamvere zinthu izo. Izo ndi za mdierekezi." Mmalo momwe mmene iwo akuyenera azimukonda Iye!

Ndipo zizindikiro zomwe zimene Yesu anati zikanati zidzachitike, "Mawu a Mulungu ali akuthwa koposa lupanga lakuthwa konsekonse; Mawu, ozindikira maganizo, a zolinga za mtima." Ndipo Iwo akutchedwa mdierekezi, kuchokera kuti? Maguwa, malo opatulika. O, Mulungu, Iye angakhoze bwanji kuyang'ana pansi? chifundo chokha, ndizo zonse, chisomo. Ife sitingakhoze kuchita kalikonse koma kulunjika ku chiweruzo. Ife tiri kale kumeneko.

112 Taganizani za izo. Kulasa Kwake kolimbikitsitsa kukuchokera mu guwa. Ndiko kumene Gologota Wake watsopano ali. Iwo akumupachika Iye, Mawu, pa guwa. Ndiko kulondola. Motani, kodi iwo anachita motani izo? Mwa maonekedwe awo aumulungu. Ndizo ndendende!

Kuvekedwa nduwira kuchokera kwa omvetsera, ndi otonza! Iye ali nayo nduwira yatsopano ya minga, otonza! Akupyozedwa kuchokera mu guwa; kuvekedwa nduwira ndi otonza. Kodi Iye akupachikidwa panonso, mwatsopano? Kukwapulidwa ndi tizikhulupiriro topangidwa ndi anthu, aphunzitsi a chipembedzo motsutsa Mawu Ake. Iwo akuwukwapula Iwo, mwa manyazi, kuwatsutsa Iwo.

Yesu anati, "Mwa chabe iwo akundipembedza Ine." Mwa chabe, "sizikuchita ubwino ayi." Kodi iwo akumupembedza ndani? Iwo akumupembedza Mulungu yemweyo. Iwo anali kumupembedza Mulungu yemweyo pa kupachikidwa Kwake koyamba, ndipo iko kunali kupembedza kwachabe. Ndi chinthu chofanana lero. Mwa chabe iwo akumanga zipembedzo izi. Mwa chabe iwo akumanga maseminare awa. Mwachabe iwo ali ndi tizikhulupiriro iti, kuphunzitsa ngati chiphunzitso malamulo a anthu, ndi kumakana Mawu a Mulungu. Iwo ali olakwa pa kumupachika Kalonga wa Moyo, kuphunzitsa tiziphunzitso ta anthu mmalo mwa Mawu Ake. "Mwa chabe iwo akundipembedza Ine,"... kukwapulidwa, kupyozedwa, kuvekedwa chisoti cha minga.

113 Pamene inu muwaona iwo akupita pansi mu msewu, ndi ena a inu madona muli ndi tsitsi lalitali; kumati, "Iye ndi wakachitidwe kachikale, sichoncho iye?" Kumbukirani, ndiwo otonza, ndicho chipewa chaminga chimene inu mukuvala. Mulungu anati iwo unali ulemerero wanu; muziuvala iwo ndi kunyadira. Aleluya! Muzilivala ilo ndi kunyadira, monga inu mukanavalira nduwira ya minga mmalo mwa Ambuye wanu. Muzilivala ilo ndi kunyadira. Musati muzichita manyazi. Iye ananena chomwecho, ziribe kanthu zomwe Mayezebeli awa akunena lero. Zomwe onamizira awa omwe amaima mu guwa, omupachika Khristu, ziribe kanthu zimene iwo akunena, inu muzilivala ilo ndi kunyadira. Mulungu ananena chomwecho. Inu muzilisunga ilo.

Kuvekedwa nduwira, ndi onyoza kachiwiri, minga. Akupyozedwa kuchokera kuguwa, ndi tizikhulupiriro.

Iye ali naye Gologota watsopano, kumene iwo akumutengerako Iye: makwayara amikanjo awa, akazi ovala zazifupi, atsitsi lodula, ankhope zolochedwa, akuimba mu kwayara ngati Angelo, ndi maluso. Ndiye Gologota Wake watsopano, basi odzivula modolola amakono otetezedwa ndi lamulo, monga ku Sodomu ndi Gomora.

114 Inu mumawona garu wamng'ono wamkazi akuyenda pansi mu msewu. Pa nthawi zina sipamakhala garu wamwamuna yemwe angati apite kumene wamkaziyo ali. Mungolola chinthu china kuti chichitike, ndipo mmodzi wa aliyense wa iwo amathamangira pambuyo pake. Pali chinachake chachitika kwa iye. Inu mukudziwa chifukwa chake. Nchiyani chimene akazi awa amachotsera zovala zawo, ndi kumapita pansi

mu msewu? Musati mundiuze ine kuti si chiri chinthu chomwecho. Ndicho chizindikiritso. Musati mumuweruze mwamunayo. Koma iwo ali otetezedwa ndi lamulo la Sodomu. Lamulo limenelo linayenera kunena kuti nkosaloledwa kuti iwo azikhala ali kunja uko. Ndipo alaliki mu guwa anayenera kumakhala ndi mapitikoti mmalo mwa chikhotho chaubusa; ataima kunja uko ndi kumaloleza izo, ndi kumachita manyazi kuti ayankhule motsutsa izo, chifukwa chipembedzo chawo chiwatulutsa iwo. Inu mukumupachikira, kwa osonkhana, Mawu a Mulungu amene amati, "Ndi themberero kuti mkazi azivala chovala choyenera kwa mwamuna."

Ine ndikuweruza chinthucho. Ine_ine_ine_ine_ine_ ine ndikuyimba mulandu iwo wa kupachika Mawu a Mulungu pamaso pa anthu. Akazi odula tsitsi, ovala zazifupi mu gulu, kumaimirira mu kwayara!

115 Wina wake ananena kwa ine, tsiku lina, mkazi wina anandifunsa ine, anati, "Chabwino, kodi inu mukuganiza kuti mungakawapeze kuti?"

Ine ndinati, "Ngati Ambuye akanandifunsa ine kuti ndipeze khumi ndi awiri kuchokera, pa dziko, ine ndikanachita mantha ngati ndife." Pamene, mwa kuzindikira zinthu mwa Uzimu, ndikaima pamenepo ndi kumawayang'ana iwo, ndi kuima monga choncho ndi kumawona zinthu izo pa iwo; auve, anyansi, otsika-pansi, okhwewa-ndudu, kunja uko akupitirira kuchita monga choncho, ndi kuima mu kwayara yamiinjiro ndi kuimaimba mu chikhalidwe chimenecho, ndi kuwalola omvetsera kuti aziwaona iwo. Iwo nkumati, "Chabwino, ngati uyo angakhoze kuchita izo, ine ndikhoza nanenso."

Moyo wa Chikhristu ndi moyo wachiyero ndi ungwiro, wosalakwa!

Ine ndikuwatsutsa iwo, mu Dzina la Yesu Khristu, chifukwa cha uve wawo ndi nyansi. Iwo abweretsa Uthenga ku chochititsa manyazi. Ndipo iwo amene amayesa kuti awugwiritse Iwo, amatchedwa "otentheka," kumazitcha, "Izo zachikale zamkutu." Ine ndikuwatsutsa iwo, mu Dzina la Yesu Khristu.

116 Ozivula pa msewu amakono basi, akuimba mu makwayara, osuta-ndudu, omanena nthabwala zonyansa, amuna atatu kapena anai, ndipo akakhala ndi wachisanu ndi chimodzi, ndiyeno nkumaimba mu kwayara chifukwa iwo ali ndi liwu. Inu osauka aluntha, operewedwa mwauzimu, okanidwa pa zifukwa zanu zomwe. Inu mumawerenga Baibulo lomweli limene munthu wina aliyense akhoza kuliwerenga, koma inu mwawukana Mzimu wa Mulungu, mpaka Baibulo linati inu mudza "perekedwa ku zosokoneza zamphamvu, kuti mukhulupirire bodza ndi kulangidwa nalo." Inu ndithudi mukukhulupirira kuti inuyo mukulondola, ndipo Baibulo limati inu mudzakhulupirira izo ndi kulangidwa ndi bodza lomwelo limene inu mumalikhulupirira kuti linali Choonadi. Chotero, ine ndikukutsutsani inu ndi Mawu a Mulungu. Inu mukuwaphunzitsa anthu cholakwika, ndipo mukupachika mfundo za Khristu, za chiyero ndi Moyo mmwamba.

Munthu azikhoza kumayenda kunja pa msewu ndi kukhala munthu wosiyana.

117 Alaliki kumaima pa bwalo la mpira, akusuta ndudu; miyala yopunthwitsa; zovunda zammimba zonse zimene iwo amachita nazo. Akazi mu kwayara yawo, atavala zazifupi, tsitsi lodula, ndi kumachita mopitiriza monga choncho, nkhope zopaka utoto, ndiyeno nkuzitcha izo, "Mlongo, uyu ndi uyo," ndipo Baibulo limatsutsa zinthu zimenezo. Ndiko kulondola. Kupita ku maphwando ndi kumachita mopitiriza, nkukhalabe membala wa mpingo; kusungabe umboni wanu, ndi kumakhala moyo mulimonse momwe inu mukufunira kutero.

Musati muganize kuti ine ndikuyankhula pazonsezi za Apresbateria. Ine ndikuyankhula za inu Achipentekoste. Ndiko kulondola. Inu nthawiyina munadziwa Choonadi, koma ine munkaganiza kuti inu simukanakhoza kuchitenga Icho. Inu simumakhoza kumuthandizira m'busa wanu. M'busa wanu_ wanu samakhoza kukhala pa ntchito yaikulu ya madola mazana ochuluka chotero pa sabata, ndi mpingo wabwino waukulu woti azilalikiramo, ndi kumakwera galimoto ndi kumachita mopitiriza momwe iwo akuchitira. Ngati iye atatsutsa izo, bungwe lingamuponye iye kunja; kotero iye ayenera kuzisunga izo, iye ayenera kumanena izo. Chotero, iye anagulitsa maufulu obadwa nawo ake, chifukwa cha nyansi za chipere cha dziko, cha kusasamala kwa Esau. Ndipo kodi iye apeza chiyani chifukwa cha izo? Onsewo agwera mu dzenje la kuweruzidwa, ndi kukhala oweruzidwa. Ine ndikuwatsutsa iwo, monga achiwerewere a Uthenga.

118 Ine ndinali ku kwayara, amodzi mwa malo otchuka, aakulu, osati kale litali, ena mwa malo apamwamba a Chipentekoste amene alipo. Ndipo ine ndinapezeka nditakhala mowerengera mwa m'bale ameneyu mmene makwayara anai kapena asanu anabwera pamodzi. Ndipo ndi amodzi a^ limodzi la mabungwe abwino kwambiri a Chipentekoste. Ndipo iwo sankadziwa kuti ine ndinali mowerengera mwa mtumiki uyu, ku Oklahoma. Ine ndinakhala pansi kumeneko, pansipo, kumene mtumiki uyu amawerengera asanati abwere ku nsanja yake. Ndipo pamene ine ndinatero...Uko kunali ma Rickie aang'ono awo kunja uko; ndi ma Ricketta, utoto, popanda mmodzi wa iwo amene anali ndi tsitsi lalitali, mmodzi aliyense wa iwo anali ndi tsitsi lodula, mmodzi aliyense wa iwo anali ndi zopakapaka, mmodzi aliyense wa iwo atavala mikanjo. Ndipo Ricky wamng'ono ataima cha pamenepo, akupitapita pamenepo monga choncho, (ndipo bambo wina anali akutenga chopereka cha mishonare), iye ankachita monga iye anali munthu wakhungu

ali ndi chipewa, ndipo akupita mozungulira akunena mtundu wonse wa zinthu zochitira mwano zokhudza kutenga chopereka, ndi zinthu monga choncho. Koma anapita kunja uko nakayesa kuti aimbe “Mesiya”, O, maine, ndipo amakhoza kuchita ntchito yabwino pa izo, koma izo zinalibe kamvekedwe. Ayi, izo zinali zakufa, mwaona. O, maine! Ndi inu pamenepo. Ndiye Gologota Wake watsopano.

119 Inu mukuganiza chiyani za msungwana wina wamng'ono, kapena mkazi wina wamng'ono kumeneko? Bwanji, ngati iye akanati abwere mmenemo, atavala monga iye anayenera kuvalira, ali ndi tsitsi lalitali, ndipo utoto wonse utachotsedwa, ndi zinthu monga choncho, iwo akanamamuseka iye; ngati iye akanati aimirire, ndipo pamene iwo anali kupanga izo-zochita pamenepo, gulu lija la anthu aang'ono, pafupi makumi atatu kapena makumi anai a iwo. Gawo losankhidwa la Chipentekoste, ndi kumachita zinthu monga choncho! Ndipo ngati dona wamng'onoyo akanati anene chinachake chokhudza izo, iwo akanamuchotsa iye mu kwayara. Mulole mlaliki wa Uthenga aime mu guwa ndi kunena chinachake chokhudza izo, iwo akhoza kumuchotsa iye mu bungwe. Inu mukupachika Mwana wa Mulungu kachiwiri, ndipo mukumuika Iye ku manyazi apoyera. Uthenga Wake umene inu mukuti mukuulalikira, inu mukumupachika Iye. Ine ndikuwutsutsa m'badwo uno wokana-Khristu, mwa Mawu a Mulungu, ndi mwa mphamvu Zake za chitsimikiziro cha masiku otsiriza ano kuti Iye akanali wamoyo.

Inde. Iwo akutsutsana ndi Mawu a Mulungu odulidwa bwino, otsimikiziridwa. Mabungwe awo sangakhoze kuima kwa Iwo.

120 Mipingo yaikulu ndi zipembedzo ndizo Gologota Wake watsopano. Ine ndinena izo kachiwiri. Izi, kudzivula kodolola kwamakono kwaoku, ndiwo makwayara awo. Wansembe wamkulu wa chipembedzo chirichonse akufuula monga wansembe wamkulu wa tsiku limenelo, “Tsopano bwerani pansi ndi kudzatisonyeza ife chozizwitsa.” Kumeneko kunali kupachikidwa koyamba. Ndi zofanana lero. Ine ndinakhalapo nawo iwo akuti, “Chabwino, tsopano, inu mumawukitsa akufa, sichoncho inu? Bwanji inu simukupita kumtunda uko? Iwe uli ndi mkazako kumandako. Iwe uli ndi mwana kumtunda uko.”

Iwo anati kwa Iye, “Ife tinamva kuti Inu mumawukitsa akufa. Ife tiri nawo manda odzaza kumtunda kuno. Bwerani mudzawadzutse iwo.” O, umbuli udzabala umbuli.

Mipingo yaikulu, makwayara aakulu, ansembe aakulu a tsiku lino, “Tsikani pansi, tisonyezeni ife chozizwitsa chimene chipembedzo chathu sichingakhoze kuchichita.”

121 Ine ndinali ndi munthu, osati kale litali, yemwe anapanga ndemanga pa^atatha kuwulutsa kwapang'ono kumene ine ndinali nako mu Jonesboro, Arkansas, ndikunena za mkazi wina yemwe anali atachiritsidwa. Munthu uyu anali wa chipembedzo china cha mpingo, ndipo iye anaimirira kuseri uko ndipo anati, “Ine ndikuchita makani kwa munthu aliyense kuti andibweretsere ine ndi kundisonyeza ine chozizwitsa.” Ine ndinapita ndipo ndinakamutenga dokotala. Mwamuna anali atachiritsidwa, ndi khansara. Ine ndinapita ndipo ndinakamutenga mkazi yemwe anakhala ali mu chikuku kwa pafupi zaka makumi awiri; iye anachiritsidwa ku nyamakazi, anakhala ali mu chikuku. Ine ndinatenga izo zonse ndipo ndinati, “Tsopano ine ndikufuna ndalama, madolla chikwi.”

Iye anati, “Chabwino, ha, ha, ha, ha, izo siziri kuno. Izo ziri komwe ku Waco, Texas, komwe likulu lathu liri.”

122 Ine ndinati, “Chabwino, ife tingopita kumeneko ndi kukazitenga izo.” Anati, ine ndinati, “Inu mupange kukonzekera ndipo ife tipitako mawa.” Mwaona? Ine ndinati, “Ife titumiza^” Ine ndinati, “Pano pali dokotala woti anene kuti anthu awa mwamtheradi anali ndi khansara. Pano izo ziripo pa mndandanda, kujambula kwamagetsi. Pano pali mkazi uyu yemwe oyandikana nawo onse akudziwa kuti ankakhala mu chikuku chimenecho kwa zaka makumi awiri, ndipo iye akuyenda pakali pano. Ndipo madokotala, pakhala pali dokotala pambuyo pa dokotala pambuyo pa dokotala, ndi chirichonse, ndipo pano iye ali wamoyo lero. Tsopano, inu munati inu 'mupereka madola chikwi.' Ine ndikuzifuna kuti ndikaziyike izo mu thumba la umishonare. Ine ndikuzifuna izo.”

Iye anati, “Chabwino, izo ziri komwe ku Waco, Texas.” Ine ndinati, “Ife tipitako mawa.”

Iye anati, “Dikirani miniti. Ndiroleni ine ndikuuzeni inu chinachake. Ine ndimutenga msungwana wamng'ono ndi ine. Ndipo mukandirole ine nditenge lumo ndi kudula mkono wake, ndiyeno inu mukamuchiritse iye, pamaso pa abale athu. Ndipo iwo akakupatsani inu ndalamazo.”

Ine ndinati, “Iwe mdierekezi!”

“Ngati Iwe uli Mwana wa Mulungu, tsika pa mtanda uwu.” “Tiuze ife yemwe wakumenya Iwe,” ali ndi kasanza mozunguza pa mutu Wake. Anamumenya Iye pa iwo, nati, “Tsopano, ngati Ndiwe mneneri, tiuze ife ndani....

“Ngati Iwe uli Mwana wa Mulungu, tsika pa mtandapo.”

Atsogoleri akhungu kwa akhungu! Iwo akusowa kuchizidwa kwa ubongo, munthu yemwe angachite

chinthu chonga icho, kapena kupanga ndemanga yonga iyo. Ndithudi.

123 Kulira kozolowereka kwachikale, ngakhalebe, "Tiloreni ife tiwone Inu mukuchita chozizwitsa. Mbuye, ife tikukhumba chozizwitsa kuchokera kwa Inu." Pamene, tsiku lirilonse, ora lirilonse, izo zinali kuchitika motsatira kumene, basi monga Mulungu akanatsogolera kuti izo zichitike. Koma iwo sanali kukhalapo. Ngati iwo analipo, iwo amadzitcha izo "Belezebule, mdierekezi." Mwaona? "Mbuye, ife tikanakhumba ngati Inu mukadachita izo mwanjira yomwe ife tikanafunira kuti Inu muchite izo." Ndi zimenezo. "Mupite kumene ife tikufuna kuti Inu mupiteko, mukachite zomwe ife tikufuna." O, inde. Iwo analibe zingwe pa Iye. Ayi, bwana. Ndicho chifukwa iwo anachita kumuchotsa Iye pakati pawo. Inde, bwana. Iwo akuyesera kuchita chinthu chomwecho lero. Ndipo kupyolera mu chitaganya cha mipingo, iwo potsiriza akwaniritsa kuchita izo, mwaona, onse a iwo akupita palimodzi. Kulira kozolowereka kwachikale kuja.

124 Pano ife tikuwona, kachiwiri, malo achipembedzo kwambiri, opambana, azamulungu opukutidwa, akuitana momveka kachiwiri, ndipo momutsutsa Iye, akuitana momveka. Azamulungu opambana kumene, omwe akanayenera kudziwa mosiyana; mipingo yapamwamba kwambiri, ndi azamulungu ophunzitsidwa bwino, anamuchotsa Iye pakati pawo. Iwo sakuzifuna Izo.

Inu mukuti, "Uko nkulakwa, M'bale Branham."

Ndiye inu simunali pano kuti muyione Mibadwo ya Mpingo, kapena kuimva iyo ikulalikidwa. Inu simunali kuno, pamene, M'badwo wa Mpingo wa Laodikaya uwu unali umodzi wokha umene iwo anamuponyera Iye kunja kwa mpingo. Ndipo Iye anali ali kunja, kunjako, akugogoda, kuyesera kuti abwerere mkati. Iwo anamutayira Iye panja chifukwa iwo analibe naye ntchito Iye. Iwo akumupachika Iye katsopano. Ameni! Ife tingapite motalika chotani?

125 Kumbukirani, mneneri wa Mawu a Mulungu anatiuziratu ife, mu Timoteo Wachiwiri 3, ngati inu mukuzilemba izo. Ife tiribe nthawi yoti tiziwerenge izo. Koma ananena, kuti, "Mu masiku otsiriza, onyoza akanadzabwera. Iwo akanati adzakhale ammutu, oganiza za pamwamba, okonda zosangalatsa koposa kukonda Mulungu; onenera zabodza, osadzigwira, owopsya, ndi onyoza iwo amene ali abwino, opereka amzawo, ammutu, oganiza zapamwamba, ophunzira; okhala nawo maonekedwe aumulungu, koma kumakana Mphamvu yakeyo: kwa oterowo chokaniko! Pakuti uwu ndi mtundu umene umatenga opusa, akazi odula tsitsi." ovala zazifupi, a nkhope-zolochedwa, "omka malo ndi malo, ndi kumawatsogolera iwo mogwidwa." Ndizo ndendende. Iye anati, "Chokaniko kwa izo, mu masiku otsiriza."

Tiyeni tizimumvera mneneri. Chokaniko ku zinthu zimenezo mu masiku otsiriza. Izo ziri pano. Ine ndikuitanira kwa Mpingo tsopano. Inde, bwana. Chokaniko kwa izo.

126 Iwo ali, iwo, a_atumiki a tsiku lino, anayenera kumazidziwa zinthu zimenezi. Iwo bwezi atamudziwa Yesu mu masiku Ake. Iwo bwezi atadziwa. Ndipo tsopano iwo akanayenera kumazidziwa izo, koma iwo sali kuzidziwa izo.

Basi monga aphunzitsi Achiyuda a masiku Ake akanayenera kumudziwa Iye pa tsiku Lake, chotero izo ziri lero, wa Mawu a Mulungu otsimikiziridwa bwinobwino pamenepo. Iye anali Mawu, ndipo Iye anatsimikizira kuti Iye anali Mawu. Iye anatsimikizira kuti Iye anali Mawu a tsiku limenelo. Ndipo Mulungu watsimikizira lero kuti Iye ali Mawu a tsiku lino, Kuwala kwa ora. Ndipo iwo bwezi atazidziwa izo pamenepo, ndipo iwo akanayenera kumazidziwa izo tsopano. Iwo anamupachika Iye apo, ndipo iwo akumupachita Iye tsopano. Ine ndikuwatsutsa iwo za icho! Kulondola. Icho chikungopitirira kuthwanima kupyolera mwa ine, "Ndikuwatsutsa iwo, chifukwa Mulungu adzawalipitsa iwo chifukwa cha icho!"

127 Ayuda a tsiku lawo.... Mulungu kachiwiri, mu masiku pa dziko lapansi, Yesu anati, "Yerusalemu, Yerusalemu, ndikusonkhanitsa mowirikiza chotani iwe mu gulu limodzi lalikulu, koma iwe sukufuna ayi."

Momwe Mulungu wayesera, mu masiku otsiriza ano, kuti awayanjanitse anthu Ake palimodzi, koma inu simukufuna ayi. Inu mwakhumba kachikhulupiriro kanu, chotero tsopano inu mwaperekedwa ku chiwonongeko. Ndicho chimene Yerusalemu analandira; iye wagwetsedwera pansi, wawotchedwa pansi, iye salinso. Ndipo ndizo ndendende zomwe ziti zikhale, ena amasiku awa, ku zinthu zonse zazikulu izi kuno. Tizikhulupiriro tanu tatikulu ndi zipembedzo zidzafa ndi kuwonongeka, koma Mawu a Mulungu adzakhala Amuyaya ndipo adzakhalapo kwanthawi zonse.

128 Mabala Ake akuya kwambiri akuchokera ku nyumba ya iwo otchedwa abwenzi. Taganizani, taganizani za izo. Taganizani za izo! Imani! Ine ndikudikira miniti. Atumiki, taganizani za izo! Kodi mabala ake anachokera kuti? Nyumba ya iwo otchedwa abwenzi Ake. Monga izo zinali, chotero izo ziri. Taganizani za izo! Pa Gologota Iye sanali atazunguliridwa ndi_ndi opulikira, achikunja, koma ndi azitumiki omwe ankati ankamukonda Iye. Ndipo lero, pamene Uthenga watsimikiziridwa bwinobwino, pamene zizindikiro zazikulu za chiwukitsiro Chake zatsimikiziridwa pakati pathu, si apamsewu kunja uko omwe amalumphira pa iwe, ndi iwo otchedwa atumiki. Iwo amene akuyenera kuti azimukonda Iye, ndi omwe Iye wazunguliridwa nawo lero. "Ife sitikhala nacho Chinthu chimenecho pakati pathu. Ife sitikhala naye Munthu uyu kuti azilamulira pa ife. Ife sitimamuthandizira. Ife sitikhala ndi chiyanjano ndi Izo, mu mzinda uno, ngati

Chinthu icho chiti chibwere njira ino. Sindicho kanthu koma zamizimu. Ndi mdierekezi.” Posawadziwa Mawu a Mulungu, akhungu akutsogolera akhungu. Monga izo zinali pamenepo, taganizani, chotero izo ziri tsopano. Basi monga izo zinali pamenepo, chotero izo ziri tsopano. Taganizani!

129 Mphamvu Yake kuti ichiritse ndi kumasula amuna ndi akazi kuchoka ku chikondi cha dziko lapakali pano ili, kuchoka kwa odula tsitsi, Mayezebeli olocha nkhope omwe amadzitcha okha Akhristu; ndi kumabala moyo wotero monga umenewo, osuta-fodya, onena nthabwala-zonyansa. Atakhala pansi ndi kukhala nalo gulu la umishonare, ndipo kuluka ndi kusoka, ndi kuyankhula, ndi kunyozetsa, ndi_ndi kutuluka panja pa msewu ndi kuvala zazifupi, ndi chirichonse monga izo; ndiyeno nkumadzitcha okha Akhristu, pamaso pa akazi ena.

Inu mukukumbukira nkhani yanga yokhudza kapolo podziwa kuti iye anali mwana wa mfumu, khalidwe lake. Kodi ife tikuyenera kukhala chiyani? Amuna ndi akazi... ndi kumakana....

130 Atumiki awa, maguwa awa kumene Iye akulandira kulasidwa Kwake, iwo akweza ndi kuvomereza makhalidwe a mtundu umenewo pakati pa anthu, kumene iwo akumulasa Iye. Iwo akukana Mphamvu kuti_kuti iwamasule iwo kuchoka kwa izo, ndipo iwo akuvomereza izo kuti zikhale chomwecho. Pamene, izo ziri mosiyana ndi Mawu a Mulungu, kuti mkazi azidula tsitsi lake, kapena kuti azilocha nkhope yake, kapena kuti azivala zazifupi. Ndizo zosiyana ndi Mawu a Mulungu, koma iwo amavomereza izo, akupanga Gologota wina (kuchokera kuti? kuchokera pa msewu? kuchokera ku chipinda chaku mowa?) kuchokera ku guwa, kuchokera ku guwa.

131 Ndipo, kachiwiri, kulirako kunali chiyani? “Iye akudzipanga Iyeyekha Mulungu.” Iwo anakana Umulungu Wake. Iwo akuyesa kumugawaniza Iye ndi kupanga atatu kapena Amulungu anai kuchokera mwa Iye. Pamene, Iye ali Mulungu; Iye anali Mulungu; Iye nthawizonse adzakhala ali Mulungu, yemweyo dzulo, lero, ndi kwa nthawizonse. Pamene iwe uyankhula za Mulungu mmodzi, kwa iwo, iwo amaseka pa iwe. “Ife timakhulupirira mu utatu woyera.” Ine ndimakhulupirira mwa Mulungu mmodzi woyera, inde, bwana, Mphamvu Yake kuti achiritse, kuti amasule, ndi kuwatenga anthu awa kuchoka ku chikondi cha padziko, kuti iwamasule iwo monga Iye anamchitira Maria wa Magadala.

Kumbukirani, iye anali Yezebeli wamng'ono wolochedwa, nayenso. Iye anali ndi ziwanda zisanu ndi ziwiri mwa iye. Iye anali wodzivula modolola. Basi monga mkazi wamakono pa msewu lero; pitani kulikonse kumene inu mukufuna ndipo penyani. Ngati inu simumakhulupirira kuti anthu amagwada pa guwa la chosemedwa cha akazi amaliseche, penyani panja mu msewu lero. Monga izo zinali mu masiku a Sodomu, chomwecho izo zidzakhala ziri. Yang'anani kunja, ngati inu simuli kukhulupirira izo, ingopitani kulikonse. Katseguleni pepala, katseguleni magazini, kayang'aneni pa cholengeza, kodi inu mukupezapo chiyani? Kumbukirani zomwe ilo linanena, “Pamene ana aamuna a Mulungu anawawona ana aakazi a anthu kuti anali okongola, iwo anadzitengera kwa iwo akazi.”

Tayang'anani pa chonyozetsa mu England, tayang'anani pa chonyezetsa kuno, tayang'anani pa chinthu chonsecho, yakhala nyumba ya aziwerewere.

132 Nchifukwa chiyani izo ziri? Nchifukwa chiyani Russia anakhala chikominisi? Chifukwa cha zachabe ndi zauve, ndi kupanda Mphamvu kwa mpingo wa Katolika. Ndipo ndicho ndendende chifukwa chimene fuko lino likulandidwa, chikominisi ndi chitaganya cha mipingo, ndipo likudzilumikiza lokha ndi mpingo wa Katolika. Chimene, chikominisi ndi Chikatolika zidzalumikizana limodzi, inu mukudziwa, ndipo pano iwo akuchita izo. Chifukwa chiyani? Chifukwa iwo awukana Uthenga umene umawalekanitsa iwo ndi kuwapanga iwo anthu osiyana. Ndicho ndendende chifukwa chake.

133 Ndipo atumiki mu guwa akuyanjana nazo izo, chifukwa cha tikiti ya chakudya, chifukwa cha maimidwe a chitukuko kwa kachikhulupiriro kena, kuti, “Ine ndine Wakuti-ndi- wakuti,” kusinthanitsa maphunziro ndi Mphamvu ya Mulungu;

Amasuleni iwo kuchokera ku mtundu wa anthu amisala uno, monga Maria wa Magadala. Mphamvu yomwe imene ingamutenge wamng'ono wodzivula modolola uja pa msewu, ndi kumupangitsa iye kuvala zovala zake ndi kumachita monga dona, kupanga Mkhristu kuchokera mwa iye, iwo anaitsutsa Mphamvu imeneyo, ndi kumupachika Munthu yemwe anali nayo Iyo, pa Gologota.

Ndipo lero, Uthenga womwe ndi Mzimu Woyera umene ungatenge wodzivula modolola wamng'ono uyo ndi kumupanga iye kumavala monga dona ndi kumachita monga Mkhristu, iwo amautcha Iwo “zotentheka.” Iwo sakufuna kuti Iwo usakanizikana pakati pa osonkhana awo, kuti Iwo uwafikitse pokondowezedwa, kuwapangitsa akazi ena kuti azichita izo. Kodi iwo akuchita chiyani? Iwo akuwuthamangitsira Iwo kunja, basi monga iwo anachitira pamenepo. Ndipo tsopano iwo akuwapachika Mawu omwe ndi kumati Iwo anali a m'badwo wina. Ine ndikuwatsutsa iwo kachiwiri, inde, bwana, mofanana basi monga iwo anatsutsidwira pamenepo.

134 Chizindikiro chimene chinampanga Legio wakale kuti avale zovala zake. Kumbukirani, munthu yemwe amavula zovala zake ndi wamisala. Mwaona? Nanga bwanji mkazi? Legio anali wamisala; iye ankavula

zovala zake pa iye. Mulungu anatenga Mphamvu Yake ndipo anamupangitsa iye kuvala zovala zake. Iye anavekedwa, ali mu malingaliro ake abwino, anakhala pansi pa mapazi a Yesu. Tayang'anani pa Mphamvu yomwe inamupanga Bartumeyo wachikulire wakhungu kuti apenye, pakati pomwe pa tizikhulupiriro tawo. Iye anali pa dziko lapansi pamene uko kunali kusakhulupirira basi monga iko kulipo lero, koma izo sizinamulepheretse Iye. Iye anapitirirabe. Iye sanabweze nkhonya kwa iwo. Iye anawauza iwo, "Ndinu a atate wanu, mdierekezi." Iye anaweruza chinthu chonsecho.

135 Mphamvu yomwe ikanakhoza kumuwutsa Lazaro kuchokera mmanda, ndi kumupatsanso mkazi waku Naini mwana wake! (O Mulungu) Mphamvu yomwe inkakhoza kuchita zinthu zimenezo, yomwe inkakhoza kuneneratu zinthu zomwe zinkachitika. "Pali abulu awiri....pali bulu, womangidwa pa mphambano ziwiri," ndi zinthu zonse izi zomwe Iye analosera. Mwamuna yemwe amene anali nayo Mphamvu, "Kutali ndi Iye. Ife sitikhala naye Iye pakati pa anthu athu. Iye akusokoneza zophunzitsa zathu," ndipo iwo anamupachika Iye.

Chinthu chofanana chomwecho lero, "Kutali ndi Mzimu Woyera," iwo sakufuna kanthu kochita nawo Iwo. "Iwo umatsutsa ndipo kumachita zinthu izi, ndipo kumawauza anthu athu zinthu izi, ife sitikufuna kuti zifike posakanizikana pakati pa mabungwe athu. Ndizo zotsutsana ndi tizikhulupiriro tathu." Iwo akumupachika Iye kachiwiri. O, maine!

Zindikirani tsopano pamene ife tikutseka. Tiyenera kutseka. Ndipo, kachiwiri, iwo akuzitcha Izo "zotentheka."

136 Ndipo iwo anamutcha Iye "wotentheka." Iwo ankati, "Iye anali wopenga." Aliyense akudziwa kuti Baibulo linanena kuti, "Yesu anali," Afarisi aja ankati, "Munthu uyu ndi Msamaria, ndipo Iye ndi wamisala." Tsopano mawu akuti misala amatanthauza chiyani? "Wopenga." "Munthu uyo ndi wopenga. Iwo ali gulu la anthu openga omwe akumutsatira Iye. Iye ndi Belezebule."

Ndipo, kachiwiri, iwo akunena chinthu chomwecho, "Ndiwo mtundu wa ufiti. Ndi m'bwebwe," kumuyika Iye kachiwiri pa mtanda wa manyazi. Mtanda wotani? Manyazi otani? Iye ndi Mawu otsimikiziridwa; akuwaseka Iwo, kumawauza anthu Iwo ndi mdierekezi. Kupanga chinachake.... ndi kumachitcha....

137 Iye anati, "Iwo akutcha ntchito zoyera za Mulungu kuti 'mzimu woipa ukuchita izo,' palibe chikhululukiro kwa iwo." Kupangitsa manyazi Mawu Ake, kuyesera kuti awayalutse Iwo ndi kuwatcha Iwo chonyengezera kapena zotentheka.

"Musati muzipita kwa izo. Musamakakhalepo ku misonkhano imeneyo." Kodi iwo akuchita chiyani pochita izo? Iwo akutenga misomali ya kachikhulupiriro ka chipembedzo chawo. Ndiko kulondola. Aphunzitsi osaka zosangalatsa awa, achidziko, opanda umulungu, amisala mwachipembedzo, akutenga misomali ya chipembedzo ndi kumamupachika Mwana wa Mulungu ndi iyo, katsopano, kuchokera mu maguwa awo. Nchifukwa chiyani iwo akuchita izi? "Iwo amakonda kuyamikira kwa anthu," madigirii omwe mpingo ungakhoze kuwapatsa iwo, "mochuluka kuposa chikondi cha Mawu a Mulungu." Ine ndikuwaweruza iwo. Iwo sangakhoze kutengera za dziko, chifukwa iwo ali...Sangakhoze kutengera za Mawu, chifukwa iwo akutengera kale za mdziko. Iwo achita kale izo. Tsiku lachinyengo limene ife tiri kukhalamo! Kodi izi sizirri...

138 Kodi Gologota mmodzi sali wokwanira kwa Ambuye wanga? Nchifukwa chiyani kuti inu mukuchita izi? Inu amene mukuyenera kuti muzimukonda Iye, inu amene mukudziwa kuti Awa ndiwo Mawu Ake, inu amene mukhoza kuwerenga Chivumbulutso mutu wa 22, umati, "Yense yemwe ati adzatenge Mawu amodzi kapena kuwonjezera Mawu amodzi," nchifukwa chiyani inu mukuchita izi? Kodi Gologota mmodzi sali wokwanira kwa Iye? Ine ndikuima mwa kumutetezera Kwake. Ine ndine nduna Yake, ndipo ine ndikukutsutsani inu mwa Mawu a Mulungu. Sinthani njira zanu kapena inu mupita ku gehena. Zipembedzo zanu zidzaphwasuka. Ine ndikukutsutsani inu mu Kukhalapo kwa Woweruza, kulondola, inu, ndi maonekedwe anu aumulungu, zinyengo. Kodi inu mumachitchula chani? Kodi Gologota mmodzi sali wokwanira?

139 Monga Petro anati, "Makolo anu achipembedzo," Petro anakutsutsani inu ndi^Anati, "Ndani wa makolo anu yemwe sanachichite ichi?" Stefano anachita chinthu chomwecho: "Ndi manja oipa inu mwamupachika Kalonga wa Moyo."

Kodi Yesu sanati, Iye mwini, "Ndi mmodzi uti wa makolo anu amene asanawaike aneneri mu manda? Ndipo inu mumawakongoletsa iwo pambuyo pake"? Chotero izo zakhala ziri kwa munthu wolungama kupyola mu mibadwo! Kotero ine ndikutsutsa gulu ili lopukutidwa- mwapamwamba lopita ku tchalitchi la anthu omukana- Khristu la tsiku lino. Inu ndi maonekedwe anu aumulungu mukumupachika Khristu wanga nthawi yachiwiri, pa kuwawuza anthu kuti Mawu awa ndi a tsiku lina lake, ndipo iwo sali a tsiku lino. Ine ndikukutsutsani inu. Ndinu olakwa ndi mulandu womwewo umene iwo anali tsiku lija la kupachikidwa. Lapani ndi kubwerera kwa Mulungu, kapena muwonongeke.

140 Ndipo kachiwiri ine ndikuti, "Kuno," mipingo, "iwo," aphunzitsi, "akupachika," pa kuchitira mwano,

“Iye,” Mawu. Mulungu akhale wochuluka chifundo! Ndiroleni ine ndinene izo kachiwiri. Izo mwina zingakhale zitasokonezeka pa tepi. “Kuno,” mipingo, “iwo,” azibusa, “akumupachika,” pa kuchitira mwano, “Iye,” Mawu. Palibe zodabwitsa izo ziri kachiwiri:

Pakati pa miyala yosweka ndi mlengalenga mwamdima

Mpulumutsi wanga anaweramitsa mutu Wake ndipo anafa,

Koma chotchinga chotseguka chinauluka njira

Ya ku zisangalalo za Kumwamba ndi tsiku losatha.

Ine ndikunena izi pa tepi iyi, ndi kwa omvetsera awa. Ine ndikunena izi pansi pa kudzoza kwa Mzimu Woyera. Ndani ali pa mbali ya Ambuye, mloleni iye adze pansi pa Mawu awa! Mulungu zedi adzawubweretsa m'badwo wochimwa uwu, womukana-Khristu, wokana-Khristu ku chiweruzo, chifukwa chochitira mwano, kupachika kwa Mawu Ake ozindikiritsidwa. Iwo akubwera ku Chiweruzo. Ine ndikuwutsutsa iwo! “Ndani ali pa mbali ya Ambuye,” anatero Mose, “mloleni iye abwere kwa ine,” pamene Lawi la Moto linapachika pamenepo ngati umboni. Ndani ali ku mbali ya Ambuye, mloleni iye awatenge Mawu, akane kachikhulupiriro kake, ndipo amutsate Yesu Khristu pa tsiku. Ndipo ine ndidzakumana nanu inu mmawa.

Tiyeni ife tiweramitse mitu yathu tsopano kwa mawu a pemphero.

141 O Ambuye Mulungu, Wopereka wa Moyo Wamuyaya ndi Mwini wa Mawu awa, Yemwe munamubweretsa kachiwiri Ambuye Yesu kuchokera kwa akufa, Yemwe anazindikiritsa izo bwinobwino pamaso pa_m'badwo wa anthu osakhulupirira. Izi zakhala motalikitsa, mmawa uno. Ambiri akhala pano. Mpingo wadzaza. Anthu akuima mozungulira. Ndipo matepi akadali nkupangidwa, kuti apite kunjako kudutsa mdziko lonse, mu malo osiyana. Atumiki akamvetsera izi mowerengera mwawo. Ine ndikuwapempherera iwo, Ambuye. Mulole mawu awa agwere mwakuya kupita mu mtima, acheke mwakuya, adulemo chidziko chonse. Kuti iwo akakhoze kuyankhula monga, mtumiki wamng'ono wa Chimethodisti uyu uko ku Kentucky, anabwera kwa ine tsiku lina, ndipo anati, “Pamene ine ndinali kumvetsera Mibadwo Isanu ndi iwiri ya Mpingo, ine ndinamva ilo likufuulira, 'Chokaniko ku makoma amenewo a Babeloni,' ” anati, “Ine ndinazisiya izo ndipo ndinachokako. Ine sindikudziwa njira iti yoti ndizipita kapena choti ndichite, koma ine ndinachokako.” Kudalitsidwe kulimbamtima kwa mnyamata ameneyo, ndi mkazake, ndi ana awiri kapena atatu.

142 Mulungu, mulole ambiri apeze njira yawo kupita ku Mawu a Mulungu, njira yokha ya Moyo, pakuti Iye ali Mawu. Ine ndikupempherera mmodzi aliyense, Atate. Nthawizina pa kunena zinthu izi, sindizo nkhaza; ndi mwa chikondi, chifukwa chikondi chimakonza. Ndipo ine ndikupemphera, Mulungu, kuti anthu amvetse izo kuti zikhale mwanjira imeneyo, kuti chimatanthauza chikhale chokonza.

Inu Amene munachita kuwakonza, ndipo munadzawapempherera iwo pa mtanda, kuti, “Atate, akhululukireni iwo. Iwo, ali akhungu, iwo sali kumvetsa basi chimene iwo akuchita.” Ine ndikuwapempherera atumiki awo lero amene akuwapachika Mawu kachiwiri, pa kutenga tizikhulupiriro tawo ndi zipembedzo ndi mbalume, ndi kuloweza izo mmalo mwa Mawu a Moyo. Ndiyeno, pamaso pa anthu, iwo amatsutsa Choonadi chenicheni chimene Mulungu akuchitsimikizira kuti chiri Choonadi Chake. Ife tikuwapempherera iwo, Atate, kuti Inu muwaitanire iwo ku Mgonero wa Chikwati kachiwiri. Ndipo mulole iwo abwere nthawi ino, ndipo asapeze zowiringula, pakuti ine ndikuzindikira kuti kuitana kotsiriza mwina kungakhale kutapita kale. Kukhoza kukhala kuli mochedwa kwambiri tsopano. Ine ndikudalira kuti sichoncho.

143 Dalitsani osonkhana pang'ono awa amene ali pano, mazana pang'ono a anthu awa omwe asonkhana muno mmawa uno, tsiku lotentha ili, akhala pano motalikitsa, mwinamwake maora awiri kapena kupitirira, utumiki, ndi kumvetsera. Iwo sanachoke. Iwo anakhala bata ndi kumamvetsera. Ambiri a iwo akuyembekeza chakudya chawo chamadzulo, ndipo akazi ataima ndi ana awo, ndipo iwo akuyembekezera. Iwo akugwiritsabe ku Mawu aliwonse.

Ambuye, ine ndikuzindikira chomwe chiti chidzachitike kwa ine pa Tsiku la Chiweruzo ngati ine ndawasocheretsa anthu amenewo. Ine ndikuzindikira, Ambuye, kuzindikira kumene ine ndingakhoze kukumverera. Kuti, ine ndikuyesera kuti ndiwatengere iwo ku Mawu, ndi kuwalola iwo akhale moyo ndi Mawu, kuwauza iwo kuti Ndinu “yemweyo dzulo, lero, ndi kwa nthawizonse,” kuti Mzimu Woyera wawukulu uli Yesu Khristu, mu maonekedwe basi a Mzimu Woyera, Munthu yemweyo. Inu munanena chomwecho. “Kanthawi pang'ono ndipo dziko silindiwonanso Ine; komabe inu mudzandiwona Ine, pakuti Ine ndidzakhala ndi inu, ngakhale mwa inu.” Ndipo ine ndikudziwa kuti izi ndi Inu, Ambuye. Ndipo ife tikukhulupirira Inu, chifukwa ife tikukuonani Inu mukuchita chinthu chomwecho pakati pathu.

144 Ife tikudzipereka tokha lero, mwaubwino, ife tikutero pano mwa osonkhana awa ndi pa matepi. Ambuye, basi pa miniti ino, mulole mwamuna aliyense ndi mkazi, mnyamata kapena msungwana, yemwe alipo pano, kapena waima kunja, kapena akumva izo pa tepi, mulole ife pa mphindi ino tipange

kudzipereka kwakuya ndi kudzipereka mwini wathu wathunthu tokha ku utumiki wa Mulungu.

Sunthirani pa omvetsera, Ambuye, mu Mphamvu, ndipo chiritsani odwala. Iwo anati iwo ali ndi mnyamata wamng'ono wolumala wakhala cha apa. Mulole Mzimu Woyera wawukuluwo^Ife tikudziwa, kuti tikangokhala mu Kukhalapo Kwake monga izi ziri, Iwo uchita izo. Ngati Inu mungakhoze kupita kupyolera mu wailesi ndi televizioni, kunja kudutsa mu maiko, ndi kumachiza odwala, "Inu munatumiza Mawu Anu ndipo Iwo anakawachiza iwo," Inu mukhoza kuchita chinthu chomwecho pa miniti ino. Ine ndikupemphera, Mulungu, kuti Inu muchiza munthu wodwala aliyense, wolumala aliyense, wosautsika aliyense, pano ndi amene atakamvere Mawu awa. Mulungu, perekani izi. Pemphero langa liri kwa iwo.

Ndi chikondi cha Khristu mu mtima wanga ndi kumverera chifukwa cha osowa, ine ndikuwapereka iwo, Ambuye, kwa Inu, pa guwa la nsembe, pamene thupi Lamagazi la Mwanawankhosa uja lagona monga chitetezero cha machimo athu ndi matenda, zagona apo. Ine ndikuchonderera chifundo kwa anthu. Ine ndikufuna ndiyime monga Mose anachitira, pakati chifukwa cha iwo, Ambuye, ndi kuti, "Mulungu, achitireni chifundo iwo, kwa iwo, motalika pang'ono, ndipo apatseni iwo mwayi wina." Musati muchite izo pakali pano, Ambuye. Lolani Uthenga upite patsogolo pang'ono kaye.

145 Iwo aweruzidwa, Ambuye. Ine ndikupemphera kuti chifundo Chanu ndi chisomo zitambasukire kwa munthu wotsiriza yemwe ali nalo dzina lake pa Bukhu. Ndipo ine ndikudziwa iwo atero. Si chovuta kupemphera motsutsana ndi Mawu anu Auzimu, kapena motsutsa.... kapena motsutsana.... ndi Mawu Auzimu, ine ndikutantha kuti nditi, Ambuye; Mawu omwe alonjezedwa, Mawu amene atsimikiziridwa, Mawu amene anawakonzeratu anthu awa kumbuyo uko maziko a dziko asanaikidwe. Siziri zovuta kuti tipemphere kuti Inu muwapulumutse iwo amene maina awo ali pa Bukhu, chifukwa ine ndikudziwa Inu muchita izo. Yesu ananena chomwecho, "Onse amene Atate andipatsa Ine adzabwera." Ndipo palibe munthu angakhoze kubwera pokha pokha chitapatsidwa kwa iye.

Tsopano ine ndikupemphera, Mulungu, kuti kulikonse kumene Mawu awa akagwera, konse pa tepi ndi ali panowa, kuti Mzimu Woyera uyitane munthu aliyense wokonzedweratu pakali pano, kuchokera ku maziko a dziko pamene dzina lawo linaikidwa pa Bukhu la Moyo wa Mwana wankhosa. Mulole iwo amve Liwu la Mulungu likuyankhula lero, mu Liwu laling'ono lija, lodekha, lochepa, pansi mu mtima mwawo, likuti, "Iyi ndi njira, yenda mu Iyo." Perekani izi, Atate. Ine ndikufunsa izi mu Dzina la Yesu.

146 Ndipo pamene tikadalipo ife taweramitsa mitu yathu pano mwa omvetsera. Ngati inu mukukhulupirira izi kuti ziri Choonadi, ndipo inu....(Ine ndaika, dzanja langa pa mipango iyi ili apa, ndi maphukusi a odwala ndi osautsika.) Ine ndikufuna kuti ndikufunseni inu funso, modzipereka tsopano. Ine sindimabwera kuno basi kuti ndidzamvedwe. Ine_ine_ ine ndatopa. Ine ndafooka. Ine sindiri wamng'ono monga ine ndinaliri, ndipo ine ndikudziwa masiku athu awerengeredwa. Ndipo ine ndikudziwa ine ndiyenera kuikamo kanthu kakang'ono kalikonse kamene ine ndingakhoze, kwa Ufumu wa Mulungu. Ine ndiyenera kuti ndilalikire nthawi iliyonse imene ine ndingapeze mwayi. Ine ndiyenera kutero, ine ndiyenera kuti ndipite ngakhale ine ndikumverera ngati izo kapena ayi.

Ine ndinabwera kuno chifukwa ine ndikumverera kuti ndichite izo. Ine ndikufuna kuti ndichite izo. Ine ndimakukondani inu. Ndipo ine sindimanena zinthu mwaukali ndi molimba, naponso, chifukwa ine ndikufuna kutero. Pali kututuma mkati mwa ine. Chinthu ichi chomwe chimene chakhala chitatsimikiziridwa ndi chinthu chimene chimandikakamiza ine kuti ndizichita zinthu izi. Ine ndimanena izo mwachifundo, ndi chikondi. Ine sindimatanthauza kuti ndizizazira akazi athu kapena amuna athu. Ine sinditanthauza kuti ndizichita zimenezo, m'bale, mlongo. Ine ndikungotanthauza kuti ndikubweretseni inu ku_ malo akuthwa, kumene inu mungakhoze kuwona kukonza ndi chikwapu cha Ambuye, kuti inu muyenera kubwera mkati tsopano. Musati muzinyalanyaze izo; inu mukhoza kuyembekezera motalika kwambiri.

147 Ndipo inu amene mukukhumba kuti mubwere pa mbali ya Ambuye, ndi kudzipereka kwathunthu mu mtima mwanu, mu kukhalapo mwa omvetsera tsopano, kapena mu dziko kumene matepi ati akakhale; inu mungatero, ndi mitu yanu yoweramitsidwa....Musati mudzutse manja anu ngati inu simukutanthauza izo. Tsopano ngati inu mukutanthauza kwenikweni izo, inu mukufuna kuti mubwere kwa Ambuye, ndi moyo wodzipereka mochulukira, kodi inu simungangokweza dzanja lanu pakali pano. Inu, Ambuye akudalitseni inu. Inu mukudzipereka nokha mwatsopano kwa Khristu, kuti muyesere kunyamula chitonzo. Inu mukuti, "Ine ndikulolera lero kuti nditenge chitonzo." Ine ndaimika manja anga onse mmwamba, inenso. Ine, ine ndikufuna kuti nditenge chitonzo cha Yesu Khristu pa ine. Ine mokondwera ndikuvala chilemba ichi chotchedwa "woyera wodzigudubuza," chirichonse chimene inu mungafune kuti muchitche icho. Ine ndikuvala icho ndi kunyadira, chifukwa ndi mwa chifukwa cha Ambuye. Ine ndikuvala icho ndi kunyadira.

148 Kodi inu nonse simukufuna kuti muchite mofanana? Kwezani manja anu, ndikuti, "Mwa chisomo cha Mulungu, ine ndikufuna...ine..."

Ophunzira anabwerera, akuganiza kuti iwo unali mwayi wawukulu kunyamula chitonzo cha Dzina Lake. Kapena, inu mukufuna kuti munyamule chitonzo cha katswiri wina waku Hollywood, kapena chinachake cha televizioni, kapena membala wina wa mpingo, kapena chinachake? Kapena, kodi inu mukufuna chitonzo cha Mawu a Yesu Khristu? "Ndipatseni ine chitonzo cha Mawu, Ambuye. Ine

ndikudziwa Iye ananyamula chitonzo cha Mawu a Mulungu. Ndiroleni ine ndinyamule icho, inenso, Ambuye.”

Ndipo mtanda wopatulika uwu ine ndidzanyamula

Mpaka imfa itadzandimasula ine,

Ndiye nkupita kwathu, kukavala korona.

Kudzakhala korona tsiku lina wa ife. Iye ali nkupangidwa tsopano. Pamene moyo wapadziko uno watha, ndiye ife tikudziwa izo zidzakhala ziri bwino.

Tsopano palibe malo oti tiwabweretse anthu kuzungulira pa guwa. Lolani mpando wanu, pamene inu muli, pakhale paguwa. “Onse amene akhulupirira.....” Pamene ife tikupemphera.

149 Atate Akumwamba, izo zinawoneka kwa ine ngati kuti pafupi dzanja lirilonse la wamng'ono ndi wamkulu, linali mmwamba, mwa omvetsera awa. Ndipo ine ndikupemphera kuti, nthawi iliyonse yomwe tepiyi iti idzaseweredwe, kuti anthu adzakweze manja awo, ndi kugwada pansi mu chipinda; bambo ndi mai kupita ndi kukagwirana chanza wina ndi mzake, ndi kuti, “Wokondedwa, ife takhala tiri mamembala a mpingo utali wokwanira. Tiye tibwere kwa Khristu.” Perekani izi, Ambuye.

Adalitseni anthu awa. Ine ndikupemphera kuti Inu muwapatse iwo, Ambuye, moyo wopatulika. Ambiri a iwo, Ambuye, ndi anthu abwino. Iwo ali_iwo ndi anthu Anu; iwo anangokhala alibe Choonadi. Ndipo ine ndikupemphera kuti Inu muwasonyeze iwo Choonadi Chanu, Ambuye. “Mawu Anu ali Choonadi.”

Monga Inu munanena mu Yohane, ine ndikuganiza pafupi mutu wa 17, Inu munati, “Ayeretseni iwo, Atate, kupyolera mu Choonadi. Mawu Anu ali Choonadi.” Ndipo Izo panonso, Mawu Anu, ali Choonadi panobe. Iwo nthawizonse ali Choonadi, chifukwa Iwo ndi Mulungu. Ndipo ine ndikupemphera, Mulungu, kuti Inu muwayeretse iwo kupyolera mu Choonadi. Ndizo kuti, ayeretseni, atsukeni iwo kuchoka ku tizikhulupiriro tonse ndi zipembedzo. Ayeretseni iwo kuchoka ku zinthu zonse zachidziko, kupita ku moyo wopatulika wa Mawu. Perekani izi, Ambuye. Iwo ndi Anu tsopano. Inu munalonjeza kuti mudzachita izo. Ndipo monga wantchito Wanu, ine ndikupereka pemphero langa mmalo mwawo. Mu Dzina la Yesu Khristu.

150 Tsopano ndi mitu yathu yoweramitsidwa, tiyeni tiyimbe nyimbo iyi pamene ife tikupitiriza kupemphera.

Yesu analipira zonse,

Zonse kwa Iye..(Taganizani za izo!) Tchimo...

Dzulo ine ndinali mu_malo, ndipo mwamuna anali kundiyeza ine suti yomwe m'bale muno mu mpingo wandigulira ine. Iye anati, “Suti yanu imawoneka yotentha, ndipo ine ndakugulirani inu imodzi yozizirira.”

Ndipo ine ndinapita uko kuti ndikaidulitse iyo, ndipo iye anati, “ phewa lanu lamanja likugwera pansi. Inu muyenera kuti munanyamula katundu wolemera tsiku lina.”

Ndipo ine ndinaganiza, “Inde, katundu wa tchimo. Koma Yesu analipirira iwo onse.” Mvetserani pamene ife tikuyiimba iyo.

Yesu analipira onse,

Ndiye wonse, moyo wanga wonse, kwa Iye ine

Kodi tchimo linali litachita chiyani?

Tchimo linali litasiya dontho lofiira, Iye walitsuka ngati chisanu.

151 Mulungu, chitirani chifundo kwa ife. Pamene nthawi yakuya iyi ya kusinkhasinkha, mulole Mawu alowerere mkati mwakuya, Ambuye, mu mtima. Mulole anthu, ngakhale iwo akhale atachedwa ku chakudya chamadzulo^Koma, Ambuye, izi ndi zoposa chakudya. Uwu ndi Moyo. “Mawu Anga ndiwo chakudya,” Inu munatero. Ndipo ndicho chimene miyoyo yathu yanjala ikudyererapo.

Tsopano titengeni ife, Ambuye, tiwumbeni ife. Ambuye, nditengeni ine limodzi nawo. Ine ndikufuna kuti ndipite ndi iwo. Ine ndikupita ku Gologota tsopano, Ambuye, awa chikhulupiriro. Ine ndikupita ndi osonkhana awa. Tsopano ingondiwumbani ine kenanso, Ambuye. Ine ndachita cholakwa. Nthawi zambiri zimene ine....Kuno posachedwapa ine ndinkati ndingosiya kulalikira. Anthu sanali kundimva ine. Iwo anali kumangopitirizabe kuchita chinthu chomwecho, ndipo ine_ine ndinakhumudwitsidwa. Ine ndinayamba kuipidwa. O Mulungu! Malamlungu awiri apitawo, pamene Inu munandipatsa ine chizindikiro chija kunja uko, ndipo ndikuwerenga Baibulo, ndi kukuonani Inu mukumuwuza Mose, basi momwe loto lija linali, kuti uko kunali phiri, ukonso, ndipo chikanakakhala chizindikiro kwa iye. Ndiyeno pa mapeto pomwe pa icho, kudziwa kuti ine_ine ndinali nditasiya anthu ochuluka odwala; utumiki osati mwa uneneri okha, koma mwa kuphunzitsa Mawu, ndi_ndi wa kupempherera odwala. Inu munamulola munthu kugwa wakufa apa pomwe

pansipa, ndiye nkumubwezera iye ku moyo, mwa chitsimikiziro kuti izo zinali zoona. Inu nthawi zonse mumatsimikizira Mawu Anu.

152 Tsopano, Ambuye, atsimikizireni Iwo pakali pano pamene ine ndiri patsogolo pa Mpandowachifumu Wanu. Tengani aliyense wa anthu awa, Ambuye, tengani dziko lichoke mwa ife. Nditengeni ine, Ambuye, pamene ife tiri mu Kukhalapo Kwanu. Ingotengani dziko, lizani mitima yathu, Mulungu, pakali pano. Sololani dziko ndi zosamalira za dziko kutali ndi ife. Tiloleni ife tikhale Akhristu odzipereka, O Mulungu, kuti tikhale okonda ndi achifundo ndi okoma, tikubala chipatso cha Mzimu. Kodi simutero inu, Ambuye? Ife tiri pamaso pa Mpando wachifumu Wanu. Tchimo lasiya banga lofiira pa mmodzi aliyense wa ife, koma Magazi Anu akhoza kuchotsa izo, Ambuye, ndi kulipanga ilo loyera ngati chisanu. Perekani izi, pamene ife tikuyembekezera pa Inu. Titengeni ife; ife ndife Anu; tapereka miyoyo yathu kwa Inu. Mu Dzina la Yesu Khristu, perekani izi, Ambuye, kwa mmodzi aliyense wa ife.

Finyani mtima wanga, Ambuye. Ine ndikuwona zolakwitsa zanga zonse. Ine ndikuwona zophonyetsa zanga. Mulungu, kuyambira nthawi ino, ine ndikuyesera kuti ndizikhala mopambana momwe ine ndingakhoze, kuti ndikuthandizeni Inu. Ine ndikufuna kupita, ine ndikufuna kudzipereka moyo wanga mwatsopano kwa Inu, kudutsa pano mmawa uno. Nditatha kubweretsa chitsutso ichi motsutsa anga_azibusa amzanga kunja uko, ndipo ndimachita kunena zinthu zolimba izi, koma, Ambuye, ine ndinachita izo mwa kudzoza Kwanu. Ine ndikumverera kuti Inu munandiuza ine kuti ndichite izo. Tsopano izo zachoka pa mapewa anga, Ambuye. Ine_ndine wokondwa kuti izo zandichoka. Asiyeni iwo achite ndi izo chirichonse chimene iwo afuna, Atate. Ine ndikupemphera kuti iwo avomereze izo.

Ine ndikupemphera kuti Inu mumupulumutse mmodzi aliyense, Ambuye. Mulole pamenepo pabwere chitsitsimutso cha olungama, ndi Mphamvu yaikulu ibwere pakati pa Mpingo Iwo usanapite basi. Siziri zovuta kupempherera izo, chifukwa Inu munalonjeza izo.

Ndipo ife tikuyang'anira, Ambuye, ku chikoka chachitatu chija chimene ife tikudziwa kuti icho chidzatichitira zinthu zazikulu ife pakati pathu.

153 Ndine Wanu, Ambuye. Ine ndikudzigoneka ndekha pa guwa ili, basi modzipatula monga ine ndikudziwira kuti ndidzipange ndekha. Tengani dziko lichoke mwa ine, Ambuye. Tengani zinthu kuchokera kwa ine zomwe ziri zakutha; ndipatseni ine zinthu zosatha, Mawu a Mulungu. Mundirole ine ndikhoze kumakhala moyo Mawu amenewo mwapafupi kwambiri, mpaka Mawu akhale ali mwa ine, ndi ine mu Mawu. Perekani izi Ambuye. Mundirole ine ndisadzachoke konse kwa Iwo. Mundirole ine ndigwiritse Lupanga la Mfumu lija mofumbata kwambiri, ndi kuligwira Ilo mwapafupi kwambiri. Perekani izi, Ambuye.

Tidalitseni ife palimodzi. Ndife antchito Anu, pamene ife tikudzipereka tokha kwa Inu mmawa uno, katsopano, mu mitima yathu. Ndife Anu, mu Dzina la Yesu Khristu, mwa kutumikira.

Yesu analipira zonse.

Mulungu akudalitseni inu! M'bale Neville.

MESSAGE online

www.messagehub.info

Maulaliki wolalikidawa ndi
William Marrion Branham
"...mu masiku a liwu..." Chivumbulutso 10:7